

# 1. CHIPULUMUTSO

*Kulandira Yesu Khristu monga mpulumutsi wamoyo wako ndi chisankho chofunikira kwambiri chimene munthu angapange pa moyo wake. Chisankho ichi chimene chiri chosavuta ndi chofanana ndi chikhulupiriro cha mwana, chiri chofunikira kwambiri kwamuyaya wonse.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*UBALE*

**Mafunso ofunikira amene ayankhidwe mu phunziro iri ndi awa:**

*Kodi zimatanthauza chiyani tikati munthu wabadwa mwatsopano?*

*Kodi chipulumutso changa chimakhudza bwanji ubale wanga ndi Mulungu?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kufotokoza mwachidule za zimene zinachitika m'moyo wanu panthawi imene munalandira Yesu Khristu monga mpulumutsi wamoyo wanu komanso kudziwa zam'mene chisankho chimenechi chinasinthira ubale wanu ndi Mulungu.*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Ubale wathu ndi Mulungu uli ubale wa atate wolungama ndi wamwana wake.*

**MAU A PAMTIMA:**

*“Pakuti muli wopulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwacikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwainu; cirri mphatso ya Mulungu; cosacokera kunchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense ” – Aefeso 2:8-9*

*“Koma onse amene analandira lye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwaiwotu, akukhulupirira dzina lace; amene sanabadwa ndi mwazi, kapena ndi cifuniro cha thupi, kapena ndi cifuniro camunthu, koma ca Mulungu.” – Yohane1:12-13*

# **MUMAKHALA M'BANJA LIMODZI MWA MABANJA** **AWUZIMU AWIRI**

## **A. Banja la Satana**

1. Munthu wina aliyense pa dziko pano amabadwa m'banja la Satana.

***Yohane 8:31-44; 1Yohane 3:10***

2. Munalowa m'banja la Satana pamene munabadwa **KUTHUPI** kudzera mwa bambo a pa dzikolapansi, amene mwachidziwikire anachokera kwa kholo lathu Adamu. Onse obadwa kuchokera mwa Adamu amabadwa ndi chifanizo ndi maonekedwe a munthu wochimwa.

***Genesesi 5:3; Masalimo 51:5***

3. Inu munalandira chikhalidwe cha uchimo kuchokera kwa tate wanu, Adamu.

***Aroma 5:12; Aefeso 2:1-3***

4. Baibulo likukamba mwachimvekere kuti, chifukwa cha uchimo, inu munaweruzidwa ku imfa.

***"Pakuti photo yauchimo ndi imfa..." – Aroma 6:23***

## **NJIRA YOKHAYO YOTHANA NDI VUTO LANU LA TCHIMO NDIKO KUKHULUPIRIRA YESU KHRISTU MONGA MPULUMUTSI.**

***"Yesu ananena naye, Ine ndine njira, ndi coonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine" – Yohane 14:6***

– **Yesu ndi njira.**

Baibulo limanena kuti anthu onse adzafa mumachimo awo ngati sapulumutsidwa kuchilango chimene anayenera kulandira kudzera pa kukhetsedwa kwa mwazi wa Yesu Khristu. Yesu anakhala njira ya chipulumutso pakufa m'malo mwanu pantanda, ndipo anaikidwa m'manda masiku atatu, ndikuukanso pogonjetsa ntchimo ndi imfa.

***1 Akorinto 15:1-4; Akolose 1:12-14***

– **Yesu ndi choonadi.**

Baibulo limanena kuti anthu onse amakana za choonadi choti Mulungu ndindani posankha kulambira iwo eni komanso chilengedwe. Yesu ndi choonadi chimene anthu anayenera kuchifuna komanso kulambira ngati Mulungu m'modzi woona.

***Aroma 1:20-25; 1 Yohane 5:20***

– **Yesu ndi moyo.**

Anthu onse amabadwa mu tchimo, ndipo amatsutsidwa polekanitsidwa ndi Mulungu kudzera mu imfa yosatha mu ng'anjo yamoto. Iwo akufuna moyo wosatha umene umapezeka mwa Yesu Khristu.

***Chibvumbulutso 20:15; 2 Atesalonika 1:7-9***

## B. Banja la Mulungu

1. Mumalowa m’banja la Mulungu kudzera mu kubadwa kwa UZIMU mwa Atate wanu wakumwamba. Pa kukhulupirira Yesu Khristu monga Mpulumutsi wako, umakhala mwana wa Mulungu kudzera mu kubadwa mwamzimu. Izi ndizimene zimatanthauza tikamati “kubadwa mwatsopano”.

***Yohane 3:3-7; 1Petro 1:23***

2. Kubadwa kwatsopano uku kwa fotokozedwa mu ***Yohane 1:12-13***.

*“Koma onse amene anamlandira lye...”*

Ngakhale Yesu anafera onse, mukuyenera kuika chikhulupiriro chanu mwa Khristu monga Mbuye ndi Mpulumutsi, ndikusankha kuti mukhale wophunzira wake.

*“...kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu...”*

Mulungu amakupangitsani inu kukhala mwana wa Mulungu ndikulowanso m’banja lake.

*“...kwaiwotu akukhulupirira dzina lace...”*

Mwayenera kukhulupirira mwachisomo kudzera mu chikhulupiriro chimene Yesu anapereka kamba katchimo lanu pokhetsa mwazi mu imfa yake, ndiponso lye anauka mu chigonjetso.

*“...amene sanabadwa ndi mwazi, kapena ndicifuniro cathupi, kapena ndi cifuniro cha munthu...”*

Inu simumalowa m’banja la Mulungu kudzera kubadwa m’thupi (mwazi), kapena mu mphamvu zanu (cifuniro cathupi), kapena munthu wina akufuna kuti mukhalenazo (cifuniro ca munthu).

*“...koma ca Mulungu.”*

Kulowa kwanu m’banja la Mulungu kumadzera mukubadwa monga mwa uzimu.

3. Mulungu wakumwamba amakhala Atate wanu pamene mwatengedwa kulowa m’banja lake.

***Aroma 8:15***

4. Mutatha kupulumutsidwa, Mulungu sadzakutengani ngati wochimwa, koma ngati mwana wake.

***1 Yohane 2:1; Aefeso 5:1***

## MFUNDO YOFUNIKIRA YA PHUNZIRO!

Ubale wathu ndi Mulungu uli ubale wa atate wolungama ndi wamwana wake. Mosiyana ndi atate a dziko lapansi, Mulungu samalakwitsa pamene akuchita ndi ana ake.

*“Comweco, ngati inu, muli oipa, mudziwa kupatsa ana anu mphatso zabwino, kopambana kotani monga nanga Atate wanu waKumwamba adzapatsa zinthuza bwino kwa iwo akumpempha lye?”*

– **Mateyu 7:11**

## ZOKAMBIRANA:

Kodi inu munalowa liti m’banja la Mulungu?

Njira yokhayo imene inu mungathe kupulumutsidwa nayo ndi kukhala moyo wanu wonse ndi Mulungu ndikudzera kukhulupirira kuti Yesu anafa, anaikidwa mmunda, ndipo anauka chifukwa cha inu. Mumalandira mphatso yodabwitsa imeneyi poitanira ndikupempha Yesu Khristu kuti akupulumutseni.

- Ngati simungathe kunena nthawi kapena malo amene inu munapulumutsidwira, ndiye kuti ndizotheka kuti simungakumbukire, kapena kuti simunabadwe mwatsopano.
- Anthu ene anakhalapo ndi chidziwitso pa nkhani za chipemebedzo, koma sanakhonze kumvetsa zakufunikira kwa uthenga wabwino. Ena akhonza kunena pemphero, koma sanapange izi kuchokera pansu pa mtima.
- Ngati inu simukutsimikizika za chipulumutso chanu, bwanji osakonza mlandu wanu ndikumupempha Mulungu kuti akupulumutseni tsopano?

***Aroma 10:9-13***

Kodi ubale wanu ndi atate anu adziko lapansi ukukhudzana bwanji ndi m’mene inu mumawonera za ubale wanu ndi Mulungu monga atate wanu wakumwamba?

## NDI CHINTHU CHOFUNIKIRA KUMVETSA ZA MMENE MOYO WANU WASINTHIRA MUTALANDIRA CHIPULUMUTSO

### A. Inu tsopano muli ndi Mzimu Woyera mkati mwanu

*“Cosungitsa cokomaco udikire mwa Mzimu Woyera amene akhalitsa mwa ife” – 2 Timoteo 1:14*

*“Kodi simudziwa kuti muli kacisi wa Mulungu, ndi Mzimu wa Mulungu agonera mwainu? – 1 Akorinto 3:16*

## **B. Inu tsopano ndinu wolengedwa watsopano mwa Khristu.**

*“Cifukwa cace ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita zatsala zatsopano.” – 2 Akorinto 5:17*

## **C. Inu muli ndi moyo wosatha.**

Ndi wanu ndithu tsopano; simuyenera kudikira kulandira mu nthawi ina mtsogolo. Ndime ziri m’musizi zikukamba zam’mene moyo wanu uliri munthawi yatsopano ino.

*“Iye amene akhulupirira Mwana yo alinao moyowosatha...” – Yohane 3:36*

*“...Iye wokhulupira ali nao moyo wosatha.” – Yohane 6:47*

*“Iye wakukhala ndi Mwana ali nao moyo...” – 1 Yohane 5:12*

## **D. Inu tsopano muli ndi chikhalidwe chatsopano cha uzimu.**

1. Monga m’mene inu mumalandirira chikhalidwe cha umunthu kuchokera kukubadwa mwathupi, mwalandiranso chikhalidwe cha uMulungu kudzera mu kubadwa kwanu kwatsopano mu uzimu.

**2 Petro 1:3-4**

2. Tsopano chifukwa muli ndi chikhalidwe chatsopano mwa Yesu Khristu, Baibulo limatiuza kuti tikhale m’moyo wosiyana ndi iwo amene ali otaika.

**2 Akorinto6:14-18**

### **MFUNDO YOFUNIKIRA PA PHUNZIRO IRI:**

Inu simumataya chikhalidwe chanu cha umunthu pamene mwabadwa kuuzimu. Mumakhala ndi zikhalidwe ziwiri zimene zimaonekera mwa inu pa nthawi zofanana. “Umunthu wanu wakale” ndiwo wa kuthupi, wauchimo umene umakhazikika mwa Adamu, monga mwachikhalidwe chakugwa. “Umunthu wanu watsopano” ndi umunthu wanu wakuuzimu umene wapangidwa pamodzi ndi Khristu. Nkhani kwa wokhulupirira wina aliyense ndiyokuti, iye asankhe chikhalidwe chimene akufuna kutumikira komanso kufanizidwa nacho. Chikhalidwe chimene inu mutachipatse mpata wochulukana ndi chimene chingathe kukulamulirani.

## **MFUNDO ZINA ZOVUTA KUMVETSA ZOKHUDZA CHIPULUMUTSO**

---

### **A. Kodi anthu onse ali mbali imodzi ya anthu amene ali m’banja la Mulungu?**

Ayi. Tikhonza kukhala ana a Mulungu mwachikhulupiro mwa Yesu wowukitsidwa.

***Agalatiya 3:26***

### **B. Kodi tikuyenera kuchita kanthu kuti tipite kumwamba?**

Ayi. Kuchita ntchito zabwino sikungathe kubweretsa chipulumutso pa moyo wathu. Timachita ntchito zabwino chifukwa tinapulumsidwa.

***Aefeso 2:8-10; Aroma 4:4-5***

### **C. Kodi pali njira zambiri zopitira kumwamba?**

Ayi. Yesu yekha ndiye njira yopitira kukakhala ndi Mulungu.

***Machitidwe4:12***

## **MAFUNSO ENA AMENE INU MUKHONZA KUFUNSA**

### **A. Kodi ndingathe kuchimwa nditatha kupulumutsidwa?**

Inde. Pamene mwapulumutsidwa, chikhalidwe chanu chakale sichimasintha, ndipo chimatha kukukokerani kuuchimo m'moyo wanu wonse.

***Aroma 7:18-25; Yakobo1:14***

### **B. Kodi tchimo limaononga bwanji ubale wanga ndi Atate wanga a kumwamba?**

Tchimo lanu limapangitsa kuti ubale wanu ndi Mulungu uonongeke, koma ubale wanu ndi Iye monga mwana wake sumasintha. Komabe, Mulungu adzakulanga chifukwa iweyo ndiwe mwana wake.

***Ahebri 12:5-11; Miyambo 3:11-12***

### **C. Kodi ndichite chiyani ndikachimwa?**

Choyamba muyenera kulapa machimo anu kwa Mulungu, ndiponso kukhulupirira m'mwazi wa Yesu Khristu kuti ukuyeretse. Ndipo utatha kulapa machimo ako, uyeneranso kulapa tchimo lako potembenuka ndikulisiya ndicholinga choti ukhale womasuka polondora choonadi cha Mulungu. Pofuna kukana mayesero wobwereranso kutchimo, muyeneranso kupemphera ndikumupempha Mulungu kuti akupatse mtima wodana ndi tchimo.

***1Yohane 1:9; 2Akorinto 7:1; Miyambo8:13***

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi moyo wanu wasintha bwanji kuyambira pa nthawi imene munalandira chipulumutso?

Kodi mukuganiza kuti mungathe kuuza munthu zam'mene akhonza kulandira chipulumutso ndikukhala mwana wa Mulungu? Kodi mungayambe bwanji kukamba za chinthu chimenechi?

Kodi muli ndimafunso pa phunziro iri?

## **KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA**

- 1. Gwiritsani ntchito *1Akorinto 15:1-4* kufotokoza kuti uthenga wabwino ndi chani.**

---

---

---

---

- 2. Njira yokhayo imene munthu amalowera m'banja ndikudzera pa kubadwa. Fotokozani mwa mau anu zam'mene anthu amalowera m'banja la Satana komanso la Mulungu.**

---

---

---

---

- 3. Kodi moyo wanu wasintha bwanji kuyambira pamene munamulandira Yesu Khristu monga mpulumutsi wanu?**

---

---

---

---

- 4. Kodi mungafotokoze bwanji za zikhalidwe ziwiri zimene inu muli nazo tsopano?**

---

---

---

---

---

5. Lembani zam'mene ubale wanu ndi Atate wanu a kumwamba uliri pofanizira ndi ubale wa atate apa dziko pano.

---

---

---

6. Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?

## KUPHUNZIRA ZA BAIBULO PAWEKHA

Werengani Aefeso 2:8-9 ndipo mufotokozere chifukwa chimene wina aliyense sangathe kupulumuka chifukwa cha mphamvu zake?

---

---

Molingana ndi Aroma 10:9-10, kodi munthu amalandira bwanji chipulumutso?

Ubale wanu ndi Mulungu umaonetsedwa ndi ubale wa padziko lapansi wa abambo ndimwana wake. Werengani ndime zotsatirazi ndipo mulembe zina mwa njira zimene Mulungu amasamalira ana ake.

*Masalimo 46:1*

*Yohane 14:26*

*Akolose 3:21*

---

---

*Mateyu 4:4*

*Aroma 8:28-30*

*Ahebri 12:5-11*

---

---

*Mateyu 18:5-6*

*Afilipi 4:19*

*1 Petro 5:7*

---

---







## **2. CHITETEZO CHA MOYO WAMUYAYA**

*Ndi chinthu chofunikira kumvetsetsa komanso kudziwa kuti ubale wanu ndi Mulungu ndi wamuyaya. Pamene munavomereza Yesu Khristu monga Mpulumutsi wanu, Mulungu anakupatsani moyo wosatha ndi chitsimikizo cha chitetezo cha ubale wamuyaya ndi Iye. Kupulumutsidwa kumatanthauza kuti munthu walandira moyo wosatha, komanso kukhala ndi moyo wosatha zimatanthauza kuti wapulumutsidwa.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*CHITETEZO*

**Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndi iri:**

*Kodi moyo wanga watsopano mwa Khristu ndi wamuyaya?*

**Cholinga chenicheni cha phunziri iri:**

*Kudziwa kuti chitetezo chanu pa ubale umene muli nawo ndi Mulungu umakhazikika pa ntchito imene Yesu Khristu anaimaliza osati penanso ayi..*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Kubadwa kwathu sikungasinthike*

### **NDIME YOLOWEZA:**

*“Cinthu conse cimene anandipatsa Ine Atate cidzadza kwa Ine; ndipo wakudza kwa Ine sindidzamtaya kunja” – Yohane 6:37*

*“Izi ndakulemberani, kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu.” – 1 Yohane 5:13*

## **MALEMBA AMAONETSA ZA MPHATSO YA MOYO WOSATHA**

---

- C. Munalandira moyo wosatha mwa Yesu Khristu panthawi imene munalandira chipulumutso.**

*Yohane 3:15; 1 Yohane 5:12*

- D. Yesu Khristu analipira dipo la tchimo lathu kudzera mu nsembe yake. Inu munalandira mphatso ya moyo wamuyaya kudzera mu kuuka kwake.**

*Aroma 6:9-11*

- E. Mulungu sanganame, lye walonjeza inu za moyo wosatha.**

*Tito 1:2*

## **MALEMBA AKUTSIMIKIZA ZA CHITETezo CHA MOYO WAMUYAYA**

---

- A. Baibulo likunena kuti inu muli ndi moyo wosatha chifukwa Mulungu sangakutayeni pa chifukwa chirichonse.**

1. Yesu analonjeza kuti sadzakutayani kunja.

*Yohane 6:37*

2. Yesu analonjeza kuti muli otetedwa manja mwake, ndipo palibe munthu angalande chipulumutso chanu kwa inu.

*Yohane 10:27-29*

3. Munayenera kusankha kukhulupirira kuti moyo wanu uli otetezeka monga wake wa Mulungu.

*2 Timoteo 1:12*

- B. Baibulo likuti inu simungataye chipulumutso cha inu eni**

1. Moyo wosatha ndi mphatso yaulere ya Mulungu yomwe timalandira pa nthawi imene munthu akulandira chipulumutso mwa chisomo cha Mulungu osati mwa ntchito. Inu simungataye moyo wosatha chifukwa simunagwirire ntchito kuti mupeze moyo wosanthawo.

**Aefeso 2:8-9; Aroma 6:23**

2. Ngati pali chinthu china chomwe inu mungachite kuti mupeze kapena kusunga moyo wosatha, ndiye kuti inu mukhonza kudzilungamitsa kudzera mu mphamvu zanu, ndipo Yesu Khristu anafa kwachabe.

**Agalatiya 2:16, 21**

3. Ngati muli ndi udindo wopanga kuti inu mukhale ndi moyo wosatha, ndiye kuti palibe chikaiko kuti mukhonza kuutaya chifukwa cha tchimo lanu. Mulungu yekha ndi amene amateteza chipulumutso chanu.

**Agalatiya 3:10; Yakobo 2:10**

**BAIBULO LIKUTI PALIBE CHIMENE CHINGATILEKANITSE IFE NDI CHIKONDI CHA MULUNGU.**

Werengani **Aroma 8:38-39**. Lonjezo lalikuru ndi chitetezo chochokera mu chikondi cha Mulungu zikuonetseredwa kwa okhulupirira wina aliyense mu ndime zimenezi. Palibe chinachirichonse chimene chingatilekanitse ndi chikondi cha Khristu, ngakhale chitetezo cha moyo wosatha chimene tiri nacho mwa lye.

- **Imfa** – simungakhonze kutaya pamene mwafa • **Zinthu zomwe ziripo** – *palibe chimene chingalande pakadali pano*
- **Moyo** – simungakhonze kutaya pamene muli ndi moyo • **Zinthu zirinkudza** – *palibe chimene chingalande mtsogolo*
- **Angelo** – Angelo sangatenge kwa inu • **Utali** – *palibe chinthu kumwamba chimene chingalande ichi*
- **Maukuru** – *government cannot take it from you* • **Kuya** – *palibe chinthu pansu pa inu chingalande ichi*
- **Zimphamvu** – Mphamvu za satana sizingatenge ichi • **Colengedwa ciriconse** – *palibe chamoyo chirichonse chingalande*

**ZOKAMBIRANA:**

Ndi chinthu chofunikira kudziwa zokhudza kale sizinatchulidwe apa. Tchimo lanu linakulekanitsani inu ndi Mulungu, koma tsopano ndinu mwana wa Mulungu. Inu simuli wolekanitsdwanso ndi Mulungu chifukwa cha zinthu zam’mbuyo. Kodi inu mukulora kuti zinthu za m’mbuyo ziononge ubale wanu ndi Mulungu? “*Ndipo inu anakupatsani moyo, pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zocimwa zanu, zimene munayendamo kale, monga mwa mayendedwe a dziko lapansi lino, monga mwa mkulu wa ulamuliro wa mlengalenga, wa mzimu wakucita tsopano mwa ana a kusamvera; amene ife tonsenso tinagonera pakati pao kale, m’zilakolako za thupi lathu, ndi kucita zifuniro za thupi, ndi za maganizo, ndipo tinali ana a mkwiyo cibadwire, monganso otsalawo;* **Aefeso 2:1-3**

**MALEMBA AKUTSIMIKIZA ZA CHITETEZO CHANU**  
**CHA MOYO WAMUYAYA**

## A. Ubale wanu ndi Mulungu uli wotetedwa chifukwa ndinu mwana wake monga mwa chibadwidwe.

*Yohane 1:12-13; 1 Yohane 3:1-2*

### MFUNDO YOFUNIKIRA PA PHUNZIRO IRI!

Kubadwa sikungabwerezedwenso. Inu mudzakhala mwana wa bambo a kuthupi chifukwa munabadwa mu mbeu yawo. Ngakhale m' modzi kapena onse a makolo anu sanakhalepo mbali imodzi ya moyo wanu mokwanira, sizimasintha pa choonadi choti inuyo ndi mwana wao. Mukhonza kulekana, kusintha dzina lanu, kapenanso osonanso mu moyo wanu wonse, koma bambo anu adzakhala bambo anu basi. Zirinso chimodzimidzi ndi Atate wanu wa kumwamba. Simungathe kukhala "osabadwa" chifukwa kubadwa kwanu kwa uzimu ndikokhazikika.

## B. Kubadwa kwanu kwatsopano mwa Khristu kwasindikizidwa ndi Mzimu Woyera wa Mulungu.

1. Pamene munabadwanso kwatsopano, Mulungu anadziwa chimenechi ndipo analemba dzina lanu m' buku la moyo la mwana wa Nkhosa.

*"Inde ndikupemphaninso, mnzanga wa m'goli woona, muthandize akazi awa amene anakangalika nane pamodzi mu Uthenga Wabwino, pamodzi ndi Klementsonso, ndi otsala aja antchito anzanga, amene maina ao ali m' buku la moyo." – Afilipi 4:3*

2. Inu munasindikizidwa ndi Mzimu Woyera wa Mulungu panthawi yakubadwanso mwa uzimu.

*"Mwa lyeyo inunso, mutamva mau a coonadi, Uthenga Wabwino wa cipulumutso canu, ndi kumkhulupirira lye, munasindikizidwa cizindikilo ndi Mzimu Woyerawa lonjezano, ndiye cikole ca colowa cathu, kuti ace ace akaombedwe, ndi kuti ulemelero wace uyamikike. – Aefeso 1:13-14*

## C. Malemba akutsimikizira chikhulupiriro chathu ngakhale ife sitikumva motero.

Chipulumutso chanu sichimatengera zimene mukumva, koma pa choonadi cha mau a Mulungu. Zokaikira ndi mantha zikhonza kukhala zenizeni, koma zonsezi zimayenera kuunikiridwa bwino ndi mau a Mulungu.

1. Inu mukhonza kudziwa kuti muli ndi moyo wosatha.

*"Izi ndakulemberani, kuti mudziwe kuti muli moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu" – 1 Yohane 5:13*

2. Mulungu analonjeza za moyo wosatha, ndipo moyo wosatha ulibe chimaliziro.

*"Ndipo ili ndi lonjezano lye anatilonjezera ife, ndiwo moyo wosatha." – 1 Yohane 2:25*

3. Mulungu amadziwa kuti ndinu opulumutsidwa, koma inunso muyenera kutsimikizika pa za chipulumutso chanu.

*“M’mene monse mtima wanu utitsutsa; cifukwa Mulungu ali wamkuru woposa mitima yathu nazindikira zonse.” – 1 Yohane 3:20*

4. Chikondi cha Mulungu chidzagonjetsa mantha onse amene inu muli nawo.

*“Mulibe mantha m’cikondi; koma cikondi cangwiro citaya kunjira mantha, popeza mantha ali naco cilango ndipo wamanthayo sakhala wangwiro m’cikondi.” – 1 Yohane 4:18*

#### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi munakhalapo ndi nthawi yokaikira za chipulumutso chanu pa moyo wanu?

Kodi kudziwa kuti muli ndi chitetezo cha moyo wosatha kwasintha chiyani za m’mene mumaonera za ubale wanu ndi Mulungu?

## **MFUNDO ZINA ZIMENE SIZIMVETSETSEKA ZOKHUDZA CHITETEZO CHA MOYO WOSATHA**

---

### **D. Kodi ndiyenera kugwira ntchito kuti nditeteze chipulumutso changa?**

Ayi. Ntchito ziri zotsutsana ndi chisomo. Timapulumutsidwa mwa chisomo chokha, kudzera mu chikhulupiriro chokha, ndi mwa Khristu yekha. Chikhulupiriro chimatilungamitsa ife pamaso pa Mulungu, pamene ntchito zanu zimatilungamitsa pamaso pa anthu. Iye tinayenera kuyenda ndi Khristu monga m’mene tinamulandira lye mwa chikhulupiriro.

*Tito 3:5; Agalatiya 2:16; Akolose 2:6-7*

### **E. Kodi ndidzataya chipulumutso changa ndikachimwa?**

Ayi. Pamene tichimwa, timadula chiyanjano chathu ndi Mulungu, koma lye samatichotsa mu banja lake. Iye timayenera kulapa machimo athu kwa Atate, kulapa, ndipo ubale umakonzedwanso.

*1 Yohane 1:9; 2 Akorinto 7:1*

### **C. Kodi okhulupirira akhonza kutaya chipulumutso chawo ngati atasankha kumukana Yesu?**

Ayi. Mphatso ya chipulumutso siyotengera nyengo, koma ndi ya muyaya. Mulungu sangawakane ana ake. Komabe, pali zotsatira zimene zimadza kamba kosankha kukhala moyo osati wa mu chiyanjano ndi Mulungu. Mulungu adzalanga ana ake ndi cholinga choti awatsogolere ku chiyero.

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu muli ofuna kukhulupirira ndi kuvomereza chimene baibulo likukamba zokhudza chitetezo cha moyo wanu wosatha?

Kodi ndi zotsatira ziti zimene inu mwakumana nazo chifukwa munasankha kukhala moyo osati wa mu chiyanjano ndi Mulungu?

Kodi muli ndi funso zokhuza phunziro iri?

## **KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA**

- 7. Kodi ndi malonjezo ati amene ife tikhonza kukamba kuti ndi athu pa Yohane 6:37 ndi Yohane 10:27-29?**

---

---

---

- 8. Fotokozani mwa mau anu kuti kutsindikizidwa ndi Mzimu Woyera zimatanthauza chiyani. Gwiritsani ntchito malemba kutsimikiza zomwe mutalembe.**

---

---

---

---

- 9. Kodi pali china chirichonse chimene chingakulekanitseni ndi chikondi cha Mulungu? Gwiritsani ntchito malemba kutsimikiza zomwe mutalembe.**

---

---

---

- 10. Lembani ndime zina za m'baibulo zimene zikuonetsa kuti inu mungathe kudziwa kuti muli ndi moyo wosatha tsopano lino?**

---

---

---



**11.Kodi ndi zotheka kuti inu mukhonza kupanga china chake chimene chingapangitse inu kutaya chipulumutso chanu?**

---

---

---

---

**12.Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?**

---

---

---

---

---

---

## **KUPHUNZIRA ZA BAIBULO PAWEKHA**

**2 Timoteo 2:15-19** ikulankhura za gulu la anthu amene anachoka pamaso pa Ambuye. Kodi ndi chifukwa chiyani iwo anataya chikhulupiriro chawo? Kodi baibulo limati chiayani za mmene Mulungu amaonera za ubale wao ndi lye?

---

---

---

Molingana ndi **1 Petro 1:3-5**, muli ndi chiyembekezo chamoyo chifukwa mwabadwa mwatsopano kuchokera ku kwa akufa. Kodi ndime imeneyi imaphunzitsa chiyani za cholowa chanu cha kumwamba? Kodi ndi mphamvu ya ndani imene imateteza chipulumutso chanu?

---

---

---

---

Fananizani **Afilipi 1:6; Yuda 1:24-25; ndi 2 Timoteo 1:12** ndi kufotokoza zifukwa zimene inu mungakhalire ndi ndi chitsimikizo pa za chipulumutso chanu.

---

---

---

**Baibulo limaphunzitsa kuti simungataye chipulumutso chanu. Komabe, mukhonza kuvutika ngati simutumikira Ambuye. Chonde werengani ndi kuyankha mafunso pa ndime zimenezi.**

***Masalimo 51:12***

Kodi inu munayamba mwayatapo chimwemwe cha chipulumutso chanu? Kodi mukusoweka kufunsa Mulungu kuti abwezeretse chimwemwe cha chipulumutso chanu ku moyo wanu tsopano?

---

---

***2 Akorinto 6:1-3***

Ndi zotheka kutaya umboni wanu monga otsata Khristu. Kodi panakhalapo nthawi ina mutapulumsidwa imene inu simunalemekeze Mulungu molingana ndi mmene mumakhalalira? Kodi umboni wanu ndiwotani lero?

---

---

***1 Akorinto 3:11-15***

Pali mphoto ya muyaya imene idzaperekedwe komanso kusaperekedwa motengera ndi zimene inu mukhonza kuikiza pa zinthu zamuyaya kapena zosakhalitsa. Kodi pakadali pano, mukukhala komanso kuikiza mu zinthu zimene zingakhale kwa muyaya?

---

---

## 3. MZIMU WOYERA

*Mzimu Woyera wa Mulungu anatenga malo okhazikika mumtima mwanu pamene munamulandira Yesu Khristu monga mpulumutsi wanu. Mzimu Woyera ndi chionetsero kuti Mulungu ali m'moyo mwanu, ndipo amakhumba kukupangani inu kukhala oyera pamene muyenda naye. Anthu ambiri samamvetsa bwino komanso amatha kukana za Mzimu Woyera monga m'modzi mwa UTATU wa Mulungu.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*KUDZALA*

**Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Kodi ntchito ndi kufunikira kwa Mzimu Woyera ndi kotani m'moyo wanga?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kukupatsani inu zinthu zofunikira ZOONA zoti mudziwe zokhudza ntchito ya Mzimu Woyera wa Mulungu pa moyo wanu.*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Mzimu Woyera amakhala mwa inu.*

**MAU A PAMTIMA:**

*“Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri kacisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo simukhala a inu nokha. Pakuti munagulidwa ndi ndi mtengo wace wapatali; cifukwa cace lemekezani Mulungu m'nthupi mwanu – 1 Akorinto 6:19-20*

*“Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, cikhulupiriro, cifatso, ciletso, pokana zimenezi palibe lamulo” –Agalatiya 5:22-23*

# **KODI MZIMU WA MULUNGU UMACHITA CHIYANI M'MOYO MWANGA?**

## **MFUNDO YOFUNIKIRA MU PHUNZIRO IRI!**

Mzimu Woyera amakhala mwa inu. Baibulo lonse, timawerenga za abambo ndi amayi amene anakumanapo ndi kupezeka kwa Mulungu mu nthawi komanso nyengo zosiyana. Pemene inu munavomera Yesu Khristu monga mpulumutsi wanu, Mulungu anapereka Mzimu wake kuti akhale mwa inu. Inu tsopano muli ndi kupezeka kwa Mulungu mkati mwanu, ndipo thupi lanu lasanduka kukhala kachisi wa Mzimu Woyera!

*Yohane 14:16-17; Agalatiya 3:2; 1 Akorinto 3:16*

**C. Mzimu Woyera ndiye wosindikiza komanso kutsimikizira za chipulumutso chanu.**

*Aefeso 1:13-14*

**D. Mzimu Woyera amatipatsa mphamvu zotumikira Mulungu.**

*Aefeso 3:16*

**E. Mzimu Woyera amachitira umboni kwa inu za chipulumutso chanu.**

*Aroma 8:16*

**F. Mzimu Woyera amakupembedzerani m'mapemphero.**

*Aroma 8:26-27*

**G. Mzimu Woyera adzakuphunzitsani baibulo**

*Yohane 16:13-15; 1 Akorinto 2:9-14*

**H. Mzimu Woyera amapereka chitsogozo popanga chiganizo**

*1 Akorinto 2:15-16*

**I. Mzimu Woyera amakulimbikitsani mu nthawi ya kusowa.**

*Yohane 14:15-18*

**J. Mzimu Woyera adzapereka chimene lye anatiphunzitsa kuti tidzikumbukira.**

*Yohane 14:26*

**K. Mzimu Woyera adzatsutsa za machimo**

*Yohane 16:8-11*

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi kukhala kachisi wa Mulungu zasintha chiyani za m'mene mumakhalira mmoyo mwanu?

Kodi mungathe kupereka chitsanzo cha mmene Mzimu Woyera anakuthandizirani kumvetsa za ndime mu baibulo?

## **KODI TCHIMO LIMAKHUDZA BWANJI MZIMU WOYERA?**

**A. Tchimo lanu limakwiitsa Mzimu Woyera**

Mulungu anaika Mzimu wake mwa okhulupirira wina aliyense chifukwa ndi cholinga chake kuti moyo wathu uonetsere ku dziko lapansi chikhalidwe chake. Mzimu Woyera amakwiitsidwa (kudandaula) pamene okhulupirira asankha kukhala moyo wawo ndi zikhumbitso za dziko lapansi.

*Aefeso 4:30*

**B. Tchimo lanu limazima mphamvu ya Mzimu Woyera**

Pamene okhulupirira apitilira komanso mwadala akana kutsutsidwa ndi Mzimu Woyera chikumbumtima chao chimakhala chouma komanso mtima wao umalimba. Mzimu Woyera amatha kukhala kuzimitsidwa komanso chifukwa mitima yawo yolimba imakana zimene Mzimu Woyera amawauza kuti akawatsogolere ku chiyero.

*1 Atesalonika 5:19; 1 Timoteo 4:1-2*

## MFUNDO YOFUNIKIRA KUDZIWA:

“Baibulo likugwiritsa ntchito mau oti *“cisoni ca kwa Mulungu”* pofotokoza za kutsutsidwa, komanso *“cisoni ca dziko lapansi”* pofotokoza za mkwiyo. Zinthu izi kwa okhulupirira ndi zovuta kuzifotokozero kusiyana kwa kutsutsidwa ndi nkwiyo chifukwa zimaoneka ngati zofanana; komabe ziri ndi zotsatira zosiyana.

Kutsutsidwa kumachokera kwa Mulungu amene akuonetsa za tchimo lenileni m’moyo wa munthu kuti alape. Kutsutsidwa kumabweretsa chisoni cha kwa Mulungu, ndi kukhudzika kuti tanyoza Mulungu. Izi zimatifikitsa **KWA** Mulungu kudzera mu kulapa, zimene zimabweretsa chipatso cha chikhululuko, mtendere, komanso ubale wabwino ndi Mulungu.

Nkwiyo umachokera kwa satana, amene amatipangitsa ife kukhala anthu osayenera pa chikondi cha Mulungu ndi madalitso. Izi zimabweretsa, nkwiyo, mantha, kukhumbitsa komanso kubwezera chilango zimene zimatilepheretsa kukhala pa ubale ndi Mulungu.

**2 Akorinto 7:9-11**

## ZOKAMBIRANA:

Kodi pali china chirichonse chimene m’moyo mwanu chimene chikupangitsa kuti Mzimu Woyera akwiye?

## KODI CHIPATSO CHA MZIMU NDI CHIYANI?

Mzimu Woyera amabweretsa zikhalidwe zambiri za uMulungu mwa inu zotchedwa chipatso cha Mzimu. Chikhalidwe chirichonse chikubwera pa nthawi imene mwapereka moyo wanu kwa Mulungu komanso kuyenda mu mphamvu yake. Ndi zofunikira kumvetsa kuti pali chipatso chimodzi chimene chimaonetsedwa mu zikhalidwe zisanu ndi zinai zosiyanasiyana. Njira yokhayo yoti munthu akhale ndi moyo wonga wa Yesu ndi kuonetsa za chipatso cha Mzimu m’moyo wanu.

*“Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, cikhulupiriro, cifatso, ciletso, pokana zimenezi palibe lamulo” –Agalatiya 5:22-23*

### A. Pali zikhalidwe zamkati mwa munthu zimene zimasintha moyo wanu.

#### 1. Chikondi

*Mzimu Woyera amapereka chikondi chenicheni cha pa Mulungu ndi anthu.*

#### 2. Chimwemwe

*Mzimu Woyera amapereka chimwemwe chokhazikika mkati posatengera ndi zimene zimachitika kunjira kwa moyo wa munthu.*

**3. Mtendere**

*Mzimu Woyera amapereka mtendere wa mumtima ngakhale pali mikangano.*

**B. Pali zikhalidwe za kunja kwa munthu zimene zimasintha ubale wanu ndi anthu ena.**

**1. Kuleza mtima**

*Mzimu Woyera amaloleza inu kuti mupereke chisomo kwa anthu posatengera zofooka zawo*

**2. Chifundo**

*Mzimu Woyera amapereka kuthekera koti tiwasamale anthu ena mwaulemu, modekha komanso mwachikondi*

**3. Kukoma mtima**

*Mzimu amapereka kwa inu chikhalidwe cha uMulungu chimene chimaonetsa kukoma mtima kwake.*

**C. Pali zikhalidwe zina zokhudzana ndi Mulungu zimene zimalimbikitsa ubale wathu ndi Mulungu.**

**1. Chikhulupiriro**

*Mzimu Woyera amapereka chitsimikizo choti tikhulupirire mau a Mulungu*

**2. Chifatso**

*Mzimu Woyera amapereka mphamvu za mkati zimene zimaonetsa kudzichepetsa.*

**3. Chiletso**

*Mzimu Woyera amatitsogolera kukhala moyo wokhazikika*

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi ndi zikhalidwe ziti zauzimu zimenezi (chipatso) zimene inu mukufuna kuona zikukura mwa inu?

## **KODI NTCHITO ZA THUPI ZIMENEZI NDI ZOTANI?**

Chipatso cha Mzimu zichingabwere mwa okhulupirira amene amatsogozedwa ndi thupi osati Mzimu. Ndikosavuta kudziwa anthu okhulupirira amene asankha kukhala mmoyo wa uchimo chifukwa ntchito za thupi zikhala zoonekera mmoyo wawo.

*“Ndipo ntchito za thupi zionekera, ndizo dama, codetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madando, ndeu, kaduka, zopsa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mcezo, ndi zina zotere; zimene ndikucenjezani nazo, monga ndacita, kuti iwo akucitacita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu.” – Agalatiya 5:19-21*

– Dama

*Kukhala osakhulupirika kwa okonedwa wako*

– Mkiyo waukuru

*ntchito yamphamvu ya nsanje, kuonetsera mkiyo*

**– Machitidwe onyasa**

*Tchimo lina lililonse lachigololo la kunja kwa banja*

**– kutetana**

*Kuutsa makangano, kuyambitsa magawano*

**– Chidetso**

*Zolakwika, china chiri chonse chodetsa thupi*

**– Mipatuko**

*Kuwachotsa ena pa choonadi*

**– Chilakolako**

*Chilakolako, zikhumbitsa za chiwerewere*

**– Ziphunzitsa zonyenga**

*Ziphunzitsa zabodza*

**– Kupembedza mafano**

*Kupembedza zinthu zina osati Mulungu*

**– Kukhumba zonyansa**

*Kusilira koipa kwa anthu amene akuchita bwino*

**– Nyanga**

*Kugwiritsa ntchito mphamvu za Satana, za matsenga kapena kuukira*

**– Okupha**

*Kupha munthu wina, angakhale kudzera mmawu*

**– Kaduka**

*Mkwiyo wamkati*

**– Kuledzera**

*Kulola chinthu china kulamulira moyo wako*

**– Magawano**

*Kukangana kosayenera/mkangano*

**– Kukomedwa ndi choipa**

*Kugawana koopsa, kukhumbitsa za thupi*

**– Kutengera**

*Nsanje kwa anthu ena, kukonda za dziko*

**– Ndi zina zotere**

*China chirichonse chimene chikhonza kukuchotsano pamaso pa Mulungu*

**MFUNDO YOFUNIKIRA KUDZIWA:**

China chiri chonse pa ndandanda uwu ndi chothekera kubweretsa kulimbana mu thupi lanu padakali pano. Pamene thupi likulamulira inu, ntchito ina iriyonse yathupi idzaonetsedwa. Ntchito za thupi zionekera mmoyo wanu chifukwa tikadali kuthupi. Ndi chifukwa chake ntchito zathupi posakhalitsa zidzaonekera pemene mulora kuti thupi likulamulireni.

## **KODI NDINGADZALE BWANJI NDI MZIMU WOYERA?**

**A. Inu muli odzala ndi Mzimu wa Mulungu chimodzimodzi ndi mmene muli odzazidwa ndi mau a Mulungu.**

Pamene mufananiza ndime imene iri mmusimu, muona kuti kulora kuti mau a Mulungu akhale mwa inu ndi kudzala ndi Mzimu ziri ndi zotsatira zofanana mmoyo mwanu. Inu mukhala odzazidwa ndi Mzimu pamenenso malingaliro ndi mitima yanu idzadzidwa ndi mau a Mulungu.



*“Ndipo musaledzere naye vinyo, m’mene muli chitayiko; komatu mudzale naye Mzimu, ndi kudzilankhulira nokha ndi masalaimo, ndi mayamiko, ndi nyimbo, zauzimu, kuyimbira ndi kuyimba m’malimba Ambuye mumtima mwanu; – Aefeso 5:18-19*

*“Mau a Khristu akhalitse mwa inu, cicurikire mu nzeru yonse, ndi kuphunzitsa ndi kuyambirirana eni okha ndi masalmo, ndi mayamiko ndi nyimbo zauzimu, ndi kuyimbira Mulungu ndi cisomo mumtima mwanu. Akolose 3:16*

## **B. Inu muli odzala ndi Mzimu Woyera wa Mulungu pamene mulora kuti Iye alamulire inu**

Kudzala ndi Mzimu wa Mulungu ndi ndondomeko ya moyo wonse pamene tikukura muuzimu, choncho munthu amayenera kudekha ndi kukhazikika. Pamene mukukura ndi kukhwima mu uzimu pa kumvera mau a Mulungu, Mzimu Woyera adzalamulira malingaliro anu, zochita zanu ndi zokhumba zanu.

*“Ngati tiri ndi moyo ndi Mzimu, ndi Mzimunso tiyende” – Agalatiya 5:25*

### **MFUNDO YOFUNIKIRA KUDZIWA:**

Inu muli ndi zikhalidwe ziwiri zimene ziri mwa inu. Chikhalidwe chanu chakale ndi chathupi, cha uchimo, chopangidwa mu chifanizo cha Adamu. Chikhalidwe chimenechi m’malemba chimanenedwa kuti “thupi” kapena “umunthu wakale”. Chikhalidwe chatsopano ndi chazimu, changwiro, chokonzedwanso monga mwa chifanizo cha Mulungu. Chikhalidwe chimenechi m’malemba chimanenedwa kuti “munthu watsopano.”

***Aefeso 4:22-24***

Zikhalidwe zonse zimapezeka mwa inu nthawi zonse. Inu muli ndi mwayi opanga chisankho kutsata thupi kapena Mzimu. Inu mwayenera kusakha chikhalidwe choti muchitsate. Kusankha kutsata thupi ziri ndi zotsatira zake, komanso kusankha Mzimu kumabweretsa madalitso.

***Agalatiya 5:16-17; 6:7-9***

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu mukukhala moyo wodzala ndi Mzimu Woyera?

Kodi nthawi yanu m’mau a Mulungu ikuthandiza bwanji pa m’mene inu mukudzalidwira ndi Mzimu wa Mulungu?

## **MAFUNSO ENA AMENE INU MUKHONZA KUFUNSA**

### **F. Kodi ndipemphere ndi kupempha Mulungu kuti andipatse Mzimu Woyera wochulukana?**

Ayi. Inu munasindikizidwa ndi Mzimu Woyera panthawi imene munalandira chipulumutso chanu. Inu simuyenera kufunsa Mzimu wa Mulungu winanso, koma mukufunikira kudzala ndi Mzimu Woyera amene muli naye mkati mwanu.

Kudzala ndi Mzimu zikutanthauza kuti Mulungu ndi amene akutsogolera moyo wanu mwa Mzimu Woyera. Kudzala ndi Mzimu SIKUTI ndi kutenga Mzimu wambiri, koma kuti Mzimu alamulire moyo wanu. Kudzala ndi Mzimu SIKUMAPANGITSA inu kukhala odziwa kapena kukhudzika ndi zauzimu koma zimakutsogolerani kulalikira mau a Mulungu.

***Aefeso 1:13-14; Aroma 8:1-2***

### **G. Kodi Mzimu Woyera adzandisiya pamene ndachimwa?**

Ayi. Inu munasindikizidwa ndi Mzimu Woyera kufikira pamene mudzalowa mu ulemelero wa Mulungu. Mzimu Woyera ndi lonjezo la Mulungu ndi chitsimikizo kuti inu munapuluma ndipo mudzakhala mwana WAKE kwa muyaya.

***Aefeso 4:30***

### **H. Kodi Mzimu Woyera ndi mphamvu chabe ya uzimu kapena ndi mbali imodzi ya utatu wa Mulungu?**

Baibulo limatiphunzitsa kuti Mzimu Woyera ndi munthu wachitatu mu UTATU wa Mulungu. Ndi amodzi ndi Atate ndi Mwana. Anthu ayenera kumvera Mzimu Woyera pamene atitsogolera ndi malangizo kwa okhulupirira.

***Machitidwe 5:3-4; 10:19-21; 13:1-4; 16:6-10***

## **KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA**

**13. Kodi Mzimu Woyera amakhala kuti? Tchulani ndime zitanu kutsimikiza zomwe mutalembe.**

---

---

---

**14. Kodi ndi nthawi iti imene Mzimu Woyera amalowa m'moyo wa wokhulupirira?**

---

---

**15. Tchulani zitsanzo zinai za zimene Mzimu Woyera amachita m'moyo mwanu.**

---

---

---

---

16. Kodi pali kusiyana kotani pakati pa nkwiyo ndi kutsutsidwa?

---

---

---

17. Kodi zimatanthauza chiyani kudzala ndi Mzimu Woyera?

---

---

---

---

18. Fotokozani mwa mau anu kusiyana kwa zikhalidwe ziwirizomwe muli nazo?

---

---

---

---

19. Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?

---

---

---

---

---

## KUPHUNZIRA ZA BAIBULO PAWEKHA

Werengani ndime zitsatirazi ndipo mulembe maina osiyanasiyana amene apatsidwa kwa Mzimu Woyera.

*Yohane 14:16*

*Machitidwe 5:32*

*Agalatiya 4:6*

---

---

---

*Yohane 14:17*

*Aroma 8:2*

*Aroma 8:9*

---

---

---

Werengani ndime zotsatirazi ndipo mulembe zimene zimachitika pamene munthu wadalidwa ndi Mzimu Woyera

**Luka 1:41-42**

**Luka 1:67-68**

**Machitidwe 2:4**

**Machitidwe 4:8**

**Machitidwe 4:31**

**Machitidwe 13:9-10**

Molingana ndi ndime zimenezi , kodi chotsatira chimene chiri chachidziwikire pamene munthu wadzala ndi Mzimu Woyera ndi chiyani?

---

---

**Kodi mungaphunzire chiyani za ubale wanu wa thupi ndi Mzimu kuchokera mu Aroma 8:8-10?**

---

---

---

---

**Kodi Agalatiya 3:1-3 akuphunzitsa chiyani za mmene inu mungathe kukulira mu ubale wanu ndi Mulungu?**

---

---

---

---

## 4. MAU A MULUNGU

*Chimene chimapangitsa chikhristu kukhala cha paderadera ndi kukhazikikika kwake pa mau olembedwa ndi ulamuliro wonse wa Mulungu. Mau a Mulungu ndiwofunikira kwambiri pa kukura kwanu mu chisomo ndi mu chidziwitso cha Yesu Khristu. Baibulo liri ndi muyeso umene ukuonetsa za m'mene moyo wathu ukhonza kukhalira. Mu masamba onse a Baibulo, timaona m'mene Mulungu amayendetsera zochitika za moyo wathu mu njira zonse.*

### **Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*UNGWIRO*

### **Mafunso ofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Kodi ine ndiri ndi mau a Mulungu lero?*

*Kodi baibulo ndi lofunikira bwanji pa moyo wanga?*

### **Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

Kukudziwitsani zina mwa zinthu zokhudza baibulo, kuphunzira za m'mene likugwirizanirana ndi zochitika za pa moyo wathu monga chitsogozo pa kuyenda kwanu kwa tsiku ndi tsiku ndi Yesu Khristu.

### **Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

China chirichonse chochitika m'moyo wanu, kuthupi ngakhale ku uzimu, chiyenera kuweruzidwa ndi muyeso wangwiro umene uli m'mau a Mulungu. Baibulo ndi muyeso wolungama wotsiriza wokhala ndi ulamuliro pa moyo wa okhulupirira.

## **NDIME ZA PAMTIMA:**

*“Pakuti kale lonse cinenero sicinadza ndi cifuniro cha munthu; koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu wa Woyera, analankhulat.” – 2 Petro 1:21*

*“Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo, ca m’cilungamo, kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kucita ntchito iriyonse yabwino.” – 2 Timoteo 3:16-17*

## **KUMVETSETSA ZA KUSALAKWIKWA KWA MAU A MULUNGU**

### **Baibulo linapangidwa mosiyana ndi mabuku ena**

- Baibulo liri ndi mabuku okwana 66. Mabuku 39 mu chipangano chakale, ndipo 27 mu chipangano chatsopano.
- Baibulo linalembedwa ndi anthu osachepera 40 mu zilankhuro zitatatu kwa nthawi pafupifupi zaka 2,000.
- Baibulo ndilosakwika mu nkhani zonse za mbiri, uneneri ndi zina zochitika m’ moyo wa munthu.
- Baibulo silimadzitsutsa lokha
- Baibulo limalumikizana bwino kwambiri, ndipo limakhala ngati kuti linalembedwa ndi munthu m’modzi, chifukwa Mzimu Woyera ndiye m’lembi wa mabuku 66.

### **F. Baibulo NDILOUZIRIDWA monga mau a Mulungu**

Mzimu wa Mulungu anapangitsa anthu a Mulungu kuti alembe mau a Mulungu. Mulungu anavumbulutsa mau ake ndikuwasindikiza.

*2 Timoteo 3:16-17; 2 Petro 1:20-21*

### **G. Baibulo ndi LANGWIRO monga mau a Mulungu.**

Mulungu amasunga yekha choonadi chake mu mau ake. Mau aliwonse a m’baibulo ndi oona, ndipo alibe cholakwika chirichonse.

*Miyambo 22:20-21*

### **H. Baibulo ndi mau ndithu OKWANIRA a Mulungu.**

Ife tikuchenjezedwa kuti tisaonjezere kapena kusintha mau ouzilidwa, olungama, komanso osungidwa bwino monga mau a Mulungu. Mau a Mulungu ndiwokwanira; palibenso vumbulutso lina latsopano kuchokera kwa Mulungu limene liri kunja kwa baibulo.

**Miyambo 30:5-6**

### I. Baibulo ndi a Mulungu OSUNGIDWA bwino.

Mau a Mulungu ndi a muyaya. Iye walonjeza kusunga mau ake oona mu mbiri yonse ndi mibadwo mibadwo. Inu muli ndi chitsimikizo kuti muli ndi mwayi wolumikizidwa ndi Mau a ngwirowo a Mulungu komanso ouziridwa lero.

**Mateyu 5:18**

#### ZOKAMBIRANA:

Kodi mumadziwa kuti buku limene muli nalo la mau a Mulungu ndi loona ndipo lilibe zolakwika?

### MFUNDO YOFUNIKIRA MU PHUNZIRO IRI!

Mulungu wasunga mau ake ndi cholinga chotipatsa ife malangizo kuti tikhale moyo wa chipambano. Baibulo liri ndi ulamuliro weniweni wotsiriza pa moyo wa okhulupirira. Choonadi cha mau a Mulungu ndi chachikuru kuposa zimene ife tinakumana nazo m'moyo wathu.

*“musaweruze monga maonekedwe, koma weruzani ciweruzo colungama.” – Yohane 7:24*

#### Chitsanzo:

Mu **2 Petro 1:16-21**, m'tumwi Petro anavomereza mau a Mulungu kukhala ulamuliro wotsiriza pamene amafananiza ndi zimene iye anakumana nazo pamene anali pa phiri loyera ndi Yesu mu **Mateyu 17:1-9**.

Petro amafananiza za zimene anakumana nazo ndi ulemelero umene anauona mwa Yesu komanso ndi kumva mau a Mulungu kuchokera kumwamba. Petro anamvetsetsa kuti okhulupirira ali “kutsimikizika kwakukuru” pa ulamuliro wa mau a Mulungu kusiyana ndi mau olankhulidwa a Mulungu. Pamapeto pake anadziwa kuti zina ziri zonse zokumana nazo m'moyo, zauzimu kapena kuthupi, kapena m'moyo mwathu ziyenera kuweruzidwa ndi muyeso wa mau a angwirowo a Mulungu.

## KUMVETSETSA M'MENE TINGAGWIRITSIRE NTCHITO MAU A MULUNGU PA MOYO WATHU

### L. Mau Mulungu ali ndi mphamvu kupulumutsa inu.

1. Baibulo limanena kuti mau a Mulungu amapulumsa miyoyo ya anthu. Kopanda mau a Mulungu, anthu akadakhala opanda mwayi kuti apulumuke.

***Yakobo 1:21; 2 Timoteo 3:15***

2. Njira yokhayo imene tingadziwire za uthenga wabwino ndi chifukwa choti kuli mau a Mulungu anavumbulutsa zimenezo. Yesu anafa, anaikidwa m'manda, ndipo anaukansa monga mwa malemba. Inu muyenera kumva ndi kukhulupirira chimene baibulo likunena chokhudza tchimo, khalidwe lanu lotayika, ndi dongosolo la Mulungu la chipulumutso ndi cholinga choti mupulumuke.

***Aroma 10:17; Aefeso 1:13***

3. Dongosolo la Mulungu la chipulumutso limayamba ndi lye amene anatumiza mau ake kuti munthu apulumutsidwe. Choncho, inu muli ndi udindo ogawana ndi ena za mau a Mulungu kuti iwonso apulumuke.

***Mateyu 28:18-20; Aroma 10:13-15***

### **M. Mau a Mulungu ali ndi mphamvu yotsogolera inu.**

1. Nzeru zathu za umuthu sizingathe kumvetsa bwino zinthu zonse za Mulungu. Mulungu anapereka Mzimu wa Mulungu kuti tidziwe ndi kumvetsetsa mau ake. Okhulupirira onse ali odzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo ayenera kuphunzira baibulo.

***Yohane 16:13; 1 Akorinto 2:9-14***

2. Pamene mwayamba kuphunzira ndi kumvetsa mau a Mulungu, mudzamvetsa baibulo, mudzakonzedwa bwino popanga ziganizo za baibulo komanso za uzimu za moyo wauzimu. Mau a Mulungu amapereka chitsogozo chabwino komanso amatipatsa ife malingaliro a Khristu pa nyengo ina iriyonse m'moyo wathu.

***1 Akorinto 2:15-16; Masalmo 119:105***

### **N. Mau a Mulungu amatipatsa mphamvu yoti ife tikule.**

1. Mau a Mulungu amasintha inu pamene akukuyeretsani kuchokera mkati kupita kunja.

***Yohane 15:3; Masalmo 119:9-11***

2. Mau a Mulungu amakuthandizani kuti muthane ndi zotsutsa za uzimu pamene muwagwiritsa ntchito pa mayesero.

***Luka 4:1-13***

3. Mau a Mulungu amatikonzekeretsa kuti titumikire Mulungu komanso kuti tikhale mu choonadi chake.



“Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitsa, citsutsano, cikonzero, cilangizo, ca m’cilungamo, kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kucita ntchito iriyonse yabwino” – **2 Timoteo 3:16-17**

- a. CHIPHUNZITSO- baibulo limaphunzitsa zimene ziri zoonza
- b. CHITSUTSANO – baibulo limaonetsa madera amene ali olakwika
- c. CHIKONZERO– baibulo limatsogolera chidwi chanu ku zinthu zabwino
- d. CHILANGIZO CHA CHILUNGAMO– baibulo limatiphunzitsa kukhala mu chimene chiri cholondora

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi ndi ndime ziti zimene m’baibulo zimene Mulungu anazigwiritsa ntchito kuonetsa za kufunikira kuti tipulumuke?

Kodi mukhonza kugawa chitsanzo chimene chikuonetsa za m’mene kuwerenga ndi kuphunzira mau a Mulungu zakuthandizirani kupanga ziganizo zabwino pa moyo wanu?

Kodi moyo wanu wasintha pamene munalora mau a Mulungu kukhala ulamuliro womaliza?

## **KUSAMVETSETSA KOSIYANASIYANA KOKHUDZA MAU A MULUNGU**

### **I. Kodi ndi zofunika kuti tigwiritse ntchito Baibulo pogawana ndi ena za chikhulupiriro chanu?**

Inde. Wina aliyense ayenera kumva mau a Mulungu ndi cholinga choti apulumuke.

***1 Petro 1:23; Aroma 10:17***

### **J. Kodi munthu angathe kumvetsa baibulo opanda mabuku ena othandizira?**

Inde. Bukhu labwino lothandizira kumvetsa bwino baibulo ndi baibulo lomwelo. Liri ndi ndime zomwe zimafotokozedwa bwino zokha komanso zina zimene tikhonza kufananiza ndi ndime zina mu baibulo momwemo.

***Yesaya 28:9-10***

### **K. Kodi kuwerenga baibulo kungasinthe munthu?**

Inde. Inu muyenera kuwerenga baibulo osati kuti mungouzidwa zinthu, koma kuti tikasinthike ndi choonadi cha mau a Mulungu. Choonadi cha baibulo chimatitsuka ife monsemo, ndiponso chimatipatsa chigonjetso pa tchimo m'moyo mwathu.

*Yohane 17:17; Yohane 8:32*

## **MAFUNSO ENA AMENE INU MUKHONZA KUFUNSA**

---

### **A. Kodi ndiyambire pati kuwerenga?**

Inu muyenera kupereka nthawi yanu ku mau a Mulungu poyang'ana ndime zina zimene zikukamba za ubale wanu ndi atate anu akumwamba.

1. Uthenga wabwino wa Yohane unalembedwa kuti tikhulupirire Yesu Khristu.

*Yohane 20:31*

2. Makalata a Paulo analembedwa poyang'ana za m'mene ife tingatumikire Mulungu kudzera mu mautumiki a pa mpingo wa pamalo.

*Aroma- Filemoni*

3. Buku la miyambo limapereka nzeru komanso chidziwitso pa zinthu m'moyo.  
*Miyambo 1:7*

### **B. Kodi ndingakhale bwanji ndi nthawi yachete?**

Ndi chinthu chofunikira kumvetsetsa kuti inu mukukumana ndi Mulungu, ndipo osati kungowerenga baibulo chabe. Iye adzalankhura kudzera mu mau ake olembedwa, ndipo inu mumalankhura naye kudzera mu pemphero. Mulungu akufuna inu kuti mudziwe ndi kumvetsetsa zimene mau ake amanena kwa inu. Pamene muwerenga baibulo funsani mafunso ena ophweka ngati...kodi ndime iyi ikuti chiyani? Kodi Mulungu akundiphunzitsa chiyani mu ndime imeneyi? Mutatha kuwerenga baibulo, funsani Mulungu kuti akutsogolereni ndi kukupatsani nzeru za m'mene mukhonza kugwiritsa ntchito pa choonadi cha mau ake m'moyo mwanu.

*Miyambo 2:1-6*

Pamene muphunzira baibulo, chikondi chanu cha pa Mulungu ndi mau chimakura. Mukhonza kuonetsa za chikondi chanu pa Mulungu ngati muvomereza kudzera pa kukhulupirira chimene baibulo linena, ndi kukhalanso mu choonadi chake.

*Yohane, 14:15;1 Atesalonika 2:13; Yakobo 1:22-25*

### **C. Kodi nanga nditapeza zinthu zina m'baibulo zimene sindikuzimvetsetsa ?**

Inu mupeza zinthu zambiri zimene simungazimvetse. Simuyenera kukhala ndi nkhawa. Dikirani pa Ambuye kuti akuvumbulutsireni kwa inu mu nthawi yake. Chinthu chofunikira kwambiri NDIKUCHITA chimene inu mukuchimvetse. Mulungu sangakupatseni zinthu zimene inu simungazikwanitse kuti muzimve. Pamene mutenga zinthu kuti muziphunzire, Mulungu adzakupatsani zambiri. Mzimu wa Mulungu yekha adzakutsogolerani ku chilungamo chonse pamene mufananiza malemba ndi malemba.

***Yohane 16:12-15***

#### **D. Kodi ndikhonza kudalira kusalakwika ndi ulamuliro wa mau a Mulungu?**

Pali maganizo awiri osiyana amene okhulupirira amawonera baibulo lero. Iwo amene ali ndi chikhulupiriro cha pamalemba amakhulupirira kuti mau a Mulungu ndi oona, ouziridwa, aphumphu komanso osungidwa bwino. Amakhulupirira kuti Mulungu ali othejera kusunga mau ake bwino kwambiri mu chilankhulo chirichonse. Komabe, iwo amene ali ndi maonedwe achidwi kwambiri ofuna kutsutsa malemba amakhulupirira kuti baibulo liri ndi zolakwika zimene zikufunika kukonzedwa kudzera mu mzeru za munthu komanso kufufuzafuzuza.

Koma mwatsoka, maonedwe amenewa ofuna kutsutsa za baibulo apangitsa kuti akhristu ambiri asokonekere, ndipo zapangitsa kuti anthu ambiri asakhulupirirensa kusalakwika kwa baibulo ndi ulamuliro wake umene uli wa Mulungu m' mau ake. Izi zapangitsanso anthu ena kuti apeze mitundu ina ya baibulo mu zilankhuro ndi zikhalidwe zosiyana.

Ndi chinthu chabwino kukhala ndi chikhulupiriro cha pa malemba, ndikudziwa kuti ukhonza kuwadalira ndi kusalakwika kwake komanso ulamuliro umene uli m' mau a Mulungu monga mwa chilankhuro chanu. Ngati pali mitundu ya ma baibulo yosiyanasiyani, funsani aphunzitsi anu kuti akuthandizeni kuti mudziwe kuti ndi baibulo liti limene liri ndi maziko a chikhulupiriro molingana ndi malemba, kuti inu muligwiritse ntchito ngati buku lanu la mau a Mulungu.

***Mateyu 5:18***

## **KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA**

**20. Tchulani zifukwa zinayi zimene mungadziwire kuti baibulo ndi lodalilika mu njira zambiri.**

- a. \_\_\_\_\_
- b. \_\_\_\_\_
- c. \_\_\_\_\_
- d. \_\_\_\_\_

**21. Pamene mukuyamba kuphunzira ndi kumvetse za baibulo, inu mudzadzikonzeke noka kupanga ziganizo za baibulo komanso za uzimu**

pa moyo wanu. Kodi ndi chiganizo chiti chimene inu mukhonza kudalira pa Mulungu kuti akutsogolereni mu sabata ino?

---

---

22.Molingana ndi *1 Akorinto 2:9-16*, ndi chifukwa chiyani anthu otaika samatha kumvetsa chimene mau a Mulungu akuphunzitsa?

---

---

23.Tchulani njira zinayi zimene mau a Mulungu akhoza kusinthira moyo wanu? Perekani umboni wa malemba pa mfundo iliyonse.

- a. \_\_\_\_\_
- b. \_\_\_\_\_
- c. \_\_\_\_\_
- d. \_\_\_\_\_

24.Molingani ndi *2Timothy 3:16-17*, kodi ndi zinthu zinai ziti zimene malemba akupereka poonetsa kukonzekeretsedwa kwa okhulupirira ku utumiki?

- a. \_\_\_\_\_
- b. \_\_\_\_\_
- c. \_\_\_\_\_
- d. \_\_\_\_\_

25.Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?

---

---

---

---

---

---

## KUPHUNZIRA ZA BAIBULO PAWEKHA

Werengani ndime zotsatirazi ndipo mulembe mitundu isanu ndi umodzi ya zakudya zimene malemba akugwiritsa ntchito kufotokozera mau a Mulungu.

**1 Petro 2:2**

**Luka 4:4**

**Masalmo 119:103; Miyambo 16:24**

**Aefeso 5:26; Yesaya 55:10-11**

**Miyambo 7:2; 25:11**

**1 Akorinto 3:1-2; Ahebri 5:12-14**

**Werangani *Masalmo 19:7-11* ndi *Ahebri 4:12-13*. Sankhani imodzi mwa ndime zimenezi ndipo mulembe zikhalidwe za mau a Mulungu zimene mungazipeze.**

---

---

---

---

**Werangani *Masalmo 1* ndipo mufananize ndi m'mene ubale wanu ndi mau a Mulungu zidzasinthira kukhala kwanu kwa moyo.**

---

---

---

---

**Ndi zinthu zofunika kukhala ndi nthawi yanu yoti mukumane ndi Mulungu kudzera m'mau ake. Kodi baibulo lanu mukuwerenga pati? Lembani choonadi chimodzi chimene Mulungu wakuonetsani mu ndime imeneyi. Kodi inu mukukhala bwanji ndi choonadi chimenechi m'moyo wanu?**

---

---

---

---

---

---

---

---

## 5. PEMPHERO

*Ubale wanu ndi Ambuye Yesu Khristu sungathe kukura ngati palibe kulumikizana bwino. Zinthu ziwiri zofunika zimene zimapangitsa kupambana mmoyo wa Chikhristu ndi mau a Mulungu ndi pemphero. Mulungu amalankhura nanu pemene muwerenga baibulo ndipo inu mumalankhura naye kudzera mu pemphero. Ubale wanu ndi Mulungu udzakhala olimba pamene inu mudalira pemphero.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*KULUMIKIZANA*

**Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Kodi pemphero ndi lofunika bwanji m'moyo wanga?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kukuphunzitsani za m'mene mungakulire komanso kukhala m'moyo wamphamvu wa pemphero wolumikizana ndi Mulungu..*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Pemphero ndi kulumikizana kwa muntima kwa okhulupirira kupita kwa Mulungu.*

**NDIME ZAPAMTIMA:**

*"Ndipo cimene ciriconse mukacifunse m'dzina langa ndidzacicita, kuti Atate akalemekezedwe mwa Mwana. Ngati mudzapempha kanthu m'dzina langa, ndidzacicita" – Yohane 14:13-14*

*"Musadere nkhwana konse; komatu m'zonse ndi pemphero, ndi pembedzero, pamodzi ndi ciyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu. Ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana cidziwtso conse, udzasunga mitima yanu ndi maganizo anu mwa Khristu Yesu Ambuye wathu. – Afilipi 4:6-7*

# KODI PEMPHERO NDI CHIYANI?

---

## MFUNDO YOFUNIKIRA MU PHUNZIRO IRI!

Pemphero ndi kulumikizana kochokera mumtima wa okhulupirira kupita kwa Mulungu. Tiri ndi kulimbika kwenikweni kofika ku mpando wachifumu wa Mulungu kudzera pa ubale wathu ndi Yesu Khristu.

*“Amene tiri naye cikhazikika mtima ndi ciyandikiro colimbika, mwa cikhulupiriro ca pa lye.” – Aefeso 3:12*

*“Potero tilimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wacisomo, kuti tilandire cifundo ndi kupeza cisomo ca kuthandiza nthawi yakusowa.” – Ahebri 4:16*

## J. Pemphero linganenedwe mofuula komanso mwakachetechete

*“Ine ndinakuitanani, pakuti mudzandiyankha, Mulungu; cherani khutu lanu kwa ine, imvani mau anga.” – Masalmo 17:6*

*“Koma Hana anenena mu mtima; milomo yace inatukula, koma mau ace sanamveka:” – 1 Samueli 1:13*

## K. Pemphero likhonza kunenedwa ku gulu kapenanso m’tseri.

*“Ndipo m’mene ananena izi, anagwada pansi, napemphera ndi iwo onse.”  
– Machitidwe 20:36*

*“Koma iwe popemphera, lowa m’cipinda cako, nutseke citseko cako, nupemphere Atate wako ali m’tseri, ndipo Atate wako wakuona m’tseri adzabwezera iwe.” – Mateyu 6:6*

# NDI CHIFUKWA CHIYANI INU MUYENERA

---

## KUPEMPHERA?

Phunziro la pemphero ndi lodabwitsa kwambiri. Okhulupirira ambiri amasemphana ndi madalitso amene Mulungu walonjeza chifukwa samakhala ndi nthawi ndi Mulungu mu pemphero. Mulungu ali okhudzika ndi mbali ina iriyonse ya moyo wako imene mumakhala nayo ndi lye, ndipo akulonjeza kuyankha mapemphero posatengera kuti ndi akuru kapena aong’ono motani.

## A. Mulungu amayankha mapemphero

1. Inu mwayenera kukhala ndi chitsimikizo pamene mupemphera, podziwa kuti Mulungu amayankha mapemphero.

***Masalmo 86:6-7; Masalmo 145:18-19***

2. Inu mwayenera kukhala ndi chitsimikizo pamene mupemphera, podziwa kuti Mulungu adzayankha molingana ndi chifuniro chake.

***Yohane 14:13-14; 1 Yohane 5:14-15***

## **B. Pemphero limabweretsa kusintha m'moyo wanu**

1. Pemphero limabweretsa mtendere mumtima ndi m'malingaliro anu

***Afilipi 4:6-7***

2. Pemphero limatipanga ife kukhala otsata chifuniro cha Mulungu. Silimamupanga Mulungu kuchita zofuna za munthu.

***Mateyu 26:36-39; Akolose 1:9***

3. Pemphero limasintha maonedwe a munthu pa zinthu mu nyengo zosiyanasiyana za moyo wanu.

***2 Akorinto 12:7-10***

## **C. Pemphero limakubweretsani inu chifupi ndi Mulungu kuti lye yekha aonetse kukwanira kwake pa zosowa zanu.**

*“Ndipo kulimbika kotere kwa Mulungu tiri nako mwa Khristu, sikuti tiri okwanira pa ife tokha, kuyesera kanthu monga mocokera mwa ife tokha, kukwanira kwathu kucokera kwa Mulungu;”– 2 Akorinto 3:4-5*

1. Mulungu amadziwa chenicheni chimene inu mufuna ngakhale musanapemphe.

***Mateyu 6:8***

2. Mulungu amalora kuti tikhale ndi zofuna m'moyo mwathu ndi cholinga choti akubweretseni chifupi ndi lye.

***Masalmo 50:15***

3. Inu muyenera kudziwa kuti muli ndi zinthu zofuna m'moyo mwanu. Ndi chinthu choopsa kudzitsimikizikira nokha kuti simukusowa kanthu.

***Chibvumbulutso 3:16-17***



**ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu nthawi zina mumaopa kupemphera pamaso pa anthu?

Kodi inu mumadabwa ngati Mulungu akumva mapemphero anu?

Kodi maonedwe anu anasintha pamene munakhala ndi nthawi ndi Mulungu mu pemphero?

## **KODI INU MUYENERA KUPEMPHERA NTHAWI YANJI?**

**A. Mulungu amafuna inu kuti mudzillumikizana naye mopitilira kudzera mu pemphero.**

*Luka 18:1; 1 Atesalonika 5:17*

**B. Mulungu amafuna kuti inu mudzimuthokoza pa zonse zomwe zimachitika m'moyo mwanu.**

*1 Atesalonika 5:18; Aefeso 5:20*

**Phunzirani kuchokera ku zitsanzo za anthu ambiri m'malemba amene anali ndi moyo wokhazikika mu pemphero:**

1. Nehemiya anapempera mu nthawi imene anali ndi chosowa chadzidzidzi

*Nehemiya 1:4; 2:4*

2. Danieli anapitirira kupemphera ngakhale lamulo linaperekedwa kuti anthu asapemphere

*Danieli 6:4-10*

3. Davide anakhalabe m'moyo wa pemphero nthawi zonse

*Masalimo 5:3; 55:17*

## **KODI MUNGAPEMPHERE MOTANI?**

**A. Inu simuyenera kudzera mwa munthu wina aliyense pofuna kulankhurana ndi Mulungu. Inu muli ndi mwai wolumikizana ndi Mulungu mwa inu nokha.**

*1 Timoteo 2:5; Aefeso 2:18*

**B. Lankhurani ndi Ambuye ngati mzanu.**

*Yohane 15:13-15; Exodo 33:11*

**C. Sizoyenera komanso siziri mu baibulo kuti anthu adzibwerezabwereza mapemphero**

*Mateyu 6:7*

**D. Pempherani mapemphero a chindunji. Mapemphero a anthu okhulupirira maonongeka chifukwa amakhala a chisawawa komanso osakhazikika m'mau a Mulungu.**

*Afilipi 4:6*

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi mumatha kuona kuti mapemphero anu nthawi zina siali achindunji komanso obwerezabwereza?

Kodi inu muli ndi chinthu china chimene mukudalira nacho Mulungu panthawi ino?

## **KODI MUNGAPEMIPHERERE CHIYANI?**

Palibe “njira” yeniyeni imene tiyenera kuitsatira popemphera. Komabe mau a Mulungu amakamb komanso kuonetsa za mitundu yosiyana ya mapemphero mu baibulo. Simungakhale ndi chiyanjano chabwino ndi Mulungu ngati inu simungakhale ndi nthawi komanso kudzipereka kukhala ndi lye mu magawo anai a mapemphero.

*“Ndidandaulira tsono, poyambayamba, kuti acitike mapembedzo, mapemphero, mapembedzero, mayamiko, cifukwa ca anthu onse” – 1 Timoteo 2:1*

**A. MAPEMBEDZO – Izi ndi zopempha zochoka muntima komanso zimene zimatikhudza zimene zimamusuntha Mulungu.**

*Masalmo 6:8-9; Yakobo 5:16*

**B. – MAPEMBEDZERO- Izi ndi zopempha zapaderadera zimene timazipempha m'malo mwa anthu ena.**

*Aroma 15:30-32*

**c. MAPEMPHERO – Izi ndi zimene timalumikizana ndi Mulungu pokhazikika m'mau ake.**

*Masalmo 145:18-19*

**D. MAYAMIKO**– Izi zimaonetsa kuyamika kwathu pa Mulungu pa ntchito zake zodabwitsa

**Masalmo 100:4**

**MFUNDO YOFUNIKIRA KUDZIWA:**

Mulungu amafuna inu kuti mukhale pa ubale waphumphu ndi lye kudzera mu pemphero. Okhulupirira ambiri amasankha kusapemphera chifukwa amakhulupirira kuti Mulungu samagwira ntchito m'miyoyo yawo komanso mu nyengo zawo zenizeni. Pamene okhulupirira alephera kupemphera, amalepheranso kuona mayankho pa pemphero. Mulungu akulamulira inu kuti mudikire ndi chiyembekezo kuti muone m'mene akhonza kuyankhira pemphero lanu limene mwakhala mukupemphera mopitilira.

*“Citani khama m’kupemphera, nimudikire momwemo ndi ciyamiko” – Akolose 4:2*

*“Kupemphera kwathu kukuyenera kukhala kwa mphamvu komanso kochilimika ndikuikapo mphamvu kuti tisaleme. Pemphero liyenera kukhala lokhazikika ndipo ichi tisachikane, koma ndi kulimbika konse kumene kupangitse kuti tisalephere. Mkhristu wopemphera ali ngati msilikali wopanda mantha, kuti pamene mikangano ikurirakurira, amaonetsa kulimbika mtima kwake kodabwitsa kusiyana ndi m'mene ankachitira mu nkondo za m'buyomu.” – E.M. Bounds*

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi mumapemphera mochuluka bwanji?

Kodi munganene chitzanzo chimodzi chaposachedwapa cha momwe Mulungu anayankhira mapemphero anu?

## **KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA**

**1. Tchulani njira zitatu zimene pemphero lathandizira kukusinthani.**

---

---

---

**2. Gwiritsani ntchito malemba kufotokoza kuti pemphero ndi lofunika bwanji kwa inu.**

---

---

---

---

3. Kodi nthawi yabwino kwambiri kupemphera kwa okhulupirira ndi iti?  
Chifukwa chiyani?

---

---

4. Kodi tingaphunzire zotani mu ndime zimenezi za m'mene ife  
tingapempherere?

*1 Timoteo 2:5*

---

---

*Mateyu 6:7*

---

---

5. Tchulani zinthu zikuruzikuru zokhudza pemphero ndipo muonetse kuti  
zikuchokera mu ndime zANJI.

- A. \_\_\_\_\_
- B. \_\_\_\_\_
- C. \_\_\_\_\_
- D. \_\_\_\_\_

6. Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani  
chiyani?

---

---

---

---

---

---

---

## KUPHUNZIRA ZA BAIBULO PAWEKHA

Fotokozani mwa mau anu kuti kodi *1Timoteo 2:1-2* akutiphunzitsa chiyani  
zokhudza pemphero.

---

---

---

**Longosolani zotchinga zimene zimene zimalepheretsa pemphero molingana ndi ndime ziri m'musizi.**

***Masalmo 66:18; Yesaya 59:1-2***

---

***Miyambo 28:9***

---

***Mateyu 6:14-15***

---

***1 Petro 3:7; Akolose 3:19***

---

***Yakobo 4:2***

---

***Yakobo 4:3***

---

***Yakobo 21:13***

---

**Longosolani m'mau anu zimene Yesu amaphunzitsa ophunzira ake zokhudza pemphero pa *Mateyu 6:9-13*.**

---

---

---

---

---

## 6. MPINGO WAPAMALO

*Mulungu anakhazikitsa banja, boma komanso mpingo wapamalo ngati zinthu zitanu zapaderadera zimene ziri padziko pano. Wina aliyense wapatsidwa utsogoleri, madalitso komanso kuyakhapo za m'mene tachitira m'moyo uno. Mulungu wapereka mpingo wa pamalo kuti ukhale chotengera cha Mulungu kukwaniritsa zolinga zake pofikira anthu otaika komanso kukonzekeretsa amene ali opulumuka. Ndi chinthu chabwino kumvetsa kuti dongosolo la Mulungu ya pamoyo wanu likhonza kukwaniritsidwa pamene inu muli olumikizidwa ndi mpingo wa pamalo.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*KUMANGIRIRA*

**Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Kodi cholinga cha mpingo wa pamalo ndi chiyani?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kufotokoza kufunikira kwa mpingo wa pamalo mu moyo watsiku ndi tsiku wa okhulupirira.*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Mulungu anapereka mpingo kuti uphunzitse, ukonzekeretse ndi kumangirira overa mtima a Mulungu ku ntchito ya utumiki.*

**Ndime za pamtima:**

*“Ndipo lye anapatsa ena akhale atumwi; ndi ena aneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa; ndi ena aphunzitsi; kuti akakonzere overa mtima ku ntchito ya utumiki; kumangirira thupi la Khristu. Aefeso 4:11-12*

*“koma inu ndinu thupi la Khristu, ndi ziwalo, yense pa yekha.” – 1 Akorinto 12:27*

## KODI MPINGO WA PAMALO NDI CHIYANI?

### Ndi chinthu chofunikira kumvetsetsa za zimene mpingo wapamalo SULI...

1. Mpingo **SI** mpingo monga m'mene ufotokozedwera kuti gulu la mipingo yosiyanasiyana. Mpingo imene yatchulidwa mu chipangano chatsopano inali mu gulu a anthu okhulupirira otumikira limodzi.
2. Mpingo **SI** chinyumba chomangidwa. Matupi athu ali kacisi wa Mulungu, ndipo timalambira mu uzimu ndi mu choonadi.– **1 Akorinto 6:19-20; Yohane 4:24**
3. Mpingo **Sungathe** kuchotsedwa pamalo pake ndi zinthu zina. Pali zinthu zambiri zabwino (*TV; ndi alaliki pa walesi; uthenga wodzera pa makina a chizungu, mabuku ena otanthauzira mau a Mulungu, misonkhano ndi zina.*) zimene okhulupirira amayesera kugwiritsa ntchito kuti akwaniritse chosowa chimene mpingo wa pamalo wokha ungate kupereka. Ntchito ya Mulungu m'moyo mwanu ndiyokwaniritsidwa kudzera mu mpingo wa pamalo, ndipo palibe chinthu chimene chikhonza kulowa m'malo mwake.

- L. “Mpingo” ndi thupi la Khristu looneka ndi maso padziko. Ndi kuphatikiza kwa anthu ochuruka opulumutsidwa kuchokera m'maiko osiyanasiyana padziko lapansi.**

*“Koma inu ndinu thupi la Khristu, ndi ziwalo, yense pa yekha.” – 1 Akorinto 12:27*

*“...ndipo anakonza zonse pansu pa mapazi ace, nampatsa le akhale mutu pamtu pa zonse, kwa Ekklesia amene ali thupi lace, m'dzazidwe wa lye amene adzaza zonse m'zonse.” – Aefeso 1:22-23*

*“Ndipo lye ali mutu wa thupi, Ekklesiayo” – Akolose 1:18*

- M. “Mpingo wa pamalo” ndi thupi la amuna ndi akazi amene apulumutsidwa, amene anaitanidwa ndi Mulungu kuti amutumikire mwa njira ina yake molingana ndi chitsogozo cha baibulo.**

*“Paulo ndi Timoteo, akapolo a Yesu Khristu, kwa oyer mtima onse mwa Khristu Yesu, akukhala ku Filipi, pamodzi ndi oyang'anaira ndi atumiki:” – Afilipi 1:1*

*“Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu mwa cifuniro Mulungu ndi Timoteo mbaleyo kwa oyer mtima ndi abale okhulupirika mwa Khristu a m'Kolose...” – Akolose 1:1-2*

## N. Mulungu wadzodza ma ofesi awiri kuti apereke ndondomeko ndi utsogoleri pa mpingo wa pamalo.

### 1. Ofesi ya m'busa

Ntchito ya m'busa ndi kuyang'anira, kutsogolera, kudyetsa, ndi kusamala mpingo molingana ndi baibulo. Iye ayenera kuteteza mpingo ku ziphunzitsa zonyenga kudzera mu kulakira ndi kuphunzitsa choonadi cha mau a Mulungu. Iye wayeneranso kudzipereka kupempherera mpingo wonse.

**1 Timoteo 3:1-7; Ahebri 13:17; Macitidwe 6:4; 20:28-31**

### 2. Ofesi ya atumiki

Atumiki ndi atumiki odzala ndi Mzimu Woyera amane amasankhidwa kuchokera ku mpingo kuti atumikira anthu onse. Iwo ayanera kuthandiza abusa pa china chirichonse chimene chkhonza kulepheretsa kuti asatumikire mau a Mulungu, kupempherera komanso kuyang'anira mpingo wonse.

**1 Timoteo 3:8-13; Macitidwe 6:1-10**

## MAU A MULUNGU AMAFANIZIRA MPINGO WAPAMALO NDI THUPI LA MUNTHU.

Pambuyo pa chiukitso ndi kukwera kupita kumwamba, Yesu anaika Mzimu Woyera m'malo mwake amene amakhala mwa anthu (Mzimu wake), mau a Mulungu aphumphu (moyo), komanso mpingo wapamalo (thupi lake). Mzimu Woyera adzatsogolera inu kudzera m'mau a Mulungu kuti mukwaniritse ntchito yanu pa mpingo wapamalo.

#### – Membala wina aliyense ali ndi ntchito yapaderadera

*“Pakuti thupi silikhala ciwalo cimodzi, koma zambiri. Ngati phazi likati, Popeza sindiri dzanja, sindiri wa thupi, kodi siliri la thupi cifukwa ca ici? For the body is not one member, but many. Ndipo ngati khutu likati, Popeza sindiri diso, sindiri wa thupi, kodi siliri la thupi cifukwa ca ici? Ngati thupi lonse likadakhala diso, kukadakhala kuti kununkhiza? Koma tsopano, Mulungu anaika ziwalo zonsezo m'nthupi, monga anafuna. Koma ngati zonse zikadakhala ciwalo cimodzi likadakhala kuti thupi? Koma tsopano, pali ziwalo zambiri, koma thupi limodzi.” – 1 Akorinto 12:14-20*

#### – Palibe membala amene akhonza kuchita zinthu pa iye yekha.

*“Ndipo diso silingathe kunena kwa dzanja, sindikufuna iwe, kapenanso mutu kwa mapazi, Sindikufunani inu.” – 1 Akorinto 12:21*

#### – Membala wina aliyense ali ndi mbali yofunikira kwambiri.

*“Koma makamakatu ziwalo zoyesedwa zofoka m'thupi, zifunika; ndipo zimene tiziyesa zocepa ulemu m'thupi, pa izi tiika ulemu wocuruka woposa; ndi zinthu zosakoma zikhala naco cokometsera coposa. Koma zokoma zathu ziribe kusowa; koma Mulungu analumikizitsa thupi, napatsa ulemu wocuruka kwa cosowaco; kuti kusakhale cisiyano m'thupi.” – 1 Akorinto 12:22-24*

#### – Kugwira ntchito bwino kwa thupi kumaonekera mu umodzi.

*“Koma kuti ziwalo zifanane ndi kusamalana cina ndi cinzake. Ndipo cingakhale ciwalo cimodzi cimva zowawa, ziwalo zonse zimva pamodzi, cingakhale ciwalo cimodzi cilemekezedwa, ziwalo zonse zikondwera naco pamodzi. Koma inu ndinu thupi la Khristu, ndi ziwalo, yense payekha.” – 1 Akorinto*



# **KODI CHOLINGA CHA MPINGO WAPAMALO NDI CHIYANI?**

## **MFUNDO YOFUNIKIRA MU PHUNZIRO IRI!**

Mpingo wa pamalo ndi chinthu chokhacho chimene Mulungu anachikhazikitsa kuti ukathe kukwaniritsa Kutumidwa kwakuru. Mulungu amafuna kuti mpingo wapamalo, uphunzitse, ukonzekeretse, kumangirira anthu ku ntchito ya utumiki ndi kupereka malo kuti dongosolo la Mulungu likakwaniritsidwe m'moyo mwanu. Dongosolo la Mulungu m'moyo mwanu likhonza kukwaniritsidwa ngati inu muli olumikizidwa ndi mpingo wa pamalo.

### **A. Mpingo wa pamalo umakupatsani inu malo oti mukhonze kukula mu uzimu mu magawo atatu.**

*“kuti akakonzere oyera mtima ku ntchito ya utumiki; kumangirira thupi la Khristu.”  
Aefeso 4:12*

#### **1. Kukhala OPHUNZIRA pamenenso MUKUKONZEKERETSEDWA m'mau a Mulungu**

Pali nthawi imene munthu amayenera kuonera komanso kuphunzira pamene akukonzedwa wa uphumpu. Chinthu choyambirira pa moyo wanu ndi kumvera chiphunzitsa cha mau a Mulungu komanso kuphunzira kukhala chimene Mulungu akufuna kuti mukhale.

*Mateyu 11:28-30*

#### **2. Kukhala WANTCHITO amene AKUGWIRA ntchito ya utumiki**

Pamene mukukura mu ubale wanu ndi Khristu, padzakhala nthawi imene inu mudzayamba kutumikira mautumiki ena amene alipo kale pa mpingo wa pamalo.

*Mateyu 4:19; Yakobo 1:22-25*

#### **3. Kukhala MTSOGOLERI pamene MUKUMANGIRIRIDWA mu thupi la Khristu.**

Pamene moyo wanu wa uzimu ukukula, mukhonza kufika pa mulingo woti mukhonza kutumikira anthu ena mofanana ndi m'mene inunso munatumikiridwira.

*2 Timoteo 2:2*

### **MFUNDO YOFUNIKIRA KUDZIWA:**

Ndondomeko zitatatu zimenezi zikhonza kufananizidwa ndi makulidwe a munthu kuyambira pa mwana, wachinyamata komanso wankuru. Dongosolo limeneli la kukura muuzimu limatenga nthawi, choncho munthu ayenera kudikira mofatsa. Pamene mukura, tsimikizikani kukhala okhulupirika ku mpingo wa pamalo umene Mulungu anaukhazikitsa.

### **B. Mpingo wapamalo umatipangitsa kukhala ofanana ndi cifanizo cha Khristu.**

*“Kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa chikhulupiriro, ndi wa cizindikiritso ca Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa cidzalo ca Khristu:” – Aefeso 4:13*

### **C. Mpingo wapamalo umapereka muyeso woyesera ziphunzitso kuti zikhale zoonza**

*“Kuti tisakhalenso makanda, ogwedezekagwedezeka, natengeka-tengeka ndi mphepo yonse ya ciphunzitso, ndi tsenga la anthu, ndi kucenjerera kukatsata cinyengo ca kusoceretsa;” – Aefeso 4:14*

### **D. Mpingo wapamalo umathandiza kuti inu mudziwe ndi kukwaniritsa udindo wanu weni-weni mu thupi la Khristu.**

*“koma ndi kucita zoonza mwa cikondi tikakule m’zinthu zonse, kufikira lye amene ali mutu wa ndiye Khristu: kuokera mwa lye thupi lonse, lokowanidwa ndi lolumikizidwa pamodzi, pothandizinapo mfundo yonse, monga mwa kucititsa kwa ciwalo conse pa muyeso wace, licita makulidwe a thupi, kufikira cimango cace mwa cikondi.” – Aefeso 4:15-16*

### **Zokambirana:**

Kodi phunziro iri lakusinthani bwanji pakamvetsedwe kanu ka mpingo wapamalo?

Kodi munganene kuti muli pati pa mulingo wa kkla kwanu kwa moyo wa uzimu?

Kodi mukukhulupirira kuti udindo wanu ndi wotani mu mpingo?

# **KODI MUNGAPEZE BWANJI MPINGO WABWINO WA PAMALO?**

Pakhonza kukhala nthawi m'moyo mwanu imene Mulungu adzakutsogolerani ku malo ena kuti akakwaniritse ndongosolo lake mwa inu. Ndi chinthu chabwino kudziwa kuti muyenera kupeza mpingo wabwino wa pamalo kuti mutumikire Ambuye. Kumbukirani kuti ndongosolo la Mulungu pa moyo wanu lidzakhala lolumikizidwa ndi mpingo wapamalo. Iye sadzakutengani kuchokera ku mpingo wa pamalo kukakusiyani kumene kulibe mpingo ayi.

Anthu ambiri amasankha mpingo molingana ndi zinthu zooneka, monga dera, ubwino wa nyumba yopemphereramo, maimbidwe, ndi zochitika zimene zimachitika ku mpingo umenewo. Komabe, ndi zinthu zofunikira kuti muonetsetse pa zinthu zoyenera za uzimu za mpingo komanso kuzifananiza ndi zinthu zimene baibulo limanena zokhudza za m'mene mpingo wabwino wa pamalo ukhonza kukhalira. Ndi chinthu chabwino kwambiri kuti mukhale ofatsa pochita izi komanso kukhulupirira Mulungu kuti akutsogolerani!

## **A. Molingana ndi Macitidwe 2:41-47, mpingo woyamba unakhazikika pa...**

1. Kusamalira miyambo iwiri yopatulika ya mpingo
  - a. Ubatizo – *“Pamenepo iwo amene analandira mau ace anabatizidwa”*:– **ndime 41**
  - b. M'gonero wa Ambuye – *“... mkunyema mkate...”* – **ndime 42**
2. Kuphunzitsa mau a Mulungu – **ndime 42**
3. Chiyanjano ndi okhulupirira ena – **ndime 42**
4. Kupemphera limodzi– **ndime 42**
5. Kuchitira umboni za chisomo cha Mulungu ndi mphamvu yake– **ndime 43**
6. Kutumikirana ku zosowa za anthu– **ndime 44-45**
7. Kufikira anthu ena ku mudera – **ndime 46-47**
8. Kulemekeza ndi kukweza Mulungu – **ndime 47**
9. Kubweretsa anthu ochimwa ku chipulumutso cha Yesu Khristu– **ndime 47**

## **B. Mafunso otsatilawa akuthandizani inu kudziwa ngati pali umboni wa zikhalidwe zabwino zimene mpingo uyenera kupezeka nazo molingana ndi baibulo.**

1. Kodi inu mumakhazikika pa uthenga wabwino wa Yesu Khristu, komanso kodi anthu akupulumuka?

**Mateyu 7:20; Acts 2:47**

2. Kodi utsogoleri wa mpingo wanu umakhulupirira ndikuphunzitsa baibulo kuti ndi mau a Mulungu, ndipo ali olungama kutsogolera moyo wanu?

**Tito 1:9**

3. Kodi mpingo umatumiza ndi kuthandiza anthu amene amatumikira ngati amishoni?

**Macitidwe 13:1-3**

4. Kodi gulu la mpingo ndi atsogoleri amalimbikitsika kuwerenga ndi kuphunzira mau a Mulungu payekhapayekha?

**Macitidwe 17:10-12**

5. Kodi anthu amatha kusamala ena moona mtima, ndi kutumikira ku zosowa za thupi komanso uzimu?

**Agalatiya 6:10**

6. Kodi mpingo umazindikira za ofesi ya abusa komanso atumiki monga mwa malemba?

**1 Timoteo 3:1-13; Tito 1:5-9**

**Zokambirana:**

Kodi inu mukhonza kuona za zikhalidwe za mpingo molingana ndi baibulo?

## KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA

**26. Kodi pali kusiyana kotani pakati pa “mpingo” ndi “mpingo wa pamalo”?**

---

---

---

**27. Mpingo wa pamalo umafanizidwa ndi thupi la munthu monga mwa 1 Akorinto 12:14-27. Tchulani njira zinai zimene thupi la munthu limafanizidwira ndi m'mene mpingo wa pamalo umagwirira ntchito.**

- a. \_\_\_\_\_
- b. \_\_\_\_\_
- c. \_\_\_\_\_
- d. \_\_\_\_\_

**28.Ndi maudindo ndi utumiki ati amene mumakhulupirira kuti Mulungu mwina wapereka ku mpingo wapamalo?**

---

---

**29.Kodi ndi ndondomeko zitatu ziti zakukula muuzimu zimene ziyenera kukula mu mpingo wanu wapamalo?**

- a. \_\_\_\_\_
- b. \_\_\_\_\_
- c. \_\_\_\_\_

**30.Tchulani zina mwa zikhalidwe za baibulo zimene mkhristu akhonza kuyang'ana pofufuza mpingo wa pamalo.**

- a. \_\_\_\_\_
- b. \_\_\_\_\_
- c. \_\_\_\_\_
- d. \_\_\_\_\_

**31.Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?**

---

---

---

---

---

---

## **KUPHUNZIRA BAIBULO PAWEKHA**

**Kodi abusa ndi atumiki ndi ndani mu mpingo wanu wapamalo? Fotokozani mwa mau anu zimene *1Petro 5:1-4* and *Ahebri 13:17* akuphunzitsa za ubale wathu ndi abusa.**

---

---

---

---

---

---

**Werengani *Ahebri 10:24-25*. Ndime iyi ikutiphunzitsa kuti ndichofunikira kwa mamembala a mpingo wa pamalo kumakumana pafupipafupi. Molingana ndi**

ndime imeneyi, kodi ndi zinthu ziti zimene mumaphonyana nazo ngati simusonkhana ndi abale ena ku mpingo? Kodi pali china chirichonse m'moyo mwanu chimene mwasankha chimene chiri chofunikira kwambiri kusiyana ndi kusonkhana ndi abale ku mpingo wanu wa pamalo?

---

---

---

---

---

Taphunzira mu phunziro iri kuti mpingo wa pamalo, ukufanizidwa ndi thupi lamunthu monga mwa *1 Akorinto 12:14-27*. Chonde werengani ndime zotsatirazi ndipo mulembe zithunzithunzi zina za mpingo wa pamalo monga zimene Baibulo likunena.

**1. Macitidwe 20:28; Yohane 10:1-18; 1 Petro 5:1-4**

---

---

**2. Aefeso 2:19-22**

---

---

**3. Aefeso 5:25-32; 2 Akorinto 11:1-3**

---

---

## 7. MIYAMBO YA MPINGO

*Magulu a zipembedzo zosiyanasiyana amaphunzitsa zinthu zambiri zokhudzana ndi miyambo ya mpingo monga ubatizo ndi M'gonero wa Ambuye. Baibulo limaphunzitsa kuti Mulungu anapereka miyambo imeneyi ku mpingo kuti adzikumbukira imfa, kuikidwa m'manda komanso kuuka kwa Ambuye wathu Yesu Khristu. Ndi chinthu chofunikira kumvetetsa kuti ubatizo ndi m'gonero wa Ambuye sizofunikira kuchipulumutso chanu, koma ndi zofunikira chifukwa zimaonetsa kumvera kwana kwa Ambuye pambuyo pakulandira chipulumutso chanu.*

### **Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*KUMVERA*

### **Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Kodi kufunikira kwa ubatizo ndi m'gonero wa Ambuye ndi kotani pa moyo wanga?*

### **Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kupereka tanthauzo lenileni ndi chiphunzitso cha miyambo iwiri imeneyi imene inaperekedwa ku mpingo.*

### **Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Ubatizo ndi chionetsero cha kumvera koyamba kwa okhulupirira, ndipo m'gonero wa Ambuye ndi chikumbukiro cha imfa ya Yesu Khristu kufikira kubweranso kwake.*

#### **NDIME ZA PA MTIMA:**

*"Ndipo monga anapita paniire pao, anadza ku madzi akuti; ndipo mdindoyo anati, Taonapo madzi; cindiletsa ine ciani ndisabatizidwe? **Ndipo Filipino anati, Ngati ukhulupilira ndi mtima wako wonse, ukhoza. Ndipo anayankha nati, Ndikhulupilira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu.**" – Machitidwe 8:36-37 (Zindikirani kuti ndime 37 muline mu Baibulo la Chichewa)*

*"Pakuti nthawi zonse mukadya mkate uwu ndi kumwera cikho, mulalikira imfa ya Ambuye kufikira akadzaaye." – 1 Akorinto 11:26*

# GAWO1: UBATIZO

Pafupifupi, magulu onse a chipembedzo amaphunzitsa za njira zina ina yake ya ubatizo monga mwa chiphunzitso chawo, komanso ziphunzitso zimenezi zimakhala zosiyanasiyana. Gawo iri likofotokoza za choonadi chenicheni cha baibulo ndi kufotokoza za chiphunzitso chimenechi kuti mumvetse bwino za chimene Mulungu amafuna kunena mogwirizana ndi ubatizo.

## KODI UBATIZO NDI CHIYANI?

---

**O. Ubatizo wa m’madzi umaonetsera za imfa, kuikidwa m’manda ndi kuuka kwa Yesu Khristu.**

*Aroma 6:1-7*

**P. Ubatizo wa m’madzi ndi umboni wakunja woonetsa za chipulumutso komanso kukhala ndi Yesu.**

*Aroma 1:16; 10:11*

Inu mukuonetsa kugulu kuti mwakhulupirira imfa ya Khristu pa mtanda m’ malo mwanu. Pamene muikidwa m’madzi, mukuonetsa kuti machimo anu aikidwa m’manda pamodzi ndi Khristu. Pamene muturuka m’madzi, mukulengeza za kuuka kwanu ndi Khristu, ndipo wakuukitsani inu kuti muyende m’ moyo watsopano.

**Q. Ubatizo wa m’madzi ndi chionetsero kugulu kuti inu mwasankha kutsat ndi kumvera Ambuye Yesu Khristu. Yesu anapereka chitsanzo kwa ife pomvera kubatizidwa asanayambe utumiki wake.**

*Mateyu 3:13-17*



## MFUNDO YOFUNIKIRA MU PHUNZIRO IRI!

*“Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya panso pano.” – Mateyu 28:19-20*

Molingana ndi baibulo, chotitika choyamba cha kumvera kwa okhulupirira ndi mwambo wa ubatizo. Ndi chinthu chofunikira pa kukura kwanu kwa uzimu. Musanaphunzire zakutsata Yesu Khristu, muyenera kuvomereza kumvera chochitika choyamba cha kumvera Mulungu kuti chimafuna inu kutsata chipulumutso chanu. Kukura kwanu mwa Yesu Khristu kusokonekera ngati inu simumvera lamulo losavuta la Mulungu loti mubatizidwe.

## KODI OYENERA KUBATIZIDWA NDI NDANI?

**O. Ambuye akulamulira aliyense amene waika chikhulupiriro chake mwa Yesu Khristu monga Mbuye ndi Mpulumutsi kuti abatizidwe.**

*“Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, **ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera**” – Mateyu 28:19*

**P. Pali zoyenera ziwiri zimene oyenera kubatizidwa ayenera kukwaniritsa**

*“Ndipo monga anapita paniire pao, anadza ku madzi akuti; ndipo mdindoyo anati, Taonapo madzi; cindiletsa ine ciani ndisabatizidwe? **Ndipo Filipino anati, Ngati ukhulupilira ndi mtima wako wonse, ukhoza. Ndipo anayankha nati, Ndikhulupilira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu.**” – Machitidwe 8:36-37 (Zindikirani kuti ndime 37 muline mu Baibulo la Chichewa*

**Choyenera #1** – Kukhulupirira mumtima za Yesu Khristu ngati Ambuye ndi Mpulumutsi

**Choyenera #2** - Kuvomereza kuti Yesu Khristu ndi Ambuye ndi Mpulumutsi

*Aroma 10:9-10*

# KODI MUYENERA KUBATIZIDWA NTHAWI YANJI?

---

A. Baibulo limatiphunzitsa kuti muyenera kubatizidwa pambuyo pa kupulumutsidwa.

**M'munsimu muli ndime zina zoonetsa kuti anthu anabatizidwa atalandira chipulumutso**

- Anthu a ku Samariya – **Mach 8:12**
- M'dindo wa ku Aitopiya – **Mach 8:36-39**
- Mtumwi Paulo (Saulo) – **Mach 9:18**
- Korneliyo ndi banja lake - **Mac 10:44-48**
- M'dindo wa ku Filipi – **Mach 16:25-33**
- Anthu a ku Korinto – **Mach 18:7-8**

B. Muyenera kubatizidwa panthawi imene mwamvetsetsa lamulo la Mulungu ndi cholinga cha ubatizo.

Kodi mukutsimikizika kwatunthu kuti mwapulumutsidwa?

---

Kodi munabatizidwapo mutalandira chipulumutso? Ngati sichoncho, mubatizidwa liti?

---

# KODI INU MUYENERA KUBATIZIDWA MOTANI?

---

A. Chitsanzo chirichonse cha m'baibulo cha munthu wobatizidwa chimachitika monyika m'madzi.

*“Ndipo Yesu pamene anabatizidwa, pomwepo **anaturuka m'madzi...**”*  
– **Mateyu 3:16**

*“...ndipo anatsikira onse awiri **kumadzi**, Filipo ndi mdindoyi, ndipoi anambatiza iye.”*–  
**Macitidwe 8:38**

## B. Njira ya baibulo ya ubatizo ndi kunyika m' madzi kwathunthu.

*“Cifukwa cace tinaikidwa m' manda pamodzi ndi iye mwa ubatizo kulowa muimfa; kuti monga Kristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemero wa Atate, coteri ifenso tikayende m' moyo watsopano.”— Aroma 6:4*

1. Liwu loti “kubatiza” limatanthauza kunyika, kumiza, kulowetsa pansu, komanso kumira kwa chinthu.
2. Ubatizo sungaonetse imfa, kuikidwa m' manda kapena kuuka kwa Yesu Khristu ngati munthu sanyikidwa kwatunthu m' madzi.
3. Kuthira madzi pamutu si njira ya ubatizo monga mwa baibulo chifukwa siimaonetsa imfa, kuikidwa m' manda komanso kuuka kwa Yesu Kristu.

## KODI MUNGABATIZIDWE KUTI?

- A. Ubatizo wanu wayenera kuchitika ndi ulamuliro wa mpingo wa pamalo umene umaphunzitsa chiphunzitso choona pankhani ya ubatizo.
- B. Malo a ubatizo sichinthu zofunikira poyerekeza ndi umboni wa kugulu umene umaonetsa za kuzindikirika kwanu ndi Yesu Khristu mpulumutsi ndi Ambuye.
- C. Inu muyenera kubatizidwa ndi madzi ambiri kuti mukhonze kunyikidwa bwino.

*Yohane 3:23; Machitidwe 8:36-37*

## GAWO 2: M'GONERO WA AMBUYE

Monga ubatizo, m'gonero wa Ambuye (chijanano) siukudzana kwambiri ndi chipulumutso, koma ndi wofunikira pa moyo wanu watsopano mwa Yesu Khristu. Gawo la phunziro iri lakonedwa kuti likupatseni kumvetsetsa kwa baibulo kwa momwe mungatanthauzire ntchito chikumbukiro cha m'gonero wa Ambuye pa moyo wathu wa chikhristu.

# **KODI TIYENERA KUCHITA M'GONERO WA AMBUYE CHIFUKWA CHIYANI?**

Cholinga chenicheni chimene tiyenera kuchitira m'gonero ndichakuti tikumbukire pafupipafupi za mphatso ya mtengo wapatali ya Yesu imene anapereka chifukwa cha machimo anu.

- A. Yesu anakhazikitsa za mwambo wa m'gonero pamene ananena kuti, “... citani ici kuti cikhale cikumbukiro canga.”**

*Luka 22:14-20*

- B. Mtumwi Paulo akutsimikiza za kupanga m'gonero wa Ambuye mu Chipangano Chatsopano monga chikumbukiro cha nsembe ya Yesu Khristu pa tchimo.**

*1 Akorinto 11:20-34*

# **KODI M'GONERO WA AMUYE UMAYIMIRA CHIYANI?**

- A. Mkate wopanda chotupitsa umagwiritsidwa ntchito kuimira thupi lenileni la Yesu Khristu.**

1. Chotupitsa m'baibulo chimatanthauzira ngati chinyengo, tchimo komanso chiphunzitso chonyenga. Izi zinarinso zoletsedwa pa bwando la Pasaka la ana a Israyeli.

*1 Akorinto 5:6-8; Mateyu 16:6-12; Deuteronomo 16:1-4*

2. Mkate umanyemedwa kukumbutsa za thupi la Yesu limene linaperekedwa chifukwa cha inu.

*1 Akorinto 11:24; Yesaya 53:4-6*

- B. Madzi a mtengo wa mphesa amaimira mwazi wopanda banga wa Yesu Khristu.**

1. Madzi a mtengo wa mphesa sanali osasa ndi chifukwa chake pamene “chikho” chitchulidwa pa m'gonero wa Ambuye zimatanthauza za “chipatso cha mphesa”.

*Marko 14:25; Luka 22:18*

2. Madzi a mtengo wa mphesa “amathirdwa” kutikumbutsa za mwazi wa Yesu umene unathiridwa kamba ka machimo.

*Mateyu 26:26-29*

# KODI CHOLINGA CHA M'GONERO WA AMBUYE NDI CHIYANI?

## A. M'gonero wa Ambuye umakupatsani maonedwe abwino a zinthu.

**Maonedwe atatu amene muyenera kukhala nao pamene mukudya m'gonero wa Ambuye.....**

1. **Kuyang'ana za M'BUYO** – Izi zimakukumbutsani za zimene Yesu anachita polipira machimo athu.

Kukumbukira za imfa ya Yesu Khristu zimatikumbutsa kuti machimo anu abisika ndi mwazi wake.

**1 Akorinto 11:24-25**

2. **Kuyang'ana za MTSOGOLO** – Izi zimatikumbutsa kuti Yesu Khristu akubweranso kachiwiri.

Inu mukhumbe kukhala oyera kuti musadzachite manyazi pamene Ambuye Yesu Khristu abweranso kachiwiri.

**1 Akorinto 11:26**

3. **Kuyang'ana za NTHAWI INO** — Izi zimatikumbutsa zoti tidziweruze tokha pa machimo athu.

Mulungu amafuna kuti inu mudziyese nokha pa moyo wanu ndi cholinga choti mudziweruze pa machimo anu ndi kutembenuka.

**1 Akorinto 11:27-28**

## B. M'gonero wa Ambuye umasunga chiyero mu thupi la Khristu.

1. Ndi nthawi yodziyetsa ku mkwiyo ndi tchimo zimene zimakudetsani. Inu mudzabweretsa chilango cha Mulungu pa inu nokha ngati mutenga m'gonero wa Ambuye “kosayenera” makamaka polephera kudziyesa moyo wanu wauzimu ndi kuyenda kwanu ndi Mulungu.

**1 Akorinto 11:27-32**

2. Zimateteza kuti tchimo limene anthu sanalape lisakhalebe mu mpingo.

**1 Akorinto 5:1-8**

## **MFUNDO YOFUNIKIRA MU GAWO IRI.....**

*Zinthu zofunikira kwambiri mu mbiri ndi imfa, kuikidwa m'manda komanso kuuka kwa Yesu Khristu ndi kubweranso kwake kwa ulemelero. Monga m'mene mumachitira m'moyo mwanu pokhala ndi masiku ena apadera "okumbukira," M'gonero wa Ambuye umatsatidwanso ndi mpingo monga chikumbukiro cha nsembe ya Yesu ku machimo anu ndi chikumbutso kuti adzabweranso kachiwiri.*

## **KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA**

**6. Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu akulamulira a Khristu kuti abatizidwe?**

---

---

---

**7. Kodi njira ya baibulo ya ubatizo ndi yotani, nanga imaimirira chiyani?**

---

---

---

**8. Kodi zomuyeneraza munthu kuti abatizidwe ndi zotani molingana ndi baibulo?**

---

---

---

**9. Kodi ndi chifukwa chiyani aKhristu akulamulidwa kuti atenge gawo pa m'gonero wa Ambuye?**

---

---

---

**10. Kodi m'gonero wa Ambuye umaimira bwanji mazunzo a Yesu Khristu?**

---

---

---

---

---

**11. Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?**

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

## **KUPHUNZIRA BAIBULO PAWEKHA**

**Fotokozani mwa mau anu zimene *Machitidwe 8:36-38* akuphunzitsa zokhudza ubatizo.**

---

---

---

---

---

**Werengani ndime ina iriyonse m'munsimu ndipo mufotokoze za nthawi imene wina aliyense anabatizidwa.**

***Machitidwe 8:12-13***

---

---

***Machitidwe 10:44-48***

---

---

***Machitidwe 18:7-8***

---

---

**Fotokozani mwa mau anu zimene Yesu ankaphunzitsa ophunzira ake molingana ndi *Yohane 6:48-58*.**

---

---

---

---

**Werengani *Mateyu 26:26-30* ndipo mwachidure mufananize M'gonero wotsiriza ndi m'mene M'gonero wa Ambuye umachitikira mu mpingo wanu.**

---

---

---

---

---



## 8. AKHRISTU ENA

*Inu munalowa m’banja la Mulungu kudzera mu kubadwa kwa UZIMU pamene munakhulupirira Yesu Khristu monga Mpulumutsi wanu. Tsopano inu muli ndi banja la uzimu limene muli abale ndi alongo amene anapulumsidwa ndi imfa, kuikidwa m’manda kuuka kwa Yesu Khristu. Phunziro iri likutsogolerani inu pokamba za ubale wapaderadera umene muli nawo mu banja la uzimu.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*CHIYANJANO*

**Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Kodi ubale wanga ndi akhristu ena ndi wotani?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kukupatsani inu kumvetsetsa kwabwino za m’mene thupi la Khristu likhonza kugwirira ntchito ngati banja limodzi.*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Inu muyenera kukhala ndi ubale wa pa inu nokha ndi Yesu musanakhale pa chiyanjano ndi okhulupirira ena.*

**Ndime zapamtima:**

*“Mulungu ali, wokhulupirika amene munaitanidwa mwa iye, ku ciyanjano ca Mwana wace Yesu Kristu, Ambuye wathu”*

**– 1 Akorinto 1:9**

*“Koma ngati tiyenda m’kuunika, monga lye ali m’kuunika, tiyanjana wina ndi mnzace, ndipo mwazi wa Yesu Mwana wace utisambitsa kuticotsera ucimo wonse.” – 1 Yohane 1:7*

## **KUMVETSETSA ZA UBALE WANU NDI ANTHU ENA M'BANJA LA UZIMU LA MULUNGU**

**R. Abale anu ndi alongo anu mwa uzimu ndi okhawo amene ali obadwa mwatsopano kudzera mu imfa, kuikidwa m'manda ndi kuukanso kwa Yesu Khristu.**

*“Cifukwa kuti iwo amene iye anawadziwiratu, iwowa anawalamuliratu afanizidwe ndi cifaniziro ca Mwana wace, kuti iye akakhale mwana woyamba wa abale ambiri.”  
– Aroma 8:29*

*“Taonani, cikondico Atate watipatsa, kuti tichedwe ana a Mulungu; ndipo tiri ife otere. Mwa ici dziko lapansi silizindikira ife, popeza silimzindikira iye. Okondedwa, tsopano tiri ana a Mulungu, ndipo sicinaoneke cimene tidzakhala. Tidziwa kuti, pa kuoneka iye, tidzakhala ofanana ndi iye, Pakuti tidzamuona iye monga ali.” – 1 Yohane 3:1-2*

**S. Iwo amene sanabadwe mwatsopano amene siali amodzi ndi kuuzimu, komanso siali ana a Mulungu.**

*“...Ndiko kuti, ana a thupi sakhala iwo ana a Mulungu ai; koma ana a lonjezo awerengedwa mbeu yace.” – Aroma 9:8*

*“Cifukwa cace, Turukani pakati pao, ndipo patukani, ati Ambuye, ndipo musakhudza kanthu kosakonzeka; ndipo Ine ndidzalandira inu, ndipo ndidzakhala kwa inu Atate, Ndi inu mudzakhala kwa Ine ana amunandi akazi, anena Ambuye Wamphamvuyonse.” – 2 Akorinto 6:17-18*

## **KUMVETSETSA ZA UDINDO WANU M'BANJA LA UZIMU LA MULUNGU**

**E. Muli ndi udindo wa uzimu kwa abale ndi alongo mwa Khristu.**

1. Pemphererani banja lanu.

*1Atesalonika 1:2-3; 2Timoteo 1:3*

2. Gwirani ntchito yofalitsa uthenga wabwino limodzi.

*1 Akorinto 3:5-10*

3. Gawanani mavuto ndi zolemetsa pa banja lanu.

***1 Akorinto 12:24-26; Aroma 12:13-16***

## **F. Muli ndi udindo wakuthupi kwa abale ndi alongo mwa Khristu.**

1. Khalani ozindikira bwino za zosowa za banja lanu ndipo muthandize kuti zikwaniritsidwe.

- a. Tumikirani kwa okhulupirira a pampingo panu.

***1 Yohane 3:16-18; Yakobo 2:15-16***

- b. Tumikirani kwa okhulupirira ena ku mipingo ina.

***Machitidwe 11:27-30; Agalatiya 6:10***

2. Tumikirani banja lanu modzichepetsa potenga zosowa za anthu kukhala zoyamba kusiyana ndi zanu.

***Afilipi 2:3-4***

## **G. Muli ndi udindo wina ngati munthu pa inu nokha kwa abale ndi alongo mwa Khristu.**

1. Limbikitsani ndi kuthandiza banja lanu

***Aroma 15:1-2; Ahebri 13:3; 1 Atesalonika 5:11***

2. Kondani banja lanu monga baibulo linenera ndi malingaliro abwino

***Yohane 13:34-35; 1 Yohane 3:14-16***

3. Khalani odekha ndi banja lanu.

***Aroma 15:5-7***

4. Khalani oona mtima ndi banja lanu polankhula choonadi mu chikondi.

***Aefeso 4:15, 25, 29***

5. Khululukirani banja lanu monganso m'mene Mulungu anakhulukira inu.

***Aefeso 4:32***

### **Zokambirana:**

Kodi ndi mapemphero enieni ati amene inu mumapempherera mamembala a banja la mpingo wanu?

Kodi inu mukudziwapo m'bale kapena m'longo mwa Khristu amene akuyenera kutumikiridwa mwa kuthupi? Kodi inu mungawatumikire bwanji?

Kodi inu munatumikiridwa bwanji ndi mamembala a banja la mpingo wanu?

## **KUMVETSETSA ZA KUFUNIKA KWA CHIYANJANO M'BANJA LA UZIMU LA MULUNGU**

---

### **MFUNDO YOFUNIKIRA MU PHUNZIRO IRI!**

Chiyanjano choona cha m'baibulo chimapezeka mwa Ambuye Yesu Khristu. Pamene okhulupirira akukula mu chiyanjano ndi Mulungu aliyense payekhapayekha, amakhalanso akuyanjanitsidwa wina ndi mzake. Inu muyenera kukhala ndi ubale wabwino pa inu nokha ndi Yesu musanakhale pa chiyanjano ndi okhulupirira ena.

***1 Yohane 1:1-7; 1 Akorinto 1:9-10***

### **A. Chiyanjano cha baibulo chinthu chimodzi chodziwika chimene chimalumikiza okhulupirira onse mwa Ambuye Yesu Khristu.**

Inu mumagawana zochitika pa moyo komanso utumiki ndi wina aliyense anapulumutsidwa kudzera mu imfa, kuikidwa m'manda komanso kuuka kwa Yesu Khristu. Ndi chinthu chofunikira kwa inu kuti mukhale limodzi ndi okhulupirira anzanu pazochitika, zokambirana, komanso ubale chifukwa zimapereka mwayi wa chiyanjano chomwe Baibulo limaphunzitsa kuti chikhale m'moyo mwanu. Okhulupirira amakhala pa umodzi mu chiyanjano, osati pamene asonkhana, koma pamene agawana pa zochitika za moyo wa uzimu.

***Afilipi 1:3-6; 2:1-2***

### **B. Okhulupirira amakhala amodzi kudzera mu chiyanjano cha baibulo pamene agawana pa zochitika za moyo wa uzimu.**

7. Chiyanjano chimalumikiza okhulupirira mu pemphero.

**2 Akorinto 1:11**

8. Chiyanjano chimalumikiza okhulupirira mu chikhulupiriro

**Aroma 1:12; Afilipi 1:27**

9. Chiyanjano chimalumikiza okhulupirira mu utumiki ndi ntchito

**2 Akorinto 8:4; Agalatiya 2:9**

10. Chiyanjano chimalumikiza okhulupirira mu zowawa.

**Afilipi 3:10; 1 Petro 4:13; 5:1; Ahebri 13:3**

11. Chiyanjano chimalumikiza okhulupirira mu chiphunzitso.

**Machitidwe 2:42; Aroma 16:17; Yohane 17:8, 20-21**

## **KUMVETSETSA ZA M'MENE TINGATHANE NDI MIKANGANO MU BANJA LA UZIMU LA MULUNGU.**

### **MFUNDO YOFUNIKIRA KUDZIWA:**

*“Koposa zonse mukhale naco cikondano ceni ceni mwa inu nokha; pakuti cikondano cikwiriritsa unyinjira wa macimo” – 1 Petro 4:8*

Koma mwatsoka, pakhonza kukhala nthawi zina zimene akhristu mumpingo wanu akhumudwitsidwa ndi abale komanso alongo mwa Khristu. Nthawi zambiri zokhumudwitsa ngati izi zimakhala zovuta kuthana nazo chifukwa cha maubale oyandikana amene alipo mu banja la uzimu limeneli. Zimatengera kulimba mtima, kukhala ndi khalidwe labwino komanso kukhwima moyo wa uzimu kuti munthuyi athane ndi mikangano mu banja. Chikondi, kufatsa, kukhululuka, komanso kusamala wina ndi mzake zimene tiyenera kuonetserana zidzaphimba zokhumudwitsa zina “zazing’onozing’ono.” Komabe, pamene zokhumudwitsa ziri zazikuru ndithu, baibulo limatipatsa mfundo zenizeni zothana ndi mikangano pakati pa abale ndi alongo mwa Khristu.

### **A. Kodi inu muyenera kupanga chiyani ngati mwakhumudwitsa winawake?**

1. Inu muyenera kukhala munthu osavuta kukufikira pamene m’bale kapena m’longo akaufuna kuyanjanitsidwa.

a. Ndi chinthu chofunikira kwa inu mukhale okhwima mu uzimu ndikukhala munthu osakhumudwa mwachangu pamene ena alankhura nanu.

**Yakobo 3:13-18; Masalimo 119:165**

- b. Inu mukhonza kupangitsa Mulungu kuti asalowere pothana ndi mikangano yanu ngati inu mukhala okura mtima komanso otengera zimene inu mukumva mthupi mwanu.

***Miyambo 25:28; 16:32; 1 Samueli 25:17***

**2. Dziyeseni nokha kuti muonetsetse kuti simukukhala monga mwa thupi**

Nthawi zina, mukhonza kukhala osadziwa kuti maonedwe anu ndi zochita zanu zakhumudwitsa wina wake. Pamene mwadziwa kuti mwakhumudwitsa wina wake, muyenera kudziyesa nokha ndi cholinga choti musakhale kuthupi, ndipo kuti moyo wanu ukhale monga mwa chikhalidwe cha mau a Mulungu.

***Mateyu 7:1-5; Aroma 14:1; 15:1***

**3. Funitsitsani kuyanjana mwachangu m'bale ndi m'longo amene mwakhumudwa naye.**

Tengani udindo wanu ndi kufunitsitsa kuyanjana mwachangu pa ubale wanu ndi munthu winayo. Abale ndi alongo anu mwa Khristu ali oyenera kuti mukhale nawo limodzi bwino.

***Mateyu 5:23-26; Aefeso 4:26-27***

**B. Kodi muchite chiyani pamene munthu wina wakhumudwitsa inu?**

**1. Mufikireni munthu amene wakukhumudwitsani mwanseri komanso kukambirana naye.**

Musachite mabodza kapena kukamba za iye ndi anthu ena amene sakukhudzidwa ndi nkhaniyo. Mikangano yambiri pakati pa okhulupirira ikhonza kukonzeka pamene wina aliyense aitenga nkhani bwino pokhala anthu amene akura mu chiphunzitso cha baibulo ndi kukhala nacho chikondi. Mu nthawi zambiri, mikangano imakupatsani chikondi chachikuru kwa wina ndi mzake, ndipo ubale wanu umakhala olimba.

***Mateyu 8:15***

**2. Ngati mikangano siingathe kukonzedwa mwa nseri, funsani okhulupirira wankuru muuzimu kuti athandize ndi kuti awatsogolere anthu awiriwa kugwirizana atatha kukambirana.**

Munthu ameneyu akhale mkuru wa mpingo amene ali ndi luso lodziwa kuunikira mwanzeru ndi kupereka thandizo limene liri losakondera wina aliyense motsatira baiubulo..

***Mateyu 8:16***

**3. Ngati palibe kugwirizanabe, tengani nkhani yanu ndi kupita nayo kwa utsogoleri wa ubusa ndi kutsata dongosolo la mpingo.**

***Mateyu 18:17***

- a. Abusa akhonza kuthana ndi nkhani yanu pamene Mzimu Woyera awatsogolera potsatira ndondomeko imene Mulungu anaikhazikitsa.

***Ahebri 13:7, 17***

- b. Ngati kuli kotheke, utsogoleri wanu wa uzimu ukhonza kubweretsa nkhani ija ku mpingo mwa njira ya kuimitsidwa.

***Aroma 16:17; 1 Akorinto 5:9-11; 2 Atesalonika 3:6, 14***

- 4. **Ngati munthu amene wakukhumudwitsani walapa ndipo akufuna kuti muyanjanenso, ndiye kuti inu muyenera kukhululuka pa chokhumudwitsacho.**

***Mateyu 18:21-22***

- a. Kukhululuka kwenikweni kumachokera mu mtima woona umene uli okonzeka kukhululuka monganso m'mene Mulungu anatikhululukira.

***Aefeso 4:32; Akolose 3:12-14***

- b. Kukhululuka kwenikweni kukhonza kubwera pokhapokha ngati olakwayo walapa.

***Luka 17:3-4***

- c. Kukhululuka kwenikweni nthawi zonse kumawatsogolera anthu kuti ayanjane komanso kukonzanso ubale.

***Agalatiya 6:1-2***

### **C. Inu muyenera kukhala opanda banga nthawi zonse ya mikangano ndi wokhulipilira wina.**

Pali mfundo zina zofunikira zoti mupewe kuti muonetsetse kuti simukulepheretsa kuyanjana ndi m'bale kapena m'longo mwa Khristu.

- 1. **Musapite ku dziko lotaika kuti lithetse mavuto a auzimu a mu thupi la Khristu.**

Ngati chokhumudwitsa chachitika, gwiritsani ntchito mfundo zimene ziri mu phunziro iri kuti muthane ndi vuto lanu potsata mau a Mulungu. Inu gwiritsani ntchito anthu amene ali ndi ulamuliro woyenera ngati pali mulandu wina uli wonse, ndi cholinga chofuna kuteteza ndi kusamala nthupi la Khristu ndi mpingo wake.

***1 Akorinto 6:1-6; Aroma 13:1-5***

- 2. **Musamupatse Satana mwayi oti agwiritse mikangano yanu kukuonongani inu komanso mpingo.**

Utumiki wa Mulungu komanso kuyenda naye ndi zinthu zofunikira kwambiri kusiyana ndi kudandaula, posatengera kuti ndizokura bwanji. Ngakhale mutakhala kuti mwazunzika ndi china chake choipa, perekani nkhani yanu kwa Mulungu ndi kusiya zonse m'manja mwake.

***1 Akorinto 6:7; 2 Akorinto 2:10-11***

3. **Musaleke kupempherana monga abale ndi alongo mwa Khristu.**  
Khalani a machawi ndi kuyesetsa kuti muzipemphera ndi malingaliro abwino.

*Mateyu 5:43-48; Aroma 12:14*

4. **Musayese kupeza mwayi kuti mubwezere.**  
Khulupirani Mulungu kuti athana ndi nyengo yanu, ngakhale zitakhala kuti sizinakonzedwe kwa muyaya.

*Aroma 12:17-21; Miyambo 20:22*

5. **Musalore kukhala ndi kuwawidwa mtima mkati mwanu.**  
Kuwawidwa mtima kumakhudza wina aliyense pa moyo wanu.

*Ahebri 12:14-15; Aefeso 4:31*

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu munayamba mwakhumudwitsapo okhulupirira wina? Kodi munthu ameneyo anachitapo chani pa chinthu ichi?

Kodi inu munayamba mwakhumudwitsidwapo ndi okhulupirira wina? Kodi izi zinasintha bwanji ubale wanu?

Kodi inu muli ndi nkhani ina ndi okhulupirira wina imene ikusowekera kuthana nayo monga mwa chitsogozo cha baibulo?

## **KAUNUNI NDI ZOKAMBIRANA**

32. **Fotokozani za ubale wanu ndi okhulupirira ena.**

---

---

---

33. **Tchulani maudindo anai amene amayenera kukhala kwa Akhristu ena, ndipo mupereke umboni wochokera m' malemba.**

e. \_\_\_\_\_

f. \_\_\_\_\_

g. \_\_\_\_\_

h. \_\_\_\_\_

34. **Kodi mau akuti “chiyanjano” amatanthauza chiyani?**



---

---

**35. Tchulani zitsanzo zinai za m'mene okhulupirira akhonza kukhala amodzi mwa chiyanjano.**

- d. \_\_\_\_\_
- e. \_\_\_\_\_
- f. \_\_\_\_\_
- g. \_\_\_\_\_
- h. \_\_\_\_\_

**36. Inu muyenera kufunitsitsa kukhala pa chiyanjano ndi Akhristu amene wakukhumudwitsani. Tchulani ndondomeko zimene tingatsate pamene tikufuna kuyanana ndi ena.**

- e. \_\_\_\_\_
- f. \_\_\_\_\_
- g. \_\_\_\_\_
- h. \_\_\_\_\_

**37. Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?**

---

---

---

---

---

---

---

## **KUPHUNZIRA BAIBULO PAWEKHA**

Okhulupirira ena amachiona chinthu chosavuta kupanga ubale mkati mwa mpingo kusiyana ndi ena. Werengani Machitidwe 2:46-47 ndi 1Petro 4:8-9 ndipo mulembe zina mwa zitsanzo zimene inu mungathe kugwiritsa ntchito ubwino wanu kuti mulimbikitse chiyanjano m'moyo wanu.

---

---

---

---

Werengani ndime zotsatirazi ndipo mulembe mau asanu ndi amodzi amene akugwiritsidwa ntchito pokamba za chiyanjano ndi okhulupirira ena mu Chipangano Chatsopano.

*1 Atesalonika 3:2*

*Afilipi 2:25*

*Filemoni 1:2*

*Akolose 4:7*

*3 Yohane 1:8*

*Akolose 4:11*

Werengani Afilipi 4:1-3. Mu kalata ya Paulo yolembedwa ku mpingo wa Filipi, Paulo akulimbikitsa Euodiya ndi Suntuke kuti akonze vuto la kusiyana chifukwa izi zimakhudza anthu onse owazungulira. Kodi pali nyengo ina m'moyo wanu imene inu ndi okhulupirira mukusowekera kuyanjana? Ndi njira ziti zimene inu mungatenge kuti ubale wanu ukozenkenso? Ndi njira ziti zimene inu mukufunanso kuti mutenge kuti utumiki usapsinjike?

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

## 9. BANJA

*Ma ubale ofunikira kwambiri pa moyo wathu amapezeka mu banja lathu. Mulungu anapereka maudindo osiyanasiyana kwa abambo komanso amai monga mwa udindo wawo ngati abambo okwatira, amai okwatiwa, atate komanso amayi. Kukwaniritsa malamulo a Mulungu molingana ndi udindo wanu m'banja zimapangitsa inu kuti mubweretse ulemelero kwa Mulungu poyesetsa kukhala monga mwa chimene Mulungu amachikamba kuti munthu akhale mbali imodzi ya banja la uzimu la Mulungu. Inu mukulimbikitsidwa kuti muyang'ane kwambiri mitu yokhayo ya phunziro iri amene akukhudza inuyo.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*UDINDO*

**Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri**

*Kodi maudindo anu mb'anja molingana ndi baibulo ndi otani?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kuphunzitsa za m'mene inu mukhonza kugwiritsira ntchito udindo wosiyanasiyana wa ubale m'banja.*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri**

*Mulungu amagwiritsa ntchito udindo wanu m'banja ngati chionetsero choonetsa kuti zikutanthauza chiyani kukhala m'banja lake la uzimu la Mulungu.*

**NDIME ZA PAMTIMA:**

*"Momwensho amuna inu, khalani nao monga mwa cidziwitso, ndi kucitira mkazi ulemu, monga cotengera cocepa mphamvu, monganso wolowa nyumba pamodzi wa cisomo ca moyo, kuti mapemphero anu angaletsedw." – 1 Petro 3:7*

*"Akazi inu, mverani amuna anu a inu eni, monga kumvera Ambuye. Pakuti mwamuna ndiye mutu wa mkazi, monganso Khristu ndiye mutu wa Eklesia, ali yekha Mpulumutsi wathupilo. Komatu monga Eklesia amvera Khristu, koteronso akazi amvere amuna ao m'zinthu zonse." – Aefeso 5:22-24*

# KUFUNIKIRA KWA BANJA

---

## T. Chinthu choyambirira chimene Mulungu anachikhazikitsa padziko pano ndicho banja.

Mulungu anafotokoza bwino za ukwati momveka bwino kuchokera pachiyambi. Ukwati ndi umodzi wa mamuna m’modzi ndi mkazi m’modzi kwa muyaya.

*Geneses 1:26-28; 2:18, 21-24*

## U. Mulungu akukamba momveka bwino kuti banja ndi lofunikira kwambiri pa utumiki.

Munthu asanatsogolere mpingo, ayambe waonetsa kuti akhonza kutsogolera nyumba yake.

*1Timoteo 3:4-5*

## V. Mulungu amagwiritsa banja monga chionetsero choonetsa kuti zikutanthauza chiyani kukhala m’banja lake.

1. **BANJA** – thupi la Khristu limatchulidwa kuti “banja” la Mulungu

*Aefeso 3:14-15*

2. **MWAMUNA**– Munapalitsidwa ubwenzi kwa Khristu monga “mwamuna m’modzi”.

*2 Akorinto 11:2*

3. **MKAZI**– Thupi la Khristu limatchedwa “mkazi wa Mwanawankhosa.”

*Cibvumbulutso 19:7*

4. **ATATE** – Mulungu amakhumba kuti inu mudzimufikira ngati “ATATE.”

*Luka 11:1-2*

5. **MZIMAI/MLEZI** – Inu muyenera kutumikira ena mwa uzimu monga mlezi afukata ndi kutumikira ana ace kuthupi.

*1 Atesalonika 2:7-8*

6. **ANA** – Mulungu amakhumba kukufanizirani inu ndi “ana ake amuna komans akazi”.

*2 Akorinto 6:17-18*

## **MFUNDO YOFUNIKIRA MU PHUNZIRO IRI!**

Mulungu amagwiritsa ntchito udindo wanu m’banja monga chionetsero poonetsa kuti zikutanthauza chiyani kukhala m’banja lake lauzimu. Komabe okhulupirira ambiri anaononga maanja awo ndipo chimakhala chinthu chovuta kuti amvetsetse zakukhala m’banja la Mulungu. Pamene mukura ndi kumvetsetsa za banja la Mulungu, udindo wanu m’banja lanu ukuyenera kukuthandizani kukhala ochitira umboni wa Yesu Khristu mwa mphamvu.

## **UDINDO WA MWAMUNA MONGA MWA BAIBULO**

### **A. Mwamuna AKONDE mkazi wake.**

#### **1. Chikondi chopereka**

Mwamuna akuyenera kukhala patsogolo kudziwa bwino lomwe zofuna zamkazi wake, ndipo iye asankhe kudzipereka kuti zinthu zimenezo azikwaniritse.

***Aefeso 5:23-25***

#### **2. Chikondi choyeretsa**

Amaika mau a Mulungu mwa mkazi wake ndi kumutsogolera kuti asatengeke ndi zakale koma kumuthandiza kumvetsa za zinthu za muyaya mwa Ambuye.

***Aefeso 5:26-27***

#### **3. Chikondi chochitachita**

Amakonda mkazi wake monga thupi lake lomwe, chifukwa limaonetsa za m’mene Khristu amakondera thupi lake, limene liri mpingo.

***Aefeso 5:28-30***

#### **4. Chikondi chokhazikika**

Mulungu anapanga kuti umodzi wa ukwati kuti awiri akhale m’modzi. Ndi umodzi umene sungapasuke.

***Aefeso 5:31-33***

### **B. Mwamuna ayenera KUPEREKA zosowa kwa mkazi wake.**

Mulungu wapereka kwa mwamuna udindo opereka zosowa ku banja lake. Izi zimapangitsa mkazi kuti ateteze komanso kutsogolera zinthu zonse bwino opanda chosokoneza.

*“Koma ngati wina sadzisungiratu nyumba yace ya iye yekha, makamaka iwo a m’banja lace, wakana cikhulupiriro iye yekha, ndipo aipa koposa wosakhulupirira.” – 1Timoteo 5:8*

*“chifukwa cace nditi akwatiwe amasiye, ang’ono, nabale ana, naweruze nyumba.....”*

**– 1Timoteo 5:14**

### **C. Mwamuna ayenera KUTETEZA mkazi wake.**

Ndi udindo wa mwamuna kuteteza banja lake ku zinthu za uzimu komanso zathupi zimene zingaononge banja. Ndi zofunikira kwambiri kuti mwamuna akhale wolimba mwa Ambuye, komanso mtsogoleri pa za uzimu kwa iwo amene ayenera kumvera ulamuliro wake.

*“...kapena akhonza bwanji munthu kulowa m’banja, ndikufunkha akatundu ace, ngati iye sayamba kumanga munthu wolimbayo? Ndipo pamenepo adzafunkha za banja lace.” – Mateyu 12:29*

### **D. Mwamuna wayenera KUPHUNZITSA mkazi wake**

Ngati mkazi ali ndi mafunso a baibulo komanso a uzimu, ayenera kupeza mayankho kudzera pa kukhala ndi nthawi ndi Mulungu m’mau ake. Ngati ali ndi mafunso ena, Mulungu anakonza kuti mkazi akhonza kufunsa mwamuna wake. Ndi udindo wake kuti awerenge mau a Mulungu kuti akhale okonzeka kupereka mayankho.

*“Akazi akhale chete m’Mipingo. Pakuti sikuloledwa kwa iwo kulankhula. Koma akhale omvera, monganso chilamulo chinena. Koma ngati afuna kuphunzira kanthu afunse amuna ao a iwo okha kwao; pakuti kunyazitsa mkazi kulankhula mu mpingo.” – 1 Akorinto 14:34-35*

### **E. Mwamuna ayenera KUKHALA ndi mkazi wake**

Pamene mwamuna akhala limodzi ndi mkazi wake, amapereka chitetezo chimene amachifuna. Muphunzira za m’mene mungaperekere chitetezo kwa mkazi wanu pophunzira za m’mene Yesu amaperekera chitetezo kwa mkwatibwi, mpingo.

*“Momwemonso amuna inu khalani nao...” – 1 Petro 3:7*

#### **1. Yesu anapereka kwa mkwatibwi chikondi chosatha.**

Mkazi wanu amafuna kudziwa mumtima mwawo kuti palibe chimene chingawalekanitse iwo ndi chikondi chanu.

***Aroma 8:35-39***

#### **2. Yesu anapereka kwa mkwatibwi chikhulupiriro chosatha.**

Mkazi wanu amafuna kudziwa mumtima mwake kuti palibe amene angakupangitseni inu kukhala osakhulupirika kwa iwo.

***2 Atesalonika 3:3***

#### **3. Yesu amakakhala tcheru kumvetsera kwa mkwatibwi**

Mkazi wanu amafuna kudziwa mumtima mwawo kuti inu mumasamala pomvera zimene amanena.

***1 Yohane 5:14***

**4. Yesu amakhala ndi malingaliro abwino kwa mkwatibwi**

Mkazi wanu amafuna kudziwa mumtima mwake kuti akhonza kukukhulupirani kuti nthawi zonse mumakhala ndi malingaliro abwino pa mtima panu a iye.

*Aroma 8:28*

**5. Yesu amapereka kwa mkwatibwi wake chitsimikizo choti sangabwezere moopseza.**

Mkazi wanu amafuna kudziwa mumtima mwake kuti sakuyenera kuopa mkwiyo wanu kapena mau ena aliwonse amtsutso.

*Aroma 8:1*

**6. Yesu akupereka kwa mkwatibwi kuti chitsimikizo kuti sadzamusiya.**

Mkazi wanu amayenera kudziwa mumtima mwake kuti sakuyenera kukumana ndi mavuto m'moyo mwake chifukwa inuyo popanda inu.

*Ahebri 13:5*

**7. Yesu akupereka kwa mkwatibwi chithandizo komanso kukhudzika naye.**

Mkazi wanu akuyenera kudziwa mumtima mwake kuti inu mudzasamalitsa kumva ndikuchita monga m'mene akumvera iyenso.

*Ahebri 4:15-16*

**F. Mwamuna amayenera KUMUDZIWA mkazi wake**

Akazi onse ali ndi zosowa zofanana; komabe akazi onse ndi osiyana. Ndi udindo wa mwamuna kuti aphunzire mkazi wake kuti adziwe chomwe chimamupangitsa kuti amve kukondedwa.

*“Momwemonso amuna inu khalani nao, monga mwa cidziwitso...” – 1 Petro 3:7*

**1. Mkazi wanu amafuna chikondi chanu.**

Iye amafuna mwamuna amene akhonza kufa chifukwa cha iye.

**2. Mkazi wanu amafuna chitetezo chanu.**

Iye amafuna mwamuna amene ali ofuna kupereka zosowa zake.

**3. Mkazi wanu amafuna nthawi yanu yoti mukhale limodzi pa chiyanjano**

Iye amafuna mwamuna amene ali ofuna kumumvera iye.

**G. Mwamuna ayenera KULEMEKEZA mkazi wake**

Inu muyenera kumuika mkazi wanu pa mtengo wapamwamba chifukwa ndi munthu wa mtengo wapatali kwa inu, komanso chifukwa cha ubale umene mumagawana limodzi.

*“...ndi kucitira mkazi ulemu, monga cotengera cocepa mphamvu, monganso wolowa nyumba pamodzi wa cisomo ca moyo;” – 1 Petro 3:7*

### **MFUNDO YOFUNIKIRA KUDZIWA:**

Ngati mwamuna alephera kukwanitsa udindo wake pa mkazi wake monga mwa baibulo, mapemphero ake akhonza kutchingidwa!

*"...kuti mapemphero anu angaletsedwe!" – 1 Petro 3:7*

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi mkazi wanu amadziwa kuti inu mumadzipereka kuti mumuteteze kuthupi komanso kuuzimu?

Kodi inu mukupanga chiyani kuti muonetsetse kuti mkazi wanu akumva kukondedwa?

Kodi mkazi wanu amabwera kwa inu kufuna mayankho pa mafunso a uzimu komanso a baibulo?

Kodi ubale wanu ndi Mulungu ukukhudza bwanji ubale wanu ndi mkazi wanu?

## **UDINDO WA MKAZI MONGA MWA BAIBULO**

---

### **A. Mkazi wabwino amayenera kukhala MZAKE wa mwamuna wake.**

Mulungu anapereka kwa mwamuna mzake kuti akhale waphumphu, chifukwa si kwabwino kuti mwamuna akhale yekha.

*"Yehova Mulungu ndipo anati, si kwabwino kuti munthu akhale yekha; ndidzamupangira womuthangatira iye." – Genesesi 2:18*

1. Mwamuna wanu amafuna ubale woti mudzikhonza kugawana limodzi chimwemwe komanso zovuta. Inu mukhonza kulimbikitsa mwamuna wanu pamene mukhala mzake wabwino kwambiri.

***Nyimbo ya Solomo 5:16***

2. Mwamuna amafuna inu mukhale mzake weniweni amene mukhonza kugawana naye chikondi. Inu mudzakwaniritsa izi ngati mukhala wokondedwa wake.

***Genesesi 2:24-25; 1 Akorinto 7:1-5***



## **B. Mkazi ayenera KUTHANDIZA mwamuna wake.**

Mulungu anapanga dongosolo kuti mkazi apereke zimene mwamuna wake amasisowa kuti akwaniritse cholinga cha Mulungu cha moyo. Inu mukhonza kukhala chinachirichonse chimene Mulungu akufuna kuti mukhale pothandizira mwamuna wanu kukhala chimene Mulungu akufuna kuti akhale.

*“Yehova Mulungu ndipo anati, Si kwabwino kuti munthu akhale yekha; ndidzampangira womthangatira iye.” –Genesis 2:18*

## **C. Mkazi ayenera KUPEREKA ulemu kwa mwamuna wake.**

Mulungu anakamba momveka bwino kuti akazi ayenera kukonedwa posatengera nyengo, ndipo amuna ayenera kulemekezedwa posatengera nyengo. Kapena mwina zikhonza kukhala zinthu zovuta kuonetsa ulemu pamene inu simukukonedwa, ndi chofunikira kumvetsetsa kuti iri silamulo chabe kuti munthu adzimva mkati mwake kukonedwa, koma ndi lamulo loti munthu aonetese khalidwe la ulemu.

*“Komanso inu, yense pa yekha, yense akonde mkazi wake wa iye yekha, monga adzikonda yekha, ndipo mkaziyo akumbukile kuti aziopa mwamuna.” – Aefeso 5:33*

### **TSATANI CHITSANZO CHA SARAI:**

Udindo wa mkazi pa kudzipereka kwa mwamuna wake sikumatengera kuti kodi mwamuna akukwaniritse udindo wake kapena ayi. Inu muyenera kusankha kuti mukhale odzipereka kwa kwa mwamuna wanu ngakhale iyeyo sakutumikira Ambuye. Mwamuna wosamvera ayenera kumva ndi kuona ulemu wanu wosasintha wa pa Mulungu, ndi ulemu wosasinthanso kwa mwamuna wake. Ikani chidwi chanu chonse kuti mukondweretse Mulungu ndi mtima wanu.

**1 Petro 3:1-6**

## KODI TANTHUZO LA BAIBULO LA KUMVERA NDI LOTANI?

Kumvera kukunthauza kuti kudziika wekha pamalo poti wina akulamulire. Mulungu wapereka udindo kwa mwamuna kuti akhale mtsogoleri wachikondi kwa mkazi wake, ndipo mkazi wake wapatsidwa udindo wodziika yekha pansa pa ulamuliro wa mwamuna wake. Akazi ali ofanana ndithu ndi amuna awo; komabe, Mulungu anapereka kwa yense maudindo osiyanasiyana mkati mwa banja. Pamene mkazi adziika yekha pa utsogoleri wa mwamuna wake, sizikutanthauza kuti iye ali ndi udindo wochepa m'mbanja. Izi zikungatanthauza kuti iye ali ndi udindo wosiyana.

*“koma ndifuna kuti mudziwe, kuti mutu wa munthu ndiye Khristu, ndi mutu wa mkazi ndiye mwamuna; ndipo mutu Khristu ndiye Mulungu... Pakuti mwamuna sakhala wa kwa mwamuna, koma mkazi wa kwa mwamuna; pakutinso mwamuna sanalengedwa cifukwa ca mkazi.” – 1 Akorinto 11:3, 8-9*

- 1. Mkazi ayenera KUMVERA kwa mwamuna wake monga ayenera kutero kwa Khristu.**  
Mulungu akulankhura momveka bwino kuti mkazi ayenera kumvera mwamuna wake monganso m'mene amvera Khristu. Inu muyenera kudziika nokha pa ulamuliro wa Khristu musanadzipange kukhala pa ulamuliro wa mwamuna wanu. Ndi zinthu zosatheka kuti mkazi adzipereke kwa Ambuye Yesu Khristu koma ndikukhala osamvera mwamuna wake.

*“Akazi inu, mverani amuna anu a inu eni, monga kumvera Ambuye” – Aefeso 5:22*

- 2. Mkazi ayenera KUMVERA mwamuna wake monga mpingo umvera Khristu.**  
Kumvera kwa mpingo kwa Khristu si chinthu chimene chiri chokakamiza kapena kulamulidwa kuti tichite. Koma ndi chinthu cha ulemu ndi chamwayi kuti ife tikhonza kumumvera lye. Monga mpingo umasankha kumvera ulamuliro wa Mulungu mu zonse, akazi nwonso ayenera kusankha kumvera zonse pa ulamuliro wa amuna awo.

*“komatu monga Ekklesia amvera Khristu, koteronso akazi amvere amuna ao m'zinthu zonse.” – Aefeso 5:24*

- 3. Mkazi ayenera KUMVERA mwamuna wake monga kuyenera mwa Ambuye.**  
Njira yokhayo imene anthu akhoza kukakhala thupi limodzi ndi pamene onse akhala molingana ndi cholinga cha Mulungu. Mkazi kukwaniritsa za udindo wake monga mwa Baibulo, pa kumvera mwamuna wake, ndi njira yokhayo yokwaniritsa umodzi umene Mulungu anaukonza kuti ukhalepo m'banja.

*“Akazi inu, muzimvera amuna anu, monga kuyenera mwa Ambuye.”  
– Akolose 3:18*

## ZOKAMBIRANA

Kodi mukuthandiza motani amuna kukwaniritsa cholinga cha Mulungu pa moyo wao?

Kodi ndi akazi ena ati amene mumayang'ana ngati zitsanzo zoti muzitsatire pa banjalanu?

Kodi mukumvera utsogoleri wa mwamuna wanu?

# **UDINDO WA KHOLO MOLINGANA NDI BAIBULO**

Baibulo likukamba momveka bwino kuti udindo ophunzitsa ana waperekedwa kwa atate. Komabe, pali nyumba zambiri lero zimene atate akulephera ntchito yao. Mfundo izi ndizoonza mwa azimai pakuti nawonso ndi oyang'anira amene ali ndi udindo m'malo mwa atate.

## **A. Makolo ayenera KUTETEZA ana awo.**

Ndi chinthu chofunikira kuti makolo akhale olimba mwa Ambuye, ndi kukhala atsogoleri a za uzimu kwa ana awo.

*"...kapena akhonza bwanji munthu kulowa m'banja, ndikufunkha akatundu ace, ngati iye sayamba kumanga munthu wolimbayo? Ndipo pamenepo adzafunkha za banja lace." – Mateyu 12:29*

## **B. Makolo ayenera KUPHUNZITSA ana awo.**

Mulungu anakonza kuti makolo akhale anthu amene akhonza kuphunzitsa ana awo mau a Mulungu kuti akadziwe njira ya chipulumutso. Iye akufunanso kuti makolo akhonze kuphunzitsa ana awo mau a Mulungu ndicholinga choti akhale ndi moyo wa chipambano mwa Khristu.

*"Ndipo mau awa ndikuuzani lero, azikhala pamtima panu; ndipo muziwaphunzitsa mwacangu kwa ana anu, ndi kuwalankhula awa pokhala pansu m'nyumba zanu, ndi poyenda inu panjira, ndi pogona inu pansu, ndi pouka inu." – Deuteronomo 6:6-7*

## **C. Makolo ayenera KUTSOGOLERA ana awo.**

Makolo akhonza kukhala zitsanzo zabwino za m'mene anthu angathe kuchitira molingana ndi choonadi cha mau a Mulungu pamene aika mauwo mumtima mwao. Makolo sayenera kungophunzitsa kokha ndi pakamwa, koma ayeneranso kutsogolera ana awo powaphunzitsa za moyo wawo monga mwa mau a Mulungu.

*"Cifukwa cace mudzisunga mau anga awa mumtima mwanu ndi m'moyo mwanu; ndi kuwamanga ngati cizindikilo pamanja panu; ndipo zikhale zapamphumi pakati pa maso anu; ndipo muziwaphunzitsa ana anu..." – Deuteronomo 11:18-19*

## **D. Makolo ayenera KUDANDAULIRA ana awo**

Makolo amadandaulira ana awo pokhala ndi nthawi limodzi. Ana amayenera kudziwa kuti makolo ayenera kukhala nawo limodzi nthawi zonse. Ndi chinthu chofunikira kuti makolo akhale alipo nthawi zonse.

*"Monga mudziwa kuti tinacitira yense wa inu pa yekha, monga atate acitira ana ace a iye yekha, tikudandaulirani," – 1 Atesalonika 2:11*

## **E. Makolo ayenera KULIMBIKITSA ana awo.**

Ana amalimbikitsidwa pamene makolo awo akhala nawo limodzi ndi kuwapatsa mau a chilimbikitso ndi achitonhozo. Ndi chinthu chabwino kuti makolo alankhule mau a chilimbikitso kwa ana awo.

*“Monga mudziwa kuti tinacitira yense wa inu pa yekha, monga atate acitira ana ace a iye yekha, tikudandaulirani,” – 1 Atesalonika 2:11*

## **F. Makolo ayenera kukhala osamala KUTI ASAKWIYITSE ana awo.**

Ana amabadwa mu m’dzi ndi chilakolako chofuna kupereka ulemu kwa atate. Pamene atate atenga udido bwino wawo molingana ndi Baibulo, akhonza kukhala ndi zotsatira zabwino pakusinthika kwa ana ake. Komabe, ngati akana udindo wake, iyenso ali ndi mphamvu zoononga ana ake ndipo izi zikhonza kukhudza anawo moyo wawo wonse.

1. Makolo ali ndi mphamvu yopanga ana anu kuti akhale OUKIRA.

*“Ndipo atate inu, musakwiyitse ana anu; komatu muwalere iwo m’maleredwe ndi cilangizo ca Ambuye.” – Aefeso 6:4*

2. Atate ali ndi mphamvu yopangitsa ana kuti akhale OTAYA MTIMA

*“Atate inu, musamaputa ana kuti angataye mtima.” – Akolose 3:21*

## **G. Makolo ayenera KUPELEKA MALANGIZO kwa ana awo.**

Mulungu wapereka kwa makolo udindo woperereka malangizo kwa ana. Koma mwatsoka, pali makolo ambiri amene amanyalanyaza udindowu.

*“Komanso, tinali nawo atate a thupi lathu akutilanga, ndipo tinawalemekez; kodi sitidzagonjera Atate wa mizimu koposa nanga, ndi kukhala ndi moyo? Pakutitu iwo anatilanga, masiku owerengeka monga kudawakomera; koma iye atero, kukapindulitsa; kuti tikalandire nawo ciyero cace.” – Ahebri 12:9-10*

### **3. Mwana wosalangidwa akhonza kukula ndi:**

- a. CISONI pa atate ake

*“Wobala citsiru adzicititsa cisoni; ndipo atate wa wopusa sakondwa.” – Miyambo 17:21*

- b. KUMVETSA AMAKE CHISONI

*“Mwana wanzeru akondweretsa atate koma opusa amvetsa amake cisoni.” – Miyambo 10:1*

- c. Kubweretsa CISONI ndi ZOWAWA kwa atate ndi amai

*“Mwana wopusa acititsa atate ace cisoni, namvetsa zowawa amace ombala.” – Miyambo 17:25*

- d. KUDANDAULA pa Yehova

*“Utsiru wa munthu ukhotetsa njira yace; Mtima wace udandaulira pa Yehova.” – Miyambo 19:3*

e. A KUCHITITSA MANYAZI ndi KUGWETSA NKHOPE kwa atate ndi amai  
*“Wolanda za atate ndi wopitikitsa amai, Ndiye mwana wocitititsa manyazi ndi wogwetsa nkhope.” – Miyambo 19:26*

f. Ndikukhala OKUBA za atate ndi amai ake

*“Wobera atate wace, pena amace, nati, Palibe kulakwa; Ndiye mnzace wa munthu wopasula.” – Miyambo 28:24*

#### 4. Maganizo asanu ndi awiri okamba m'mene tingachitire popereka chilango:

- a. Osalora kuti ana anu anene kuti *“ayi.”* Kumbukirani, kuti ana ayenera kuphunzira kudzipereka ku ulamuliro wa Mulungu pomvera ulamuliro wanu.
- b. Nthawi zonse siyanitsani pakati pa chibwana chabe cha mwana ndi kuukira.
- c. Musadikire kuti mulange ana anu pamene mukhonza kutero mwa mkwiyo wanu.
- d. Nthawi zonse langani nthawi yomwe mwana wachita kusamvera.
- e. Nthawi zonse langani maonedwe a zinthu komanso ngakhalenso zimene mwana wachita.
- f. Nthawi zonse yamikirani pamene mwana wanu wachita chinthu chabwino.
- g. Nthawi zonse nenani kwa ana anu kuti *“ndinalakwitsa, kodi ukhonza kundikhululukira?”*

#### **ZOKAMBIRANA:**

Mungafotokoze bwanji za ubale wanu ndi ana anu?

Kodi zimene mumachita zimagwirizana ndi choonadi cha mau a Mulungu pamene mukuphunzitsa ana anu?

Kodi ana anu mumawalanga bwanji?

Kodi ndi udindo uti mwa maudindo amene baibulo lafotokoza umene mukumukhulupirira nawo Mulungu kuti akulitse mwa inu?

# KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA

**38.Molingana ndi *1 Timoteo 3:4-5*, kodi ndi chifukwa chiyani banja iri yofunikira pa utumiki?**

---

---

---

**39.Kodi ndi maudindo asanu ndi awiri ati amene bambo wa pabanja akhonza kukhala nawo monga ndi baibulo?**

- a. \_\_\_\_\_
- b. \_\_\_\_\_
- c. \_\_\_\_\_
- d. \_\_\_\_\_
- e. \_\_\_\_\_
- f. \_\_\_\_\_
- g. \_\_\_\_\_

**40.Fotokozani mwa mau anu chimene kumvera kukutanthauza monga mwa baibulo?**

---

---

---

---

---

**41.Tchulani maudindo anai a kholo.**

- a. \_\_\_\_\_
- b. \_\_\_\_\_
- c. \_\_\_\_\_
- d. \_\_\_\_\_

**42.Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?**

---

---

---

---

---

## KUPHUNZIRA ZA BAIBULO PAWEKHA

Werengani *Geneses 20:1-13*. Kodi ndi maudindo angati a mwamuna amene mukhonza kutchula amene Abrahamu anaphwanya kwa mkazi wake Sara kuchokera mu ndime imeneyi.

---

---

---

---

Werengani *Geneses 34*. Kodi Yakobo anachita chiyani pamene anadziwa kuti munthu wina wotchedwa Sekemu wamui pitsa Dina? Kodi Yakobo anakwaniritsa udindo wake ngati kholo kwa ana ake molingana ndi baibulo? Kodi mukuganiza kuti Yakobo akanachita bwanji mosiyana?

---

---

---

---

Werengani Yobu 1-2. Ndime imeneyi ikukamba za mtumiki wa Mulungu Yobu amene anazuzika kuthupi ndi Satana. Mkatikati mwakumva zowawa ndi chisoni, kodi mkazi wake anamuthandiza motani?

---

---

---

---

Werengani Machitdwe 18:1-4; 18:18-28; ndi Aroma 16:3-5. Mtumwi Paulo angwira ntchito limodzi ndi Akula komanso Priska mu utumiki wake wonse mu mizinda yosiyanasiyana komanso m'maiko osiyanasiyana. Kodi nyumba ya Akura ndi Priska inali yofunikira bwanji pa utumiki? Kodi inu mukuigwiritsa ntchito motani nyumba yanu ku utumiki?

---

---

---

---

---



## **10. KULIMBANA NDI TCHIMO**

*Mwinatu chinthu chovuta chachikuru kwa okhulupirira ndi nkhondo yolimbana ndi tchimo. Choonadi ichi sichimakhala choonekeratu kwa a khristu a ang'ono, koma pamene ukura mwa Khristu, udzazindikira kukula kwa kolimbana uku.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*KUGONJETA*

**Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Kodi ndingagonjetse bwanji tchimo m'moyo mwanga?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kukuthandizani kuti muphunzire kugonjetsa chikhalidwe chanu cha uchimo, ndi kuyenda mwa Mzimu wa Mulungu monga afunira.*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Ngati muli ndichisoni chenicheni cha uMulungu chokhudza tchimo lanu, kulapa kudzachitika mosavuta.*

**NDIME ZA PAMTIMA:**

*"Cotero inunso, mudziwerengere, inu nokha ofafa ku ucimo, koma amoyo kwa Mulungu mwa Khristu Yesu" – Aroma 6:11*

*"Ndiwabisa mau anu mumtima mwanga kuti ndisacimwire Inu"- Masalmo 119:11*

## **KUMVETSETSA ZA KHALIDWE LA TCHIMO**

---

Tchimo ndi nkhani yaikuru kuposa m'mene anthu amaganizira. Ndi zoposera zolakwika zimene munthu wazichita chifukwa zimakhudza chikhalidwe chathu chokugwa. Kuti ife tigonjetse tchimo, ndikofunikira kudziwa kuti Mulungu walankhura momveka bwino m'mau ake zokhudza chimene tchimo liri.

### **W. Ndi tchimo kukhala ndi mtima wodzikweza.**

*Miyambo 21:4*

### **X. Ndi tchimo kukhala m'moyo wosakhulupirira.**

*Aroma 14:23*

### **Y. Ndi tchimo kuchita zosemphana ndi zimene mukudziwa kuti ndi zolondora.**

*Yakobo 4:17*

### **Z. Ndi tchimo kuphwanya lamulo la Mulungu.**

*1 Yohane 3:4*

### **AA. Ndi tchimo kulora chisalungamo china chirichonse m'moyo mwanu.**

*1 Yohane 5:17*

#### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi Mulungu anagwiritsa ntchito imodzi mwa ndime zimenezi kuvumbulutsa za tchimo m'moyo mwanu?

Kodi kuthana ndi tchimo ndikofunikira m'moyo mwanu?

## **KUMVETSETSA CHIFUKWA CHANI MUMACHIMWA**

---

### **Q. Inu mumachimwa chifukwa munatenga chikhalidwe cha uchimo kuchokera kwa Adamu.**

Monga okhulupirira, tchimo lidzapitirira kukhala nkhani pa moyo wathu, chifukwa inu simunataye chikhalidwe chanu cha thupi pa nthawi yakubadwanso mwa uzimu. Tsopano muli ndi chikhalidwe chanu chakale komanso chatsopano.

**R. Inu mumachimwa chifukwa chikhalidwe chanu chakale chimakukorani ku uchimo.**

Zikhalidwe zonse zilipo mwa inu pa nthawi imodzi. Nkhani kwa okhulupirira wina aliyense ndiyosankha kutumikira chikhalidwe chimene akufuna. Chikhalidwe chimene mumachisamala kwambiri ndi chimene chidzalamulire moyo wanu.

***Yakobo 1:13-15; Aroma 7:14-25***

**S. Inu mumachimwa chifukwa cha zotsatira zitatu za uchimo.**

*“Pakuti chiri chonse cha m’dziko lapansi, cilakolako ca thupi, cilakolako ca maso, matamandidwe a moyo, sizicokera kwa Atate, koma ku dziko lapansi.” – 1 Yohane 2:16*

1. **Cilakolako ca thupi** – mayesero ofuna kukwaniritsa zokhumba za thupi.
2. **Cilakolako ca maso** – mayesero omupangitsa munthu kusilira
3. **Matamandidwe a moyo** – yesero lopangitsa muthu kuti ayambe kudzitamandira

**Izi ndi zitsanzo zazikuru ziwiri m’baibulo zokhudza mayesero:**

**1. Yesero la Adamu ndi Hava m’manda muja – Geneses 3:1-6**

- **Cilakolako ca thupi** – Hava anaona kuti mtengo unali wabwino kudya
- **Cilakolako ca maso** – Hava anaona kuti mtengo unali wopatsa chidwi m’maso
- **Matamandidwe a moyo** – Hava anaona kuti mtengo unali wabwino omupanga munthu kukhala wa nzeru

**2. Yesero la Yesu mu chipululu– Mateyu 4:1-13**

- **Cilakolako ca thupi** – Yesu anayesedwa kuti asandutse miyala kukhala mkate.
- **Cilakolako ca maso** – Yesu anaonetsedwa ndi kupatsidwa ma ufumu a dziko lapansi a nthawi imeneyo
- **Matamandidwe a moyo** – Yesu anayesedwa kuti aonetse kuti iye anali mwana wa Mulungu polumpha pa mwamba pa kacisi.

**MFUNDO YOFUNIKIRA KUDZIWA:**

Yesu anakumana ndi mayesero monga ifenso timakumana nawo, koma sanachimwe. Yesu anawagonjetsa pogwiritsa ntchito malemba. Pamene sitingathe kukhaliratu opanda tchimo, tikhonza kuphunzira kugonjetsa mayesero m’moyo mwathu poima pa ulamuliro wa mau a Mulungu.

# **KUMVETSETSA M'MENE MULUNGU AMAONERA TCHIMO LANU**

---

Ndi zofunikira kudziwa kuti tchimo ndi chani, komaso kudziwa kuti Mulungu amaliona bwanji tchimo. Inu muli ake a Mulungu woyera amene anayenera kuthana ndi tchimo kuti inunso mukakhale oyera pamaso pake.

- C. Mulungu anaweruzana tchimo lanu pa Kavali potenga tchimo lanu ndikumupatsa Yesu Khristu.**

*2 Akorinto 5:21*

- D. Mulungu walora kuti mukolore zotsatira za uchimo wanu.**

*Agalatiya 6:7-8*

- E. Pamene mupitilira kukhala m'moyo wa uchimo, Mulungu adzakulangani ngati mwana wake.**

*Ahebri 12:5-11*

## **ZOKAMBIRANA:**

Kodi nkhondo yanu yolimbana ndi thupi komanso Mzimu iri yaikuru motani m'moyo wanu tsopano?

Kodi mukudziwa m'mene inu mukhonza kupezera malemba kuti mukonze vuto la mayesero m'moyo mwanu?

# **KUMVETSETSA ZA M'MENE MUNGACHITIRE POKONZA VUTO LA TCHIMO**

---

- D. Kuvomereza udindo wanu pa tchimo lanu osati kuloza chala anthu ena.**

*Miyambo 28:13*

- E. Weruzani tchimo lanu, osakhala anthu ozemba tchimo kapena kulipezera nzeru zina**

*1 Akorinto 11:31-32*

**F. Sankhani kutumikira Mulungu ndipo mulimbane ndi tchimo limene limapezekapezeka m'moyo mwanu.**

*Ahebri 12:1-2; Afilipi 3:13-15*

**G. Vomerezani machimo anu kwa Mulungu ndipo mukhulupirire kuti IYE akuyeretsani.**

*1 Yohane 1:9; Masalmo 41:4*

**H. Gwiritsani ntchito mau a Mulungu ku moyo wanu kuti akuyeretseni ku machimo anu. 2 Akorinto 7:1; Yohane 15:3; 17:17**

### **MFUNDO YOFUNIKIRA PA PHUNZIRO IRI!**

Lapani pakutembenuka ku machimo anu ndikufunitsitsa chiyero. Ngati inu muli ndi cisoni chenicheni cha pa Mulungu pa tchimo lanu, kulapa kudzatsatira mosavuta. Musabwererenso ku tchimo lanu, koma pempherani kwa Mulungu kuti kupatseni mtima odana nalo.

*Aroma 6:1-2; 2 Akorinto 7:10-11; Miyambo 8:13*

## **KUMVETSETSA ZA M'MENE MUNGAGONJETSERE TCHIMO**

Inu simungagonjetse tchimo m'moyo mwanu kufikira mutaliona mofanana ndi m'mene Mulungu amalionera tchimolo. Pokhapo ndi pamene mukhonza kuyamba kuchotsa tchimo m'moyo wanu kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera komanso mau a Mulungu.

**A. Vomerezani ndi Mulungu kuti tchimo lilibe ulamuliro pa inu.**

*Aroma 6:6-13*

**B. Musapereke thupi lanu ku mayesero oti mukhonza kugwa nawo mu uchimo.**

*Aroma 13:14*

**C. Musalore malingaliro a uchimo kulamulira malingaliro anu.**

*2 Akorinto 10:3-5*

**Mulungu wakukonzekeretsani inu ndi zipangizo zoti mugonjetse nazo tchimo m'moyo mwanu.**

**1. Mau a Mulungu adzakutsogolerani kuti mugonjetse tchimo.**

a. Mulungu wapanga njira yoti inu muthawire mayaesero onse a ku uchimo.  
**1 Akorinto 10:13**

b. Njira imodzi yoti tithawire ndi kuloweza mau a Mulungu.

**Masalmo 37:31; Masalmo 119:9-11**

c. Yesu Khristu anapereka chitsanzo kwa inu kuti mudzigwiritsa ntchito malemba pamene muyesedwa ku machimo.

**2. Mzimu wa Mulungu adzakutsogolerani kuti mugonjetse machimo.**

a. Inu ndinu a amfulu ndipo mukhonza kusankha chilungamo chifukwa Mzimu wa Mulungu akhala mwa inu.

**Aroma 8:1-9**

b. Chilakolako cha thupi chiribe mphamvu pa inu, pamene mwasankha kukhala m'moyo wanu mu mphamvu ya Mzimu wa Mulungu.

**Agalatiya 5:16-25**

## **MAFUNSO ENA AMENE INU MUKHONZA KUFUNSA**

**L. Kodi ine ndingapewe bwanji machitachita a dziko la uchimo kuti asandikhudze ine?**

Khalani osiyana ndi njira zonse za dziko lapansi pamene mukutsata Ambuye Yesu Khristu. Pamene mukuumba ma ubale ndi anthu ena otaika kuti abwere kwa Yesu, thawani china chirichonse chimene chingakupangitseni kukhala mu uchimo ndi iwowo. Ngati choling chanu chiri choti anthu otaika abwere kwa Yesu Khristu kudzera mu uthenga wabwino, inuyo mukhonza kukopekansa ndi uchimo wawo.

**Aefeso 5:5-12; 2 Akorinto 6:14-18**

## M. Kodi Mulungu adzatitsogolera bwanji kuti tilimbane ndi tchimo m'moyo wanga?

Mzimu Woyera wa Mulungu adzatsutsa za machimo m'moyo mwanu

***Yohane 16:7-11; Masalmo 139:23-24***

Chikumbu mtima chanu chidzaonetsa njira yabwino kapena yoipa yoti inu mukhalemo. Komabe, ngati mupitirira kukhala mu uchimo ndi kukana kudzudzula kwa Mulungu, chikumbu mtima chanu ndiye kuti chazilira.

***Aroma 2:14-15; 1Timoteo 4:1-2; Tito 1:15***

Pamene muwerenga mau a Mulungu amalankhura ku malingaliro komanso zochita pa moyo wanu.

***Ahebri 4:12-13***

### **Zokambirana:**

Kodi inu mukufuna kupanga zinthu zina kusintha m'moyo mwanu ndi cholinga choti musapereke thupi lanu ku misampha ya uchimo?

Kodi inu mukufuna kudzisiyanitsa nokha ndi anthu ena ake kuti mukhale kutali ndi mayesero amene angabweretse uchimo?

Kodi pali gawo lina ka tchimo limene Mulungu wakupatsani chigonjetso pa moyo wanu?

## **KAUNIUNI NDI ZOKAMBIANA**

---

**12.Mwachidule fotokozani kuti ndi chifukwa chiyani umachimwa ngakhale munapulumsidwa?**

---

---

---

**13.Molingana ndi 1 Yohane 2:15-17, pali magawo atatu okhudza mayesero pa moyo amene mukhonza kugwa nawo mu uchimo. Ndi magawo ati?**

---

---

---

**14.Kodi Mulungu amaona motani tchimo lanu?**

---

---

---

---

**15. Tchulani njira zitatu zogonjetsera tchimo m'moyo mwanu.**

---

---

---

**16. Kodi ndi njira ziti za baibulo zimene zingatithandize kuti tikonze vuto la tchimo?**

---

---

---

---

**6. Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?**

---

---

---

---

---

## **KUPHUNZIRA ZA BAIBULO PAWEKHA**

**Fotokozani mwa mau anu chimene mtumwi Paulo akukufotokozerani mu Aroma 7:14-15.**

---

---

---

---

**Fotokozani za ndondomeko ya tchimo molingana ndi Yakobo 1:13-15.**

---

---



---

---

**Mwa chidule fotokozani malangizo amene akuperekedwa kwa inu mu ndime zimenezi:**

***Aroma 13:14***

---

---

---

***1 Akorinto 11:31-32***

---

---

---

***1Yohane 1:9***

---

---

---

***2 Akorinto 7:1***

---

---

---

## **11. UFULU MWA KHRISTU**

*Chipangano Chatsopano chimanena momveka bwino kuti monga munthu wopulumutsidwa, siuli womangidwa ndi lamulo la Chipangano Chakale, koma uli womangidwa ndi chisomo cha Mulungu. Okhulupilira ena amagwiritisa ntchito chisomo cha Mulungu molakwikwa potenga ufulu ngati kuchita zinthu monga afunira popanda zotsatira. Ena amayesa momwe ubale wao ndi Mulungu ulili potengera momwe amasungira malamulo a makholidwe abwino komanso miyambo ya chipembedzo. Cholinga cha phunziro ndi kukhazikitsa umbuye wa Yesu Khristu monga mfundo ya baibulo yomwe imakuteteza kuti usagwiritse ntchito ufulu wako mwa Yesu molakwika.*

### **Mau ofunikira mu phunziroli:**

*UFULU*

### **Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Popeza kuti ndinakhululukidwa, kodi ufulu wanga ungabweretse bwanji ulemelero kwa Mulungu?*

### **Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kukuthandiza kumvetsetsa kuti ufulu wako mwa Yesu Khristu ndiwotani, ndi momwe ungakondweretsere ndi kubweretsa ulumelero kwa Mulungu mu kuyenda kwako kwa tsiku ndi tsiku ndi lye.*

### **Mfundo yofunika pa phunziroli:**

*Ufulu womwe uli nawo mwa Yesu Khristu umakupatsa iwe kumasuka kuchita zimene zili zoyenera kuchita wosamangidwa ndi lamulo la Chipangano Chakale.*

### **Ndime ya pa mtima:**

*“Pakuti adakuitanani inu, abale, mukhale mfulu; cokhaco musacite nao ufulu wanu cothandizira thupi, komatu mwa cikondi citiranani ukapolo.” – Agalatiya 5:13*

*“Pakuti cilamulo ca mzimu wa moyo mwa Kristu Yesu candimasula ine ku lamulo la ucimo ndi la imfa.”*

*– Aroma 8:2*

## **MULI NDI UFULU KUDZERA KWA YESU KHRISTU**

*“Kristu anatisandutsa mfulu, kuti tikhale mfulu; cifukwa cace cirimikani, musakodwenso ndi gori la ukapolo.” – Agalatia 5:1*

### **MFUNDO YOFUNIKA YA PHUNZIROLI!**

Ufulu womwe uli nawo mwa Yesu Khristu umakupatsa kumasuka kochita zoyenera kuchita wosamangidwa ndi lamulo la Chipangano Chakale. Ufuluwu sichilolezo cha tchimo, kapena wochita zomwe ukufuna, koma umakupatsa kumasuka kutumikira Mulungu kwatunthu ndi kotheratu.

Liu lina la ufulu ndi kuthekera kotsata chifuniro chako. Uli ndi kuthekera kwakusankha pakati pa chifuniro cha Mulungu ndi chifuniro chako. Komabe, chiganizo chili chonse chomwe ungapange chidzakhala ndi zotsatira zamuyaya pa iwe komanso anthu okuzungulira. Ukuyenera kukhala ndi udindo pa ufulu komanso mwayi zimene Mulungu wakupatsa kuti upereke ulemelero kwa iye.

#### **A. Yesu Khristu anakupanga kukhala mfulu kuti umtumikire iye osati tchimo lako.**

Wokhulupilira amene ali womangidwa ndi tchimo sali omasuka kutumikira Mulungu, ndipo wokhulupilira amene ali omangidwa ndi Mulungu sali omasuka kuchimwa.

*Aroma 6:12-13; Aroma 8:1-4*

#### **B. Yesu Khristu anakupanga iwe kukhala womasuka kumtumikira popanda kufunika kosunga malamulo a Chipangano Chakale, kapena malamulo ena ali wonse a chipembedzo**

- C. Yesu Khristu anakupanga kukhala womasuka kuthana ndi zotchinga zili zonse za chikhalidwe ndi chuma kuti akaone anthu akubwera kwa Khristu mu chikhulupiriro.

*1 Akorinto 9:19-22*

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi muli ndi tchimo linalirilonse limene likukulepheretsani kutumikira Mulungu?

Kodi inu munayamba mwakhala mu nyengo imene chipembedzo kapena chilamulo chinakulepheretsani kutumikira Mulungu kapena kwa anthu ena?

Kodi ufulu wanu mwa Khristu wakhudza bwanji za m'mene mumatumikira kwa wina amene ali osiyana pa chikhalidwe kapena kochokera?

## **MULI NDI UFULU WOPANGA ZISANKHO MWA INU NOKHA**

*“Koma Ambuye ndiye Mzimuyo; ndipo pamene pali Mzimu wa Ambuye pali ufulu.” – 2 Corinthians 3:17*

**A. Muli ndi ufulu wosankha chimene ndi chabwino, osati chimene mukufuna.**

1. Ufulu wanu ukupangitseni kusankha kumvera Mulungu.

*Aroma 6:17-23*

2. Ufulu wanu siumakupatsani mwayi kuti mukhutitse uchimo ku thupi lanu.

*Agalatiya 5:13*

3. Ufulu wanu umakulorani kukolora zotsatira za zisankho zanu, kaya ndi zabwino kapena zoipa.

*Agalatiya 6:7-9; Ahebri 12:5-11*

**B. Inu muli ndi ufulu osankha kukhala moyo wanu molingana ndi ufulu umene umapezeka pa choonadi cha Mau a Mulungu.**

*Yohane 8:31-32; Yakobo 1:22-25*

- C. Inu muli ndi ufulu osankha kukhala moyo wanu umene mukhonza kubweretsa ulemelero kwa Mulungu.

*Mateyu 5:16; 2 Timoteo 2:20-21*

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi pali chitsanzo china m'moyo mwanu chimene inu munapanga chisankho chochita chinthu chabwino ngakhale sichinali chenicheni chimene inu mumafuna kuchita?

Kodi zisankho zimene mukupanga m'moyo mwanu lero zimabweretsa bwanji ulemelero kwa Mulungu?

## **UFULU WANU UDZAKHUDZA ANTHU AMENE AKUZUNGULIRANI**

---

- A. Inu simuyenera kuweruza anthu ena amene ali ndi maganizo otsutsana nanu.

*Aroma 14:1-6*

- B. Inu ndinu mboni ya Ambuye Yesu Khristu nthawi zonse, ndipo moyo wanu uyenera kuyesedwa ndi anthu amene akuzungulirani.

*Aroma 14:7*

- C. Inu muyenera kupewa china chirichonse chimene chikhonza kupangitsa m'khristu ofooka kugwa mu chikhulupiriro chawo. Khalani ndi chidziwitso ku zosowa zawo za uzimu.

*Aroma 14:13-15*

- D. Ufulu wanu ukhonza kuoneka olakwika ngakhale zisali choncho. Muyenera kusamalitsa kwambiri kwa inu nokha kuti musaoneke ngati mukuchita choipa.

*Aroma 14:16*

- E. Mulungu anakupatsani ufulu monga njira yoti mutsogolere anthu ena ku chipulumutso mwa Yesu Khristu. Umboni wanu wa Yesu ndiofunikira kwambiri kusiyana ndi zokhumba zanu.

*Aroma 14:17-18*

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu mumadziwa kuti anthu nthawi zonse amaona za m'mene mukukhalira moyo wanu?

Kodi munayamba mwasankha kupewa chinthu china m'moyo mwanu kuti musakhumudwitse okhulupirira wina kapena kuononga umboni wanu kwa anthu otaika?

## **KUDZIWA MALIRE A UFULU**

---

Baibulo likufotokoza momveka bwino za malire amene inu simuyenera kudutsa. Inu simungathe kulungamitsa tchimo ndi kuphwanya kwina kulikonse kwa mau a Mulungu ponena kuti muli ndi ufulu mwa Khristu kuchokera ku chilamulo. Komabe pali zinthu zina, zimene malire athu ku ufulu wathu samakambidwa bwinobwino mu malemba. Mu zinthu ngati zimenezi, ndi chinthu chofunikira kulora Mzimu Woyera kuti atsogolere inu pamene mudzifunsa nokha mafunso achindunji molingana ndi choonadi cha baibulo.

**A. Kodi ine ndikulora ndekha kukhala pansu pa mphamvu ya chinachake chimene sichiyenera kulamulira moyo wanga?**

*1 Akorinto 6:12*

**B. Kodi chimene ndikulora kuchitika pa moyo wanga chimandisendeza chifupi ndi Mulungu, kapena kundichotsa pamaso pake?**

*1 Akorinto 10:23*

**C. Kodi Mulungu alemkekezeka pa izi?**

*1 Akorinto 10:31; Akolose 3:17*

**D. Kodi ndikhonza kukhumudwitsa wina wake pochita chimenechi?**

*1 Akorinto 10:32*

**E. Kodi ganizo limeneri likhonza kupangitsa munthu otaika kukana Yesu monga Mpulumutsi?**

*1 Akorinto 10:33*

**F. Kodi ganizo limeneri likhonza kupangitsa wokhulupirira kugwa pa chipulumutso chake?**

*Aroma 15:1-2*

**G. Kodi ine ndiri ndi kukaikira pa ganizo langa chifukwa chikumbumtima chikunditsutsa?**

*Aroma 14:22-23; Machitidwe 24:16*

**H. Kodi ichi ndi chinthu chimene ndikumva kuti ndichibise kapena kuchichita mwanseri?**

*Aefeso 5:11-13*

**I. Kodi ine ndikhonza kuchita manyazi ngati Ambuye atabwera ndikundipeza ndikuchita zimenezi?**

*1 Atesalonika 5:23*

**J. Kodi uku ndikuyesetsa kuchita zinthu ndi cholinga chofuna kudziwa kuti ndiri pafupi bwanji ndi tchimo ndisadutse malire?**

*1 Petro 2:16*

**K. Kodi pali chabwino chanji pa chinthu chimenechi kuti ndilore chikhale m'moyo mwanga?**

*Afilipi 4:8*

#### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi mafunso amenewa akupangitsani kulingaliranso chinachirichonse pa zinthu zimene pakadali pano mukhonza kulora m'moyo mwanu?

Kodi pali gawo lina lililonse m'moyo mwanu limene simumatsimikiza kuti mudakali mkati mwa malire a ufulu umene Mulungu wakupatsani?

## **UFULU WANU UMAYEZEDWA NDI UMBUYE WA YESU KHRISTU**

Cholinga cha phunziro iri ndi kukhazikitsa umbuye wa Yesu Khristu monga mfundo yofunikira ya baibulo imene imakutetezana kuti musaononge ufulu wanu mwa Yesu. Pofuna kukondweretsa Mulungu, Yesu Khristu wayanera kukhala oposeri Mpulumutsi, Iye wayanera kukhalanso Ambuye

wanu. Umbuye wa Yesu Khristu ndi maziko a moyo wa Chikhristu, komanso zimakwaniritsidwa pamene umutsata mfundo zenizeni za mau a Mulungu.

**A. Kutenga Yesu kukhala mbuye wako ndiko kusankha iye kuti akhale oyamba pa nyengo zonse.**

*“Ndipo iye ali woyamba wa zonse, ndipo zonse zigwirizana pamodzi mwa iye. Ndipo iye ali mutu wa thupi, Eklesiayo; ndiye ciyambi, wobadwa woyamba woturuka mwa akufa; kuti akakhale iye mwa zonse woyambayamba.” – Akolose 1:17-18*

**B. Kutenga Yesu kukhala mbuye wako ndiko kupindula monga mwa chifuniro cha Mulungu.**

*“Kucita cikondwero canu kundikonda, Mulungu wanga; Ndipo malamulo anu ali m’kati mwamtima mwanga.” – Maslamo 40:8*

*“Pakuti wakucita mwa inu kufuna ndi kucita komwe, cifukwa ca kukoma mtima kwace, ndiye Mulungu.” – Afilipo 2:13*

**C. Kutenga Yesu kukhala mbuye wako ndikukhala ndi chidziwitso kuti siuli wekha.**

*“Ndipo adafera onse, kuti iwo akukhala ndi moyoasakhalenso ndi moyo kwa iwo okha, koma kwa iye amene adawafera iwo, nauka.” – 2 Akorinto 5:15*

**D. Kutenga Yesu kukhala mbuye wako ndiko kukonda Mulungu ndi umunthu wako onse.**

*“Ndipo muzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mphamvu yako yonse.” – Marko 12:30*

**ZOKAMBIRANA:**

Yesu ndiye chitsanzo chenicheni komanso muyezo woonetsa m’mene umbuye umakhalira pa moyo wathu. Ngakhale anali Mulungu kuthupi, analora kudzikana yekha ndikudzipereka ku chifuniro cha Atate.

*“Iye wakunena kuti akhala mwa iye, ayeneranso mwini wace kuyenda monga anayenda iyeyo.” – 1 Yohane 2:6*

Kodi inu munasankha kutenga Yesu kukhala Mbuye wa moyo wanu komanso kutsata ndondomeko ya umbuye m’mene imakhalira?

Kodi ganizo limeneri linasinatha bwanji m’mene inu mumachitira ndi ufulu wanu mwa Khristu?



# KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA

43. Fotokozani mwa mau anu kuti kukhala ndi ufulu mwa Khristu zimatanthauza chiyani?

---

---

---

44. Kodi ndi zisankho ziwiri ziti zomwe inu muli ndi ufulu wopanga mkati mwa ufulu wanu mwa Yesu Khristu? Chonde tchulani ndime zothandizira kufotozera zimenezi.

- i. 

---

---
- j. 

---

---

45. Fotokozani m'mene kupanga Yesu kukhala Ambuye wanu kumakutetezani inu kuti musagwiritse ntchito ufulu umene Mulungu anakupatsani molakwika.

---

---

---

46. Tchulani zitsanzo zitatu za m'mene ufulu wanu ukhonza kuononga anthu ena amene akuzungulirani?

- a. 

---
- b. 

---
- c. 

---

47. Kodi inu mukudziwa funso lofunikira limene mukhonza kufunsa pofuna kudziwa malire a ufulu wanu? Nanga ndi chifukwa chiyani?

---

---

---

---

**48. Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?**

---

---

---

---

---

## **KUPHUNZIRA BAIBULO PA WEKHA**

**Mu Machitidwe 10:9-20** Mulungu anamuonetsa mtumwi Petro maloto oti adye zakudya zimene zinali zoletsedwa kwa anthu a Mulungu. Kodi mukuganiza kuti Mulungu amamuphunzitsa chiyani Petro kudzera mu malotowo?

---

---

---

**Werengani Machitidwe 10:27-35.** Kodi Petro anabwera ndi zotsatira zotani pa maloto ake? Kodi anthu amene anali m'nyumba ya Korneliyo anakhudzidwa bwanji ndi za ufulu mwa Yesu umene Petro anakamba?

---

---

---

---

**Werengani Agalatiya 2:11-16.** Ufulu umene Petro anali nawo mwa Yesu Khristu unamuvomereza iye monga myuda kutumikira ndi kugawa moyo ndi anthu amene sanali Ayuda(Amitundu). Kodi Petro anatani pamene ufulu wake mwa Yesu unayesedwa ndi chilamulo cha chipembedzo? Kodi kuyankha kwake kunakhudza bwanji anthu amene anamuzungulira iye? Kodi mtumwi Paulo ananena chiyani pa umboni wa Petro?

---

---

---

---

---

---

**Ufulu wathu mwa Khristu umatimasula ife ku kumangidwa ndi tchimo ndi cholinga chakuti titumikire Yesu Khristu monga Ambuye. Werengani 1 Akorinto 7:22-23** ndipo mufotokoze mwa mau anu kuti kumasuka kutumikira Khristu zikutanthauza

**chiyani. Kodi kumapeto kwa zonse Paulo anafotokoza zotani za kutumikira anthu kapena Ambuye monga mwa ufulu wathu wathu?**

---

---

---

---

---

---

## 12. CHIFUNIRO CHA MULUNGU

*Ngati mukufuna kukhala opambana m'moyo, muyenera kudziwa chimene Mulungu akufuna kuti mukwaniritse ndi kuchifikira. Muyeso woona wa kupambana sizimatengera ndi m'mene inu muliri, kukhazikika kwa chuma chanu, kutchuka kapena zimene anthu amakudziwani nazo; zonse zagona pa kumvera chifuniro cha Mulungu m'moyo wanu.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*KUFANIZIDWA*

**Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Kodi ndingadziwe bwanji za chifuniro cha Mulungu m'moyo mwanga?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kuvumbulutsa za chifuniro cha Mulungu kuchokera m'mau a Mulungu, ndi cholinga choti mufananizidwe ndi chifuniro cha Mulungu m'moyo mwanu.*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Inu muyenera kukhala ofananizidwa ndi chifuniro cha Mulungu iye asanakutsogolereni mu zochitika za pa moyo wanu.*

### **NDIME ZA PAMTIMA:**

*“Cifukwa cace ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano; koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno chan Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro.” – Aroma 12:1-2*

*“Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa.”*

# PALI KUSIYANA KOTANI PAKATI PA CHIFUNIRO CHA MULUNGU, DONGOSOLO LAKE NDI CHOLINGA CHAKE PA MOYO WANU?

---

## BB. Chifuniro cha Mulungu

1. Chifuniro cha Mulungu chimakhudzana ndi inu amene muli mwa Khristu, ndipo ndi zofanana kwa wina aliyense. Izi zimatengera ubale wanu ndi Mulungu, ndipo sizimayenderanso malamulo, kapena dera kapena utumiki.

*“Cifukwa cace ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano; koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene cirri cifuno chan Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro.” – Aroma 12:1-2*

2. Inu muyenera kufulumizidwa kupanga nthawi yanu ngakhale iri yochepa kuti mutumikire lye pamene mukufufuzanso kuti mudziwe ndi kumvetsa za chifuniro cha Mulungu.

*“Poteru, penyani bwino umo muyendera, si monga opanda nzeru, koma monga anzeru; akucita macawi, popeza masiku ali oipa. Cifukwa cace musakhale opusa, koma dziwitsani cifuniro ca Ambuye nciani.” – Aefeso 5:15-17*

## CC. Dongosolo la Mulungu

1. Dongosolo la Mulungu limakhudzana ndi ndi chimene inu mumachita mwa Khristu. Zimatengera chitsogozo china chake chimene Mulungu amapereka kwa inu pamene mukumana ndi nyengo zosiyanasiyana m’ moyo wanu.

*“Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwacititira ubwino, ndiwo amene aitanidwa monga mwa kutsimikiza kwa mtima wace..” – Aroma 8:28*

2. Mulungu amafuna kuti inu mukwaniritse chifuniro chake pamene muchita zimene lye akufuna monga mwa dongosolo lake pa moyo wanu. Zimene mukukumana nazo ngati munthu panokha, ziyenera kukutsogolerani kuti mukwaniritse chifuniro chonse cha Mulungu.

*“Akulankhulani inu Epafra ndiye wa kwa inu, ndiye kapolo wa Yesu Khristu, wa kulimbira, cifukwa ca inu m’mapemphero ace, masiku onse, kuti mukaima amphumphu ndi odzazidwa m’cifuniro conse ca Mulungu.” –Akolose 4:12*

## **DD. Cholinga cha Mulungu**

1. Mulungu analenga anthu ndi cholinga choti alemekeze lye.

*“Muyenera inu, Ambuye wathu, ndi Mulungu wathu, kulandira ulemelero ndi ulemu ndi mphamvu; cifukwa mudalenga zonse, ndipo mwa cifuniro canu zinakhala, nizinalengedwa.”*

**– Cibvumbulutso 4:11**

2. Mulungu amalemekezedwa pamene inu mukwaniritsa cifuniro chake kudzera m’moyo umene mumakhala mwa lye.

*“Ine ndalemekeza Inu pa dziko lapansi, m’mene ndinatsiriza ntchito imene munandipatsa ndicite.” – Yohane 17:4*

# **KODI CHIFUNIRO CHA MULUNGU PA MOYO WANGA NDI CHOTANI?**

**Ndi chifuniro cha Mulungu kuti okhulupirira wina aliyense afanizidwe ku chifanizo cha Yesu Khristu.**

*“Cifukwa kuti iwo onse amene lye anawadziwiratu, iwowa anawalamuliratu, iwowa afanizidwe ndi cifaniziro ca Mwana wace kuti lye akakhale mwana woyamba mwa abale ambiri” – Aroma 8:29*

## **D. Ndi chifuniro cha Mulungu kuti MUPULUMUTSIDWE**

Ndi udindo wanu kugawana nawo uthenga wabwino anthu otaika chifukwa ndi chifuniro cha Mulungu kuti anthu apulumuke. Sichifuniro cha Mulungu kuti wina wake asapulumutsidwe.

**2 Petro 3:9**

## **E. Ndi chifuniro cha Mulungu kuti MUYERETSEDWE.**

Inu muyenera kukhala m’moyo wosiyana ndi ena kuti mukhale mu chiyero.

**1 Atesalonika 4:3-7**

## **F. Ndi chifuniro cha Mulungu kuti inu MUONETSE KUYAMIKA**

Mulungu amafuna kuti inu mudziyamika mu zochitika zina zirizonse m’moyo wanu.

**1 Atesalonika 5:18**

### G. Ndi chifuniro cha Mulungu kuti inu MUTUMIKIRE.

Inu muyenera kutumikira iwo amene ali ndi ulamuliro pa inu monga m'mene mutumikirira Yesu Khristu.

*Aefeso 6:5-7*

### H. Ndi chifuniro cha Mulungu kuti inu mukhale ODZIPEREKA.

Inu muyenera kudzipereka ku lamulo lirilonse la munthu monga umboni ku dziko lotaika limene tiri. Komabe, kudzipereka kwanu kwa iwo amene ali ndi ulamuliro, ziyenera kuyezedwa ndi mulingo wapamwamba wofuna kukondweretsa Mulungu.

*1Peter 2:13-15*

### I. Ndi chifuniro cha Mulungu kuti inu MUZUNZIKE.

Inu mudzakumana ndi mazunzo pamene mukutsata Yesu Khristu. Mazunzo amene ife timapirira akuyenera kudza chifukwa timachita zabwino osati zoipa.

*1 Petro 3:17; 1 Petro 2:19-21*

**Chifuniro cha Mulungu chikhonza kukambidwa mwachidule komanso kumvetsetseka mu mau atatu:**

1. CHIPULUMUTSO *1Timoteo 2:3-4*
2. CHIYERETSO *1 Petro 4:1-2*
3. KULANDIRA ULEMELERO *Aefeso 1:3-5*

#### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu mukuchitapo kanthu kuti anthu ochimwa abwere ku chipulumutso?

Kodi mukukhala m'moyo mwanu ndi kukwaniritsa chifuniro cha Mulungu kapena chifuniro cha thupi?

Kodi muli okonzeka kuti mukafike pa maso a Mulungu opanda chirema?

## **KODI DONGOSOLO LA MULUNGU PA MOYO WANU NDI LOTANI?**

### **MFUNDO YOFUNIKIRA MU PHUNZIRO IRI!**

Kumvera chifuniro cha Mulungu ndizofunikira kwambiri kusiyana ndikudziwa dongosolo la Mulungu. Inu muyenera kukhala ofananizidwa ndi chifuniro cha Mulungu iye asanakutsogolereni mu zochitika za pa moyo wanu. Choyambirira m'moyo wanu chikhale kukwaniritsa chifuniro cha Mulungu m'moyo mwanu tsiku ndi tsiku, komanso kukhulupirira lye kuti akutsogolereni pa tsatanetsane wa dongosolo la moyo wanu pang'ono ndi pang'ono.

**A. Mulungu amavumbulutsa za chitsogozo chake pa moyo wanu popereka zinthu zitatu.**

- a. Mulungu wakupatsa inu Mzimu Woyera kuti akutsogolereni chifukwa lye amakhala mwa inu.

***Agalatiya 5:25; Yohane 16:13***

- b. Mulungu wakupatsa inu mau a Mulungu kuti akhale ulamuliro weni weni mu zochitika zonse za moyo wanu. Inu mwayenera kuphunzira kudzada malingaliro anu ndi malingaliro a Mulungu. Dongodolo la Mulungu pa moyo wanu siidzaononga kapena kusintha zimene ziri mu baibulo.

***Masalimo 119:105; 1 Atesalonika 2:13***

- c. Mulungu wakupatsa mpingo wa pamalo kukukonzekeretsani iwe pa moyo komanso utumiki wako. Mulungu amapereka uphungu wabwino kudzera mwa okhulupirira ena amene akuzungulira iwe.

***Aefeso 4:11-12; Machitidwe 13:1-4***

**B. Mulungu adzagwiritsa ntchito zochitika ndi nyengo za m'moyo wanu pokutsogolerani.**

Pamene nyengo zosiyanasiyana zidza, Mulungu adzatsimikiza za dongosolo lake kudzera mu baibulo, potsogolera inu ndi Mzimu Woyera komanso mpingo wa pa malo.

***Aroma 8:28; Masalimo 37:23***

**C. Mulungu ali amachita chidwi kwambiri ndi inu kusiyana ndi chimene mukhonza kumuchitira.**

Kudziwa chimene Mulungu akufuna kuti inu muchite sizofunikira kwambiri kusiyana ndi chimene Mulungu akufuna kuti inu mukhale. Pamene mukula mu chifanizo cha Mulungu, adzavumbulutsa chimene lye akukhumba kuti inu muchite.

***Afilipi 2:13***

## **MAFUNSO ENA AMENE INU MUKHONZA KUFUNSA**

---

**E. Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu samavumbulutsa tsatanetsatane wa dongosolo lake pa moyo wanga tsopano lino?**

*“Ndiri nazo zambirinso zakunena kwa inu koma simungathe kuzisenza tsopano lino.” – Yohane 16:12*



- a. Kudziwa dongosolo lonse la Mulungu ya moyo wanu pa nthawi imodzi zikhonza kukuonogngani kwambiri.
- b. Inu mukhonza kukhala kuti simunakonzekere kuchita zonse pano. Mulungu adzavumbulutsa zimene inu mukhonza kukwanitsa kuchita.
- c. Mukhonza kukhala kuti simukuyenda momvera Mulungu pa zimene lye anavumbulutsa kale.
- d. Pamene mukula kuthupi ndi kuuzimu, zokhumba zanu, luso lanu, ndi zofuna zimasintha. Mulungu akufuna kuti inu mukhale odekha pamene lye akugwira ntchito m'moyo wanu wauzimu.

**F. Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu amatha kulora zinthu zina zooneka zoipa kuchitika ku m'moyo mwanga?**

- a. Mulungu adzalora kuti inu muzunzike kuti akukonzeni mukhale amphumphu. Nthawi zovuta m'moyo wanu zimakubweretsani pafupi ndi Mulungu kuti mukadziwe kuti lye ndindani komanso kuti inu ndindani.

***1 Petro 1:6-9; 1 Petro 5:10***

- b. Nthawi zonse pali zotsatira zimene zimadza kamba ka zisankho zimene Mulungu amalora kuti tipange. Mulungu anakupatsani inu ufulu wosankha ndipo lye sadzakakamiza inu kuti mupange chisankho cholingana ndi baibulo. Mwina pakhonza kukhala nthawi zimene inu mungathe kuzunzika chifukwa cha zisankho zimene munapanga.

***Agalatiya 6:7-8***

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu muli ndi chitsanzo cha m'mene Mulungu anakupatsani chitsogozo m'moyo mwanu?

Kodi mukudziwa kuti dongosolo la Mulungu pa moyo wanu ndilotani lero?

## **KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA**

---

**17. Kodi pali kusiyana kotani pakati pa chifuniro cha Mulungu ndi dongosolo la Mulungu?**

---



---



---



---

**18. Tchulani zinthu zisanu zimene ziri chifuniro cha Mulungu pa moyo wanu.**

- E. \_\_\_\_\_
- F. \_\_\_\_\_
- G. \_\_\_\_\_
- H. \_\_\_\_\_
- I. \_\_\_\_\_

**19. Gwiritsani ntchito malemba kukamba mwachidule za chifuniro cha Mulungu pa moyo wa m'khristu.**

---

---

---

---

**20. Kodi ndi zinthu ziti zimene Mulungu wakupatsani kuti aonetsere dongosolo lake pa moyo wanu?**

---

---

---

---

---

**21. Kodi chinthu choyambirira pa moyo wanu ndi chiyani?**

---

---

---

**22. Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?**

---

---

---

---

---

## **KUPHUNZIRA ZA BAIBULO PAWEKHA**

**Werengani 1 Mafumu 17:1-9 ndipo mufotokoze zam'mene Mulungu anavumbulutsira dongosolo lake kwa Eliya.**

---

---

---

---

---

**Molingana ndi *1 Petro 5:10*, Mulungu amalora kuti akhristu kuti adutse mu mazunzo ndi cholinga choti....**

1. \_\_\_\_\_

2. \_\_\_\_\_

3. \_\_\_\_\_

4. \_\_\_\_\_

**Kodi dongosolo la Mulungu kuti uthenga wabwino ufikire ku maiko a azungu unavumbulutsidwa bwanji kwa Paulo pa Machitidwe *16:1-13*?**

---

---

---

---

---

---

**Lembani umboni wa chitsanzo chimodzi cha mmene Mulungu anavumbulutsira dongosolo lake pa moyo wanu.**

---

---

---

---

---

---

---

---

## 13. KUPEREKA

*Mulungu ndi Mulungu wopereka, ndipo chifuniro chake ndi choti inu muonetse chikhalidwe chake popereka. Ndi zinthu zofunikira kuti mumvetsetse kuti Mulungu ndiye mwini wake wa chinachirichonse, ndipo samafuna ndalama zanu. M'mene inu mumaperekerera zimaonetsa kukura kwana monga okhulupirira. Kupereka ndi chochitika cha chikhulupiliro komanso kulambira, ndipo zimaonetsa chikondi chanu pa Mulungu ndi utumiki wake. Phunziro iri likuthandizani kuti mumvetse udindo wanu poyang'anira moyo ndi zimene muli nazo.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*KUPEREKA ULAMULIRO*

***Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziroli iri ndiri:***

*Kodi kupereka kumatanthauza chiyani, ndipo kodi udindo wanga ndi wotani?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kukuthandizani kumvetsetsa za chikhalidwe cha kupereka monga mwa chiphunzitso cha Chipangano Chatsopano.*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Kupereka koona kwenikweni monga mwa Chipangano Chatsopano kumakhudzana ndi kuchotsa ulamuliro wanu pa zonse za m'moyo wanu ndi zinthu zanu ndikupereka ulamuliro kwa Yesu Khristu.*

**NDIME ZA PAMTIMA:**

*"Yense acite monga anatsimikiza mtima, si mwa cisoni kapena mokakamiza, pakuti Mulungu akonda wopereka mokondwerera." – 2 Akorintho 9:7*

*"Pakuti kumene kuli cuma cako, komwe udzakhala mtima wakonso.." – Mateyu 6:21*

# KODI MULUNGU AMAFUNA INU KUTI MUPEREKE CHIFUKWA CHIYANI?

## MFUNDO YOFUNIKIRA MUPHUNZIRO ILI!

Chirichonse chimene muli, komanso chimene mulinacho ndi za Mulungu. Iye samafuna kapena kusowa ndalama yanu. Mulungu akufuna inu! Cholinga cha kupereka kwa chipangano chatsopano ndi kupereka ulamuliro wonse wa moyo komanso chuma chanu kwa Yesu Khristu. Ngati akhala ndi ulamuliro wonse pa moyo wanu, iyenso amakhala ndi ulamuliro pa chuma chanu. Momwe mumaperekera zimawonetsera momwe mumakhulupilira Mulungu kufukira zosowa zanu za tsiku ndi tsiku.

*“Mulungu amene analenga dziko lapansi ndi zonse ziri momwemo, Iyeyo, ndiye mwini kumwamba ndi dziko lapansi, sakhala m'nyumba zakacisi zomangidwa ndi manja; satumikidwa ndi manja a anthu, monga wosowa kanthu, popeza iye mwini apatsa zonse moyo ndi mpweya ndi zinthu zonse;” – Macitidwe 17:24-25*

*“Iye amene akhulupirika m'cacing'onong'ono alinso wokhulupirika m'cacikuru; ndipo iye amene ali wosalungama m'cacing'onong'ono alinso wosalungama m'cacikuru. Cifukwa cace ngati simunakhala okhulupirika m'cuma ca cosalungama, adzakhulupirira inu ndani ndi cuma coona?” – Luke 16:10-11*

## EE. Kupereka kumakutsogoleraninso pa kuchotsa kuyang'ana pa zinthu za m'dziko ndi cholinga choti muikize pa zinthu zamuyaya..

*“Musadzikundikire nokha cuma pa dziko lapansi, pamene njenjete ndi dzimbiri ziononga; ndi pamene mbala ziboola ndi kuba: 20koma mudzikundikire nokha cuma m'Mwamba, pamene njenjete kapena dzimbiri siziononga, ndipo mbala siziboola ndi kuba; 21pakuti kumene kuli cuma cako, komwe udzakhala mtima wakonso..” – Mateyu 6:19-21*

## FF. Kupereka kumabweretsa mantha a pa Ambuye mwa inu nokha, chifukwa mukuonetsa kuti chinthu chanu choyambirira ndiko kulemekeza Mulungu..

*“Ndipo muzidye pamaso pa Yehova Mulungu wanu, m'malo m'mene asankhamo iye, kukhalitsamo dzina lace; limodzi la magawo khumi la tirigu wanu, la vinyo wanu, ndi la mafuta anu, ndi oyamba kubadwa a ng'ombe zanu ndi a nkhosa ndi mbuzi zanu; kuti muphunzire kuopa Yehova Mulungu wanu masiku onse..” – Deuteronomy 14:23*

**GG. Kupereka kumakhazikitsa kudalira Mulungu chifukwa inu mwakhulupirira lye kuti ndiye amene apereke zinthu zanu ngakhale za mtsogolo..**

*“Lemekeza Yehova ndi cuma cako, Ndi zinthu zako zonse zoyambirira kuca; Motero nkhokwe zako zidzangoti the, Mbiya zako zidzasefuka vinyo..” – Miyambo 3:9-10*

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi muli ndi chosowa chimene mukumdalira nacho Mulungu?

Kodi munayamba mwasankha kusapereka kwa Ambuye chifukwa zimaoneka ngati simungakwanitse?

Kodi munachitapo chisankho kumvera ndi kupereka kwa Ambuye ngakhale kuti munali osowa? Kodi Mulungu anakumana bwanji ndi chosowa?

## **KODI MULUNGU AKUFUNA KUTI MUPEREKE KUTI?**

---

**A. Poyambirira khalani okhazikika pa zopereka zanu potsata ndondomeko ya pa mpingo wanu wa pamalo**

Chinthu choyambirira kuchidziwa pa kupereka kumene baibulo likufotokoza ndi kupereka kudzera mu mpingo wanu wapamalo chifukwa Mulungu anasankha mpingo umenewo kuti augwiritse ntchito ndi kukwanitsa ntchito yofikira anthu onse pa dziko lapansi. Ndi chinthu chofunikira kumvetsetsa kuti kupereka kwina kulikonse kunjira kwa mpingo wanu sikuyenera kusokoneza kupereka kwanu monga mwa nthawi zonse ku mpingo wanu. Ndi chinthu chofunikanso kusamalanso kuyang’anitsitsa za kupereka kwanu pa zifukwa zimene ziri za muyaya.

**1 Akorinto 16:1-2**

**A. Atsogoleri a mumpingo wanu ali ndi udindo wokhala oyang’anira zinthu bwino.**

Atsogoleri a pa mpingo panu ali ndi udindo oyang’anira bwino anthu a mumpingo, komanso kusamala ntchito ya Ambuye. Monga membala wa mpingo wa pamalo, inu muyenera kuona za m’mene zinthu za pa mpingo zikugwiirira ntchito, ndipo muyeneranso kukhulupirira utsogoleri wanu kuti ayanang’anire bwino zinthu zonse mwa nzeru.

**2 Akorinto 8:20-22**

## **KODI MULUNGU AKUFUNA INE KUTI NDIPEREKE MOTANI?**

---

Mu kalata wake wachiwiri ku mpingo wa ku Korinto, mtumwi Paulo anagwiritsa ntchito mipingo yaku Makedoniya monga chitsanzo pa za m’mene kupereka koyenera kwa baibulo kumayenera kukhalira kwa okhulupirira a mu Chipangano Chatsopano. Umboni wokhudza za m’mene mipingo yaku Makedoniya

inaperekera ndi phunziro lalikuru limene okhulupirira onse ayanera kuphunzira.

- A. Kufunitsitsa kwanu kupereka ku utumiki wa Mulungu ndi chinthu chofunikira kwambiri kusiyana ndi kuchuruka kapena kuchepa kwa chopereka chimene inu mukhonza kupereka.

a. *2 Akorinto 8:1-3*

- B. Kupereka kwanu kuyenera kuyamba ndi kudzipereka nokha kwa Ambuye ndi kwa anthu.

a. *2 Akorinto 8:4-5*

- C. Kupereka kumakulitsa kuchisomo pamenenso mukula mu ubale ndi Mulungu.

a. *2 Akorinto 8:6-7*

- D. Kupereka kumaonetsa kuchuluka kwa chikondi chanu pa Mulungu, mpingo komanso utumiki wake.

a. *2 Akorinto 8:8-9*

- E. Kupereka kwanu kukhale molingana ndi m'mene Mulungu wakudalitsirani. Simuyenera kufananiza mulingo wa kupereka kwanu ndi m'mene anthu ena aperekera.

a. *2 Akorinto 8:10-12*

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi mukupereka mokhulupirika kudzera mumpingo wanu wapamalo?

Kodi kupereka kwanu kwa Ambuye kwasintha bwanji maonedwe anu a kufunika kwa ntchito ya Mulungu?

Kodi munayamba mwalorapo kupereka kwa munthu wina kusintha maperekedwe anu?

## **KODI MULUNGU AKUFUNA KUTI INU MUPEREKE CHIYANI?**

- A. Pali mitundu itatu ya zopereka imene inakambidwa mu malemba a Chipangano Chakale.

### **1. Zachikhumi**

Chachikhumi ndi gawo limodzi la pa magawo khumi limene munthu wapeza limene limachotsedwa pa zonse zimene wapeza. Izi zinaperekedwa kwa Mulungu ngati

chikumbutso chifukwa lye ndi amene amatipatsa zimene tirinazo, komanso kuonetsa kuti Mulungu ndiye amene amakhala koyambilira.

***Malaki 3:10; Deuteronomo 26:2, 10***

**2. Zoperera zaufuru**

Kuonjezera pa zachikhumi, zoperera zaufuru zinaperekedwa ndi anthu a Mulungu zothandizira pa zosowa zimene zikhonza kupezeka pakati pa mpingo. .

***Exosodo 25:1-2***

**3. Zoperera za msembe**

Izi ndi zoperera za mphatso zimene zimakhala ngati nsembe zimene operekayo wafunitsitsa kudzipereka motero. Inali ngati nsembe imene munthu amakhonza kupereka mwa kufuna kwake monga choikiza mu utumiki wa Mulungu.

**2 *Samueli 24:21-25***

- B. Monga okhulupirira wa mu Chipangano Chatsopano, kupereka kwanu kuyenera kukhazikika pa mfundo za baibulo pamene mukhazikitsa chozolowezi chakupereka m'moyo mwanu.**

*“Pakuti zonse zinalembedwa kale zinalembedwa kutilangiza, kuti mwa cipiriro ndi citonthozo ca malembo, tikhale ndi ciyembekezo.” – Aroma 15:4*

**1. Perekani nthawi zonse kuti muthandize ntchito yoyendetsa mpingo wa pamalo.**

Monga m'mene anthu a M'chipangano Chakale amabweretsera chakhumi kuthandizira ntchito ya utumiki wa Mulungu, inunso muyenera kuika mulingo winawake umene inu mukhonza kutsatira popereka nthawi zonse. Mphatso zimenezi zimathandizira kupereka ku ntchito zoyendetsera zinthu zina pa mpingo, kulipira ogwira ntchito, ndi kuthandizira zinthu zina pa utumiki.

***1 Akorinto 9:14; 1 Timoteo 5:17-18***

**2. Perekani molowa manja kuti muthandizire ntchito zina zapadera ndi mautumiki mu mpingo.**

Monga m'mene anthu a Mulungu anali kuperekera zoperera kuthandizira ku zosowa zapaderadera, inunso muyenera kukhala okonzeka kupereka panthawi imene pali zosoweka mu mpingo wanu. Mphatso zimenezi zimathandizira zosowa zamamembala amene ali mu mpingo amene sangathe kudzithandiza okha, komanso kuthandiza ntchito zina zapaderadera za pampingo zimene atsogoleri aziona kuti zigwiridwe.

***Machitidwe 11:27-30; 1Timoteo 5:3, 9-10, 16***

**3. Perekani nsembe zanu pothandizira utumiki.**

Monga m'mene anthu a Mulungu anali kuperekera zoperera monga nsembe kuti zithandizire utumiki, inunso muyenera kukhala okonzeka kupereka kuthandizira ntchito ya utumiki kuti mpingo ukhonza kutumiza anthu a mishoni ndi kuwavomereza kuti akatumikire. Mphatso zimenezi zimathandiza atumiki a mishoni kupita malo amene inu simungathe kupitako.



**C. Mulungu sanalamulire inu kuti mupereke ndalama ina yake yokhazikika**

Mulungu anapereka ufulu kwa munthu kuti akhonza kupereka mwina mulimonse. Kupereka kumene Chipangano Chatsopano chikukamba kumagwirizana ndi nkhani yokura ndi kukhwima mwa Khristu, kusiyana ndi nkhani ya ndalama. Mulungu amafuna inu atunthu. M'mene inu mumaperekerera zimaonetsera kuya kwa wuzimu mukuyenda kwanu ndi Mulungu. Munsimu muli mfundo zina zimene mukhonza kutsatira pamene mulingalira za mulingo oti mupereke nthawi zonse kudzera ku mpingo wanu:

**1. Pangani dongosolo labwino la nthawi yanu, utumiki wani, komanso chuma chanu moyang'anira pa kupereka.**

Okhulupirira ambiri amakhala ndi mavuto pa kupereka nthawi zonse chifukwa amalephera kukonzekera bwino kupereka.

**2 Akorinto 9:1-4**

**2. Lingalirani kuti ndi ndalama zingati zimene inu mukhonza kupereka musanafike ku tchalitchi.**

Kupereka kwanu kwayenera kukhala pakati pa inu ndi Mulungu. Ngati mudikira kuti mukafike kutchalitchi, ndi zotheka kuti kupereka kwanu kukhonza kusalongosoka mwina potengeka ndi kupereka kwa anthu ena.

**2 Akorinto 9:5**

**3. Kumbukirani lamulo lobzala ndi kututa.**

Inu simuyenera kupereka ndi chiyembekezo choti mulandire phindu pa mapeto pake. Komabe Mulungu analonjeza kudalitsa anthu opereka mokhulupirika. Pamene mudzionetsa nokha kukhala okhulupirika ndi zimene Mulungu wakupatsani, lye adzakudalirani ndi kukupatsani zinthu zina zochuluka.

**2 Akorinto 9:6**

**4. Kupereka kwanu kudzichokera mu mtima umene uli wofuna komanso kukonzeka kupereka.**

Kodi inu mukupereka kwa Mulungu chifukwa choti muyenera kutero, kapena mukufuna kubweza zake za Mulungu?

**2 Akorinto 9:7**

**5. Mulungu adzakupatsani zosowa zanu.**

Pamene mukupereka kuthandiza ku ntchito yofalitsa uthenga monga lamulo lalikuru limene timapanga nalo ophunzira pa dziko lonse lapansi, Mulungu adzaonetsetsa kuti muli nazo zinthu zokwanira kuti mukhonze kuthandiza kukwaniritsa lamulo lalikuru limeneli kudzera ku mpingo wanu.

**2 Akorinto 9:8**

**6. Mulungu adzalemekezedwa kudzera mu kupereka kwanu.**

Chikhalidwe chenicheni china cha Mulungu ndi kupereka. Iye anakupatsani mphatso yaikuru kwambiri imene iri chipulumutso kudzera mu imfa, kuikidwa m'manda komanso kuuka kwa Ambuye Yesu Khristu. Pamene mupereka molingana ndi mfundo za m'baibulo, mudzakhala monga mwa chikhalidwe cha Yesu Khristu m'moyo wanu, ndipo Mulungu adzalemekezeka kudzera mwa inu.

### **2 Akorinto 9:9-15**

#### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi mwakonzetsera nthawi yanu ndi chuma chanu kuti mukhale womasuka kuti mukhoza kukhala womasuka kupereka mwapafupifupi?

Kodi mwakonda ndalama yapadera imene mumapereka pafupipafupi?

Kodi Mulungu akulandira ulemu kudzera mukupereka kwanu?

## **KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA**

**1. Tchulani zifukwa zitatu zimene Mulungu akufuna inu kuti mudzipereka.**

a. \_\_\_\_\_

b. \_\_\_\_\_

c. \_\_\_\_\_

**2. Kodi ndi chifukwa chiyani kuri kofunikira kuti inu poyamba muyang'anitsitse za ndondomeko yaku mpingo kwanu popereka?**

\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_

**3. 2 Akorinto 8:1-2 ikutiphunzitsa kuti okhulupirira a ku Makedoniya anali odzipereka pa kupereka. Tchulani zitsanzo zisanu zimene ife tingaphunzire za m'mene anali kuperekera.**

a. \_\_\_\_\_

b. \_\_\_\_\_

c. \_\_\_\_\_

d. \_\_\_\_\_

e. \_\_\_\_\_

4. Tchulani mfundo zitatu za m'baibulo zimene inu mukhonza kuyamba kuzitsata m'moyo mwanu pamene mukukhala ndi chizolowezi cha kaperekedwe pamoyo wanu.

a. \_\_\_\_\_

b. \_\_\_\_\_

c. \_\_\_\_\_

5. Kodi Mulungu mu Chipangano Chatsopano akunena mulingo okhazikika wa kuchuruka kwa ndalama zimene munthu akhonza kuperekerana? Chifukwa chiyani?

---

---

---

6. Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?

---

---

---

#### KUPHUNZIRA ZA BAIBULO PAWEKHA

Mulungu anaitana mtundu wa Israyeli kuti abweretse zopereka pothandizira kumanga chihema pamene iwo anali mu chipululu. Werengai Ekisodo 35 ndipo mulembe zina mwa njira zimene anthu anapereka zimene si ndalama. Kodi ndime imeneyi ikukamba zotani za mitima ya anthu pamene anapereka. Kodi ndi njira zina ziti osati ndalama zimene inu mukhonza kupereka ku utumiki wa Mulungu?

---

---

---

---

Werengani Luka 6:38, ndipo tchulani malonjezo a Mulungu okhudza za kupereka.

---

---

---

Mu *Luka 21:1-4*, Yesu akufananiza za ndalama zimene mayi wamasiye anapereka poyerekeza ndi zimene bambo wina wachuma anapereka mu malo operekerana mu kachisi. Kodi Yesu ananena chiyani zokhudza chopereka cha mzimayi uja? Kodi Yesu anati chiyani zokhudza kusiyana kwa kupereka kwa mzimayi uja ndi bambo wachuma uja?

---

---

---

---

**Mu Machitidwe 2 timawerenga za anthu ambiri amene anayenda mitunda italiitali pokakhala nawo pa phwando la pentekoste. Atatha kumva uthenga wabwino, ambiri anavomereza Khristu monga Mpulumutsi. M'malo mopita kunyumba, anasankha kukhala mbali imodzi ya mpingo wa ku Yerusalemu. Izi zinabweretsa vuto lalikuru lokhudza zachuma, ndipo anthu ambiri mu mpingo watsopano anali ndi vuto lolephera kupereka zinthu zokwanira pothandizira maanja awo. Werengani Machitidwe 4:34-37. Kodi anadzipereka motani pa kupereka? Kodi mphatso zawo anazitenga kuti? Kodi ndi ndani amene anali ndi udindo wogawa zimene iwo anabweretsa?**

---

---

---

---

---

---

---

---

# NDALAMA NDI CHUMA

*Limodzi la yesero lalikuru limene okhulupirira amakumana nalo ndi kuchuluka kwa kukonda zinthu zimene ziri m'dziko. Nthawi zina timasocheretsedwa pokhulupirira kuti kuchita bwino kwa munthu kumaonetsedwa kudzera mu chuma, pamene kuchita bwino molingana ndi baibulo kumayesedwa potsatira chifuniro cha Mulungu. Okhulupirira ambiri amatha kukhala mu nyengo zoopsa chifukwa cha maonedwe ao pa ndalama ndi zinthu zimene ali nazo. Cholinga cha phunziro iri ndi kukutsogolerani kuti mukhonze kusamalira bwino zinthu zanu potsata mfundo za baibulo.*

### **Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kuphunzitsa kuchokera m'malemba zam'mene mungakhalire munthu wabwino wosamala zinthu zimene Mulungu watipatsa monga mwa baibulo.*

### **Mfundo yofunikira mu phunziro iri**

*Kukhala okhutitsidwa ndi zinthu zimene Mulungu wakupatsa.*

#### **Ndime ya pamtima:**

*“Si kuti ndinena monga mwa ciperewero, pakuti ndaphunzira ine, kuti zindikwanire ziri zonse ndiri nazo.” – **Afilipi 4:11***

*“Pakuti kumene kuli cuma cako, komwe udzakhala mtima wakonso.” – **Mateyu 6:21***

## KUKHALA NDI MAONEDWE MONGA OYANG'ANIRA

**HH. Mulungu ndi mwini wa chinachiri chonse chifukwa analenga zonse.**

*“Dziko lapansi nla Yehova ndi zodzala zace zomwe, Dziko lokhalamo anthu ndi iwo okhala m'mwemo.” – **Masalmo 24:1***

*“Pakuti zamoyo zonse za kuthengo ndi zanga, ndi ng'ombe za pa mapiri zikwi. Ndidziwa mbalame zonse za m'mapiri: ndipo nyama za kuthengo ziri ndi Ine. Ndikamva njala, sindidzakuuza: pakuti dziko lonse ndi langa, ndi kudzala kwace komwe.” – Masalmo 50:10-12*

**II. Inu muli ndi udindo woyang'anira gawo limodzi la zinthu za Mulungu. Mulungu ndi mwini wake wa zonse, inu muyan'ganira.**

*“Taonani, comwe ine ndapenyera kukoma ndi kuyenera munthu ndiko kudyu, ndi kumwa, ndi kukondwera ndi nchito zace zonse asauka nazo kunja kuno, masiku onse a moyo wace umene Mulungu ampatsa; pokhala gawo lace limeneli. Inde yemwe Mulungu wamlemeretsa nampatsa cuma, namninkhanso mphamvu ya kudyapo, ndi kulandira gawo lace ndi kukondwera ndi nchito zace; umenewu ndiwo mtulo wa Mulungu.” – Mlaliki 5:18-19*

**JJ. M'mene mumayang'anirira zinthu zanu za kuthupi zimaonetsa m'mene inu mudzayang'anire udindo wanu wa uzimu.**

*“Iye amene akhulupirika m'cacing'onong'ono alinso wokhulupirika m'cacikuru; ndipo iye amene ali wosalungama m'cacing'onong'ono alinso wosalungama m'cacikuru. Cifukwa cace ngati simunakhala okhulupirika m'cuma ca cosalungama, adzakhulupirira inu ndani ndi cuma coona? Ndipo ngati simunakhala okhulupirika ndi zace za wina, adzakupatsani inu ndani za inu eni?” – Luka 16:10-12*

**KK. Mulungu adzawerengera inu mulandu pa kukhulupirika kwanu poyang'anira zinthu zinthu zimene Iye anakupatsani.**

*“Koma kwa ine kuli kanthu kakang'ono ndithu, kuti ndiweruzidwe ndi Inu, kapena pa bwalo la munthu; koma sindiweruza ngakhale ndekha. Pakuti sindidziwa kanthu kakundiparamulitsa; koma m'menemo sindiyesedwa wolungama; koma wondiweruza ine ndiye Ambuye.” – 1 Akorinto 4:2-5*

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu munayamba mwalingalirapo kuti inu mumangoyang'anira chabe zinthu za Mulungu, ndikuti inu mulibe china chiri chonse chanu?

Kodi mukuyang'anira motani zinthu zimene Mulungu anakupatsani?

---

## **KHALANI NDI MAONEDWE A UMUYAYA**

- F. Mulingo wa zinthu zimene inu muli nazo sizimaonetsa za chikhalidwe chanu pamoyo wa uzimu.

*Luka 12:15*

- G. Palibe kufunikira kwina kulikonse kwa muyaya pakukhala ndi zinthu zambiri.

*Luka 12:16-21*

- H. Ndi kwabwino kufunitsitsa kukhala ndi ubale wabwino ndi Mulungu kusiyana ndi chuma cha dziko lapansi.

*Miyambo 15:16; 16:8*

- I. Njira yachangu kwambiri yoonetsa zimene ziri zofunikira mumtima mwanu ndi pounikira za kumene mumaziikiza zinthu zanu.

*Mateyu 6:19-21*

- J. Samalitsani kwambiri poyang'ana za ufumu wa Mulungu, ndipo lolani lye kuti asamalire zosowa za kuthupi.

*Mateyu 6:33*

- K. Chinthu cha mtengo wapatali chimene muli nacho ndi moyo wamuyaya, osati zinthu zanu.

*Mateyu 16:24-26*

- L. Inu muyenera kusankha pakati pa kutumikira Mulungu kapena zinthu zakuthupi.

*Luka 16:13; Akolose 3:2*

#### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi mumafananiza kuchuluka kwa zinthu zanu ndi m'mene Mulungu amakukonderani?

Kodi ndi mbali iti m'moyo mwanu imene mtima wanu umasamala kwambiri?

Kodi mukhala ndi nthawi yambiri poona za zimene mumapeza kusiyana ndi kufunafuna njira za m'mene mukhonzha kuuikiza zinthu zanu popititsa ufumu wa Mulungu patsogolo?

# **KHALANI NDI MAONEDWE A CHIKHULUPIRIRO**

- A. Inu muyenera kukhulupirira Mulungu kuti akuthandizeni pazosowa zanu zonse kusiyana ndi kuyesetsa kuti zinthu zonse muzipezere mwa inu nokha.

*Afilipi 4:19*

- B. Zinthu zanu zimalepheretsa ubale wanu ndi Mulungu ngati muika mtima wanu pa izo.

*Marko 10:23-27; Miyambo 11:28*

- C. Musaiwale Mulungu pamene wakudalitsani ndi zinthu.

*Deuteronomo 6:10-12; Deuteronomo 8:10-18*

- D. Musataye chikhulupiriro mwa Mulungu ngati muli mu nyengo yovuta imene zinthu zaonongeka.

*Yobu 1:20-22*

## **ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu ndi munthu amene amakhutitsidwa wa iye yekha? Kodi chinthu ichi chimasokoneza motani chimene Mulungu amafuna m'moyo mwanu?

Kodi munayamba mwakhala ndi nyengo ya mavuto pa chuma? Kodi zimenezi zinakhudza motani ubale wanu ndi Mulungu?

# **KHALANI NDI MAONEDWE OCHITA ZINTHU MONGA WANGWIRO**

- A. Pewani kukhala m'malo amene mukhonza kupeza mwayi wopeza chuma mwachangu kwambiri.

*Miyambo 20:21; Miyambo 28:20, 22*

- B. Musachite nsanje ndi chuma cha munthu wina.

*Masalimo 49:16-17; Eksodo 20:17*



**C. Musalore kuti kusamala kwanu kwa chuma kusokoneze umboni kapena kupangitsa kuti dzina la Mulungu likhale loipa makamaka mu dera limene mukukhala.**

*Miyambo 30:7-9; Masalimo 37:21*

**D. Khalani oona komanso osamalitsa pochita malonda anu. Mulungu sangakudalitseni pamene musankha kusachita zinthu molingana ndi mfundo za mau a Mulungu zopezera chuma.**

*2 Akorinto 8:21; Miyambo 10:4, 22*

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu munayamba mwalora kuti chuma cha munthu wina chisokoneze ziganizo zanu pa chuma?

Kodi umboni wanu pa nkhani yachuma ndi wotani ku dera lomwe mumakhala?

---

## **KHALANI NDI MAONEDWE OKHUTITSIDWA**

---

**MFUNDO YOFUNIKIRA MU PHUNZIRO IRI.....**

Khalani okhutitsidwa ndi zimene Mulungu wakupatsani. Kukhala okhutitsidwa sizikutanthauza kukhala ndi maonedwe monga osauka kapena kuvutika pa inu nokha ndi kuvomereza momwe moyo wanu uliri. Kukhala ndi maonedwe okhutitsidwa ndi kuzindikira kuti chinachirichonse chimene muli nacho ndi dalitso kuchokera kwa Mulungu, ndipo muyenera kuonetsa kukhutitsidwa kwanu pa zimene Mulungu anakupatsani. Kukhutitsidwa ndi khalidwe limene ife timaphunzira, ndipo nthawi zina limafuna kuti mudutse mu nyengo zovuta kuti muphunzire zimenezi. Mtumwi Paulo anafotokoza za zimene iye anaphunzira zokhudza kukhutitsidwa pamene anali mu ndende.

*“Si kuti ndinena monga mwa ciperewero, pakuti ndaphunzira ine, kuti zindikwanire ziri zonse ndiri nazo. Ndadziwa ngakhale kupeputsidwa, ndadziwanso kusefukira; konseko ndi m'zinthu zonse ndalowa mwambo wakukhuta, ndiponso wakumva njala; wakusefukira, ndiponso wakusowa. Ndikhoza zonse mwa iye wondipatsa mphamvuyo.” – **Afilipi 4:11-13***

**A. Mulungu amagwiritsa anthu osauka ndi olemera kupititsa patsogolo ufumu wake.**

Chinthu chofunikira sikuchuluka wa chuma chimene muli nacho, koma kufunitsitsa kwanu kogwiritsa ntchito zimene Mulungu wakupatsani kuti zimutumikire lye.

1. Yesu anali ndi gulu la azimai achuma amene anathandizira utumiki wake.

**Luka 8:1-3**

2. Paulo anagwiritsa ntchito mipingo yaku Makedoniya monga chitsanzo cha m'mene anthu akhonza kuthandizira utumiki ngakhale pamene iwo ali pa umphawi waukuru.

**2 Akorinto 8:1-3**

**B. Kukhutitsidwa kumachokera pa kukhala ndi kumvetsetsa kuti ubale ndi Mulungu ndi njira yokhayo imene munthu angapeze chuma cha muyaya.**

Nthawi zinanso zimafuna kupereka chuma chanu monga nsembe kuti mulandire mphotho imene Mulungu angapereke.

**Afilipi 3:7-8; 1 Timoteo 6:6-8**

**C. Chikondi cha pa ndalama ndi muzu wa zoipa.**

Olemera ndi osauka onse akhonza kukonda ndalama komanso kuipanga kuti ikhale chimene iwo amafunitsitsa m'moyo wao onse ndipo ikhale yambiri. Komabe iwo sangakhale osangalala, ndipo ikhonza kuwabweretsera chisoni.

**1Timoteo 6:9-10**

**D. Anthu amapeza mavuto a zachuma pa zifukwa zambiri**

Nthawi zambiri, ndichifukwa chakuti iwo samakhutitsidwa ndi zimene Mulungu waapatsa.

1. A zokamba nkhani ndi olingeza malonda ayesetsa kukupangani inu kuti mugule zinthu zochulukira pamene akuonetsani inu kuti mukhale osakhutitsidwa mu mtima mwanu. Baibulo limatchula ichi kuti ndi kusilira, ndipo zimafana ndi kulambira mafano.

**Masalimo 37:4; Akolose 3:5**

2. Kukhala ndi ngongole zambiri ndi zotsatira zoonetsa kuti inu mwagula zinthu zimene inu simungazikwanitse.

**Miyambo 22:7; Aroma 13:8**

**E. Mulungu amafuna kuti inu mukhale oyang'ana mbali zonse bwino pa nkhani ya chuma chanu.**

Pali njira yabwino yothandizira kuyang'ana bwino mbali zonse pa chuma imene muyenera kukhala nayo pa maonedwe a chuma ndi zinthu zimene muli nazo. Baibulo silimadzitsutsa lokha, koma limapereka mfundo zina zimene zingathandize kuyang'ana bwino mbali zonse pa nkhani ya kayendetsedwe ka chuma. Apa pali zina mwa zitsanzo....

1. Fananizani zimene baibulo likunena za kupereka pa zosowa zanu.

*Chifukwa cace musadere nkhowa, ndi kuti, Tidzadya ciani? kapena, Tidzamwa ciani? kapena, Tidzabvala ciani?" – Mateyu 6:31*

*“Pakutinso pamene tinali nanu tidakulamulirani ici, Ngati munthu safuna kugwira nchito, asadyenso.” – 2 Atesalonika 3:10*

2. Fananizani zimene baibulo likunena pa kusunga ndalama ndi zinthu zanu.

*“Wocita ndi dzanja laulesi amasauka; Koma dzanja la akhama lilemeretsa.” – Miyambo 10:4*

*“Pakuti sitinatenga kanthu polowa m'dziko lapansi, ndiponso sitikhoza kupita nako kanthu pocoka pano.” – 1 Timeteo 6:7*

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu mumamva ngati kuti moyo wanu wachuma ukukulepheretsani kutumikira Mulungu kwathunthu?

Kodi ilipo nthawi ina imene inu munasankha kupereka nsembe pa zinthu zanu ndi cholinga chakuti mukhale osamalitsa pa ubale wanu ndi Khristu?

Kodi pali gawo lina la chuma m'moyo mwanu limene muyenera kuliyang'ana kuti liyende bwino?

Kodi moyo wanu wachuma ukupangitsa kuti mudzitumikira ndalama?

Kodi inu muli ndi ndondomeko ya m'mene mumagwiritsira ntchito chuma kuti mutetezeke ku moyo wogula zinthu zimene inu simungakwanitse? Ngati ai, pangani ndondomeko ya nthawi yoti muthandizidwe ndi munthu amene akukuphunzitsani kuti mukhale nayo.

## **KUPHUNZIRA BAIBULO PAWEKHA**

Njira imodzi yabwino imene tikhonza kukura ndi mtima wokhutitsidwa pa zinthu ndikuyang'anitsitsa pa zinthu m'moyo uno zimene ziri zofunikira kusiyana ndi ndalama, komanso zimene ndalama siingagule. Werengani ndime ziri m'musimu ndipo mulembe zina mwa zinthu zimene sizingathe kugulidwa ndi ndalama.

*Masalimo 119:14, 72, 127*

*Mlaliki 4:6*

*Miyambo 16:16*

*Mlaliki 5:12*

*Miyambo 16:8; 28:6; Masalimo 37:16*

*Mateyu 16:26*

Pa Mlaliki 2:4-11, Solomo akukamba za chuma. Kodi maonedwe ake anali otani pamene anali kupeza zinthu ndi chuma? Kodi chitsiriziro chake chinali chotani atatha kupeza zonse zimene anazikhumba?

---

---

---

---

---

Werengani *Mateyu 6:25-34* ndi *Afilipi 4:19*. Mulungu akulonjeza kupereka zosowa zanu za kuthupi komanso kuuzimu. Komabe, ndi chinthu chofunikira kukhala odziwa za kusiyana pakati za zofuna ndi zosowa. Fananizani ndime ziri m'musizi ndipo mulembe zitsanzo za zosowa ndi zofuna m'moyo wanu.

**ZOSOWA:**

*Yakobo 2:15-16; Ahebri 4:15-16; Marko 2:25*

*Tchulani zina mwa zosowa....*

---

---

---

---

---

**ZOFUNA:**

*Masalimo 23:1; Miyambo 13:25; Yakobo 1:4*

*Tchulani zina mwa zofuna....*

---

---

---

---

---

## **KUPEREKA**

*Mulungu ndi Mulungu wopereka, ndipo chifuniro chake ndi choti inu muonetse chikhalidwe chake popereka. Ndi zinthu zofunikira kuti mumvetsetse kuti Mulungu ndiye mwini wake wa chinachirichonse, ndipo samafuna ndalama zanu. M'mene inu mumaperekera zimaonetsa kukura kwanu monga okhulupirira. Kupereka ndi chochitika cha chikhulupiliro komanso kulambira, ndipo zimaonetsa chikondi chanu pa Mulungu ndi utumiki wake. Phunziro iri likuthandizani kuti mumvetse udindo wanu poyang'anira moyo ndi zimene muli nazo.*

### **Mfundo yofunikira:**

*Kupereka koona kwenikweni monga mwa Chipangano Chatsopano kumakhudzana ndi kuchotsa ulamuliro wanu pa zonse za m'moyo wanu ndi zinthu zanu ndikupereka ulamuliro kwa Yesu Khristu.*

#### **NDIME ZA PAMTIMA:**

*“Yense acite monga anatsimikiza mtima, si mwa cisoni kapena mokakamiza, pakuti Mulungu akonda wopereka mokondwerera.” – 2 Akorintho 9:7*

*“Pakuti kumene kuli cuma cako, komwe udzakhala mtima wakonso..” – Mateyu 6:21*

## **KODI MULUNGU AMAFUNA INU KUTI MUPEREKE CHIFUKWA CHIYANI?**

### **MFUNDO YOFUNIKIRA MUPHUNZIRO ILI!**

Chirichonse chimene muli, komanso chimene mulinacho ndi za Mulungu. Iye samafuna kapena kusowa ndalama yanu. Mulungu akufuna inu! Cholinga cha kupereka kwa chipangano chatsopano ndi kupereka ulamuliro wonse wa moyo komanso chuma chanu kwa Yesu Khristu. Ngati akhala ndi ulamuliro wonse pa moyo wanu, iyenso amakhala ndi ulamuliro pa chuma chanu. Momwe mumaperekera zimawonetsera momwe mumakhulupilira Mulungu kufukira zosowa zanu za tsiku ndi tsiku.

*“Mulungu amene analenga dziko lapansi ndi zonse ziri momwemo, Iyeyo, ndiye mwini kumwamba ndi dziko lapansi, sakhala m'nyumba zakacisi zomangidwa ndi manja; satumikidwa ndi manja a anthu, monga wosowa kanthu, popeza iye mwini apatsa zonse moyo ndi mpweya ndi zinthu zonse;” – Macitidwe 17:24-25*

*“Iye amene akhulupirika m'cacing'onong'ono alinso wokhulupirika m'cacikuru; ndipo iye amene ali wosalungama m'cacing'onong'ono alinso wosalungama m'cacikuru. Cifukwa cace ngati simunakhala okhulupirika m'cuma ca cosalungama, adzakhulupirira inu ndani ndi cuma coona?” – Luke 16:10-11*

### **LL. Kupereka kumakutsogoleraninso pa kuchotsa kuyang'ana pa zinthu za m'dziko ndi cholinga choti muikize pa zinthu zamuyaya..**

*“Musadzikundikire nokha cuma pa dziko lapansi, pamene njenjete ndi dzimbiri ziononga; ndi pamene mbala ziboola ndi kuba: 20koma mudzikundikire nokha cuma m'Mwamba, pamene njenjete kapena dzimbiri siziononga, ndipo mbala siziboola ndi kuba; 21pakuti kumene kuli cuma cako, komwe udzakhala mtima wakonso..”  
– Mateyu 6:19-21*

**MM. Kupereka kumabweretsa mantha a pa Ambuye mwa inu nokha, chifukwa mukuonetsa kuti chinthu chanu choyambirira ndiko kulemekeza Mulungu..**

*“Ndipo muzidye pamaso pa Yehova Mulungu wanu, m'malo m'mene asankhamo iye, kukhalitsamo dzina lace; limodzi la magawo khumi la tirigu wanu, la vinyo wanu, ndi la mafuta anu, ndi oyamba kubadwa a ng'ombe zanu ndi a nkhosa ndi mbuzi zanu; kuti muphunzire kuopa Yehova Mulungu wanu masiku onse..” – Deuteronomy 14:23*

**NN. Kupereka kumakhazikitsa kudalira Mulungu chifukwa inu mwakhulupirira lye kuti ndiye amene apereke zinthu zanu ngakhale za mtsogolo..**

*“Lemekeza Yehova ndi cuma cako, Ndi zinthu zako zonse zoyambirira kuca; Motero nkhekwe zako zidzangoti the, Mbiya zako zidzasefuka vinyo..” – Miyambo 3:9-10*

## **KODI MULUNGU AKUFUNA KUTI MUPEREKE KUTI?**

**B. Poyambirira khalani okhazikika pa zopereka zanu potsata ndondomeko ya pa mpingo wanu wa pamalo**

Chinthu choyambirira kuchidziwa pa kupereka kumene baibulo likufotokoza ndi kupereka kudzera mu mpingo wanu wapamalo chifukwa Mulungu anasankha mpingo umenewo kuti augwiritse ntchito ndi kukwanitsa ntchito yofikira anthu onse pa dziko lapansi. Ndi chinthu chofunikira kumvetsetsa kuti kupereka kwina kulikonse kunjika kwa mpingo wanu sikuyenera kusokoneza kupereka kwanu monga mwa nthawi zonse ku mpingo wanu. Ndi chinthu chofunikanso kusamalanso kuyang'anitsitsa za kupereka kwanu pa zifukwa zimene ziri za muyaya.

**1 Akorinto 16:1-2**

**B. Atsogoleri a mumpingo wanu ali ndi udindo wokhala oyang'anira zinthu bwino.**

Atsogoleri a pa mpingo panu ali ndi udindo oyang'anira bwino anthu a mumpingo, komanso kusamala ntchito ya Ambuye. Monga membala wa mpingo wa pamalo, inu muyenera kuona za m'mene zinthu za pa mpingo zikugwiirira ntchito, ndipo muyeneranso kukhulupirira utsogoleri wanu kuti ayanang'anire bwino zinthu zonse mwa nzeru.

**2 Akorinto 8:20-22**

## **KODI MULUNGU AKUFUNA INE KUTI NDIPEREKE MOTANI??**

Mu kalata wake wachiwiri ku mpingo wa ku Korinto, mtumwi Paulo anagwiritsa ntchito mipingo yaku Makedoniya monga chitsanzo pa za m'mene kupereka koyenera kwa baibulo kumayenera kukhalira kwa okhulupirira a mu Chipangano Chatsopano. Umboni wokhudza za m'mene mipingo yaku Makedoniya inaperekerana ndi phunziro lalikuru limene okhulupirira onse ayanera kuphunzira.

F. Kufunitsitsa kwanu kupereka ku utumiki wa Mulungu ndi chinthu chofunikira kwambiri kusiyana ndi kuchuruka kapena kuchepa kwa chopereka chimene inu mukhonza kupereka.

*a. 2 Akorinto 8:1-3*

G. Kupereka kwanu kuyenera kuyamba ndi kudzipereka nokha kwa Ambuye ndi kwa anthu.

*a. 2 Akorinto 8:4-5*

H. Kupereka kumakulitsa kuchisomo pamenenso mukula mu ubale ndi Mulungu.

*a. 2 Akorinto 8:6-7*

I. Kupereka kumaonetsa kuchuluka kwa chikondi chanu pa Mulungu, mpingo komanso utumiki wake.

*a. 2 Akorinto 8:8-9*

J. Kupereka kwanu kukhale molingana ndi m'mene Mulungu wakudalitsirani. Simuyenera kufananiza mulingo wa kupereka kwanu ndi m'mene anthu ena aperekeru.

*a. 2 Akorinto 8:10-12*

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi mukupereka mokhulupirika kudzera mumpingo wanu wapamalo?

Kodi kupereka kwanu kwa Ambuye kwasintha bwanji maonedwe anu a kufunika kwa ntchito ya Mulungu?

Kodi munayamba mwalorapo kupereka kwa munthu wina kusintha maperekedwe anu?

## **KODI MULUNGU AKUFUNA KUTI INU MUPEREKE CHIYANI?**

D. Pali mitundu itatu ya zopereka imene inakambidwa mu malemba a Chipangano Chakale.

### **4. Zachikhumi**

Chachikhumi ndi gawo limodzi la pa magawo khumi limene munthu wapeza limene limachotsedwa pa zonse zimene wapeza. Izi zinaperekedwa kwa Mulungu ngati chikumbutso chifukwa lye ndi amene amatipatsa zimene tirinazo, komanso kuonetsa kuti Mulungu ndiye amene amakhala koyambilira.

**Malaki 3:10; Deuteronomo 26:2, 10**

**5. Zoperera zaufuru**

Kuonjezera pa zachikhumi, zopereka zaufuru zinaperekedwa ndi anthu a Mulungu zothandizira pa zosowa zimene zikhonza kupezeka pakati pa mpingo. .

**Exosodo 25:1-2**

**6. Zopereka za msembe**

Izi ndi zopereka za mphatso zimene zimakhala ngati nsembe zimene operekayo wafunitsitsa kudzipereka motero. Inali ngati nsembe imene munthu amakhonza kupereka mwa kufuna kwake monga choikiza mu utumiki wa Mulungu.

**3 Samueli 24:21-25**

- E. **Monga okhulupirira wa mu Chipangano Chatsopano, kupereka kwanu kuyenera kukhazikika pa mfundo za baibulo pamene mukhazikitsa chozolowezi chakupereka m'moyo mwanu.**

*“Pakuti zonse zinalembedwa kale zinalembedwa kutilangiza, kuti mwa cipiriro ndi citonthozo ca malembo, tikhale ndi ciyembekezo.” – Aroma 15:4*

**4. Perekani nthawi zonse kuti muthandize ntchito yoyendetsa mpingo wa pamalo.**

Monga m'mene anthu a M'chipangano Chakale amabweretsera chakhumi kuthandizira ntchito ya utumiki wa Mulungu, inunso muyenera kuika mulingo winawake umene inu mukhonza kutsatira popereka nthawi zonse. Mphatso zimenezi zimathandizira kupereka ku ntchito zoyendetsera zinthu zina pa mpingo, kulipira ogwira ntchito, ndi kuthandizira zinthu zina pa utumiki.

**1 Akorinto 9:14; 1 Timoteo 5:17-18**

**5. Perekani molowa manja kuti muthandizire ntchito zina zapadera ndi mautumiki mu mpingo.**

Monga m'mene anthu a Mulungu anali kuperekerazopereka kuthandizira ku zosowa zapaderadera, inunso muyenera kukhala okonzeka kupereka panthawi imene pali zosoweka mu mpingo wanu. Mphatso zimenezi zimathandizira zosowa zamamembala amene ali mu mpingo amene sangathe kudzithandiza okha, komanso kuthandiza ntchito zina zapaderadera za pampingo zimene atsogoleri aziona kuti zigwiridwe.

**Machitidwe 11:27-30; 1Timoteo 5:3, 9-10, 16**

**6. Perekani nsembe zanu pothandizira utumiki.**

Monga m'mene anthu a Mulungu anali kuperekerazopereka monga nsembe kuti zithandizire utumiki, inunso muyenera kukhala okonzeka kupereka kuthandizira ntchito ya utumiki kuti mpingo ukhonza kutumiza anthu a mishoni ndi kuwavomereza kuti akatumikire. Mphatso zimenezi zimathandiza atumiki a mishoni kupita malo amene inu simungathe kupitako.

**Afilipi 4:15-19**



## **F. Mulungu sanalamulire inu kuti mupereke ndalama ina yake yokhazikika**

Mulungu anapereka ufulu kwa munthu kuti akhonza kupereka mwina mulimonse. Kupereka kumene Chipangano Chatsopano chikukamba kumagwirizana ndi nkhani yokura ndi kukhwima mwa Khristu, kusiyana ndi nkhani ya ndalama. Mulungu amafuna inu atunthu. M'mene inu mumaperekera zimaonetsera kuya kwa wuzimu mukuyenda kwanu ndi Mulungu. Munsimu muli mfundo zina zimene mukhonza kutsatira pamene mulingalira za mulingo oti mupereke nthawi zonse kudzera ku mpingo wanu:

### **7. Pangani dongosolo labwino la nthawi yanu, utumiki wani, komanso chuma chanu moyang'anira pa kupereka.**

Okhulupirira ambiri amakhala ndi mavuto pa kupereka nthawi zonse chifukwa amalephera kukonzekera bwino kupereka.

#### ***2 Akorinto 9:1-4***

### **8. Lingalirani kuti ndi ndalama zingati zimene inu mukhonza kupereka musanafike ku tchalitchi.**

Kupereka kwanu kwayenera kukhala pakati pa inu ndi Mulungu. Ngati mudikira kuti mukafike kutchalitchi, ndi zotheka kuti kupereka kwanu kukhonza kusalongosoka mwina potengeka ndi kupereka kwa anthu ena.

#### ***2 Akorinto 9:5***

### **9. Kumbukirani lamulo lobzala ndi kututa.**

Inu simuyenera kupereka ndi chiyembekezo choti mulandire phindu pa mapeto pake. Komabe Mulungu analonjeza kudalitsa anthu opereka mokhulupirika. Pamene mudzionetsa nokha kukhala okhulupirika ndi zimene Mulungu wakupatsani, lye adzakudalirani ndi kukupatsani zinthu zina zochuluka.

#### ***2 Akorinto 9:6***

### **10. Kupereka kwanu kudzichokera mu mtima umene uli wofuna komanso kukonzeka kupereka.**

Kodi inu mukupereka kwa Mulungu chifukwa choti muyenera kutero, kapena mukufuna kubweza zake za Mulungu?

#### ***2 Akorinto 9:7***

### **11. Mulungu adzakupatsani zosowa zanu.**

Pamene mukupereka kuthandiza ku ntchito yofalitsa uthenga monga lamulo lalikuru limene timapanga nalo ophunzira pa dziko lonse lapansi, Mulungu adzaonetsetsa kuti muli nazo zinthu zokwanira kuti mukhonze kuthandiza kukwaniritsa lamulo lalikuru limeneli kudzera ku mpingo wanu.

#### ***2 Akorinto 9:8***

### **12. Mulungu adzalemekezedwa kudzera mu kupereka kwanu.**

Chikhalidwe chenicheni china cha Mulungu ndi kupereka. Iye anakupatsani mphatso yaikuru kwambiri imene iri chipulumutso kudzera mu imfa, kuikidwa m'manda komanso kuuka kwa Ambuye Yesu Khristu. Pamene mupereka molingana ndi mfundo za

m'baibulo, mudzakhala monga mwa chikhalidwe cha Yesu Khristu m'moyo wanu, ndipo Mulungu adzalemekezeka kudzera mwa inu.

## 2 Akorinto 9:9-15

### ZOKAMBIRANA:

Kodi mwakonzetsera nthawi yanu ndi chuma chanu kuti mukhale womasuka kuti mukhoza kukhala womasuka kupereka mwapafupifupi?

Kodi mwakonda ndalama yapadera imene mumapereka pafupipafupi?

Kodi Mulungu akulandira ulemu kudzera mukupereka kwanu?

## KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA

1. Tchulani zifukwa zitatu zimene Mulungu akufuna inu kuti mudzipereka.

a. \_\_\_\_\_

b. \_\_\_\_\_

c. \_\_\_\_\_

2. Kodi ndi chifukwa chiyani kuri kofunikira kuti inu poyamba muyang'anitsitse za ndondomeko yaku mpingo kwanu popereka?

\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_

3. 2 Akorinto 8:1-2 ikutiphunzitsa kuti okhulupirira a ku Makedoniya anali odzipereka pa kupereka. Tchulani zitsanzo zisanu zimene ife tingaphunzire za m'mene anali kuperekerera.

a. \_\_\_\_\_

b. \_\_\_\_\_

c. \_\_\_\_\_

d. \_\_\_\_\_

e. \_\_\_\_\_

4. Tchulani mfundo zitatu za m'baibulo zimene inu mukhonza kuyamba kuzitsata m'moyo mwanu pamene mukukhala ndi chizolowezi cha kaperekedwe pamoyo wanu.

a. \_\_\_\_\_

b. \_\_\_\_\_

c. \_\_\_\_\_

5. **Kodi Mulungu mu Chipangano Chatsopano akunena mulingo okhazikika wa kuchuruka kwa ndalama zimene munthu akhonza kupereka? Chifukwa chiyani?**

---

---

---

6. **Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?**

---

---

---

#### **KUPHUNZIRA ZA BAIBULO PAWEKHA**

**Mulungu anaitana mtundu wa Israyeli kuti abweretse zopereka pothandizira kumanga chihema pamene iwo anali mu chipululu. Werengai Ekisodo 35 ndipo mulembe zina mwa njira zimene anthu anapereka zimene si ndalama. Kodi ndime imeneyi ikukamba zotani za mitima ya anthu pamene anapereka. Kodi ndi njira zina ziti osati ndalama zimene inu mukhonza kupereka ku utumiki wa Mulungu?**

---

---

---

---

**Werengani Luka 6:38, ndipo tchulani malonjezo a Mulungu okhudza za kupereka.**

---

---

---

**Mu *Luka 21:1-4*, Yesu akufananiza za ndalama zimene mayi wamasiye anapereka poyerekeza ndi zimene bambo wina wachuma anapereka mu malo opereka mu kachisi. Kodi Yesu ananena chiyani zokhudza chopereka cha mzimayi uja? Kodi Yesu anati chiyani zokhudza kusiyana kwa kupereka kwa mzimayi uja ndi bambo wachuma uja?**

---

---

---

**Mu Machitidwe 2 timawerenga za anthu ambiri amene anayenda mitunda italiitali pokakhala nawo pa phwando la pentekoste. Atatha kumva uthenga wabwino, ambiri anavomereza Khristu monga Mpulumutsi. M'malo mopita kunyumba, anasankha kukhala mbali imodzi ya mpingo wa ku Yerusalemu. Izi zinabweretsa vuto lalikuru lokhudza zachuma, ndipo anthu ambiri mu mpingo watsopano anali ndi vuto lolephera kupereka zinthu zokwanira pothandizira maanja awo. Werengani Machitidwe 4:34-37. Kodi anadzipereka motani pa kupereka? Kodi mphatso zawo anazitenga kuti? Kodi ndi ndani amene anali ndi udindo wogawa zimene iwo anabweretsa?**

---

---

---

---

---

---

---

---

## 15. NTCHITO NDI OLEMBA NTCHITO

*Mulungu adzakutsogolerani kuti mugwiritse ntchito udindo wanu ku malo amene mumagwira ntchito monga malo autumiki amene mungafikire anthu otaika ndi uthenga wabwino wa Yesu Khristu. Ntchito yanu imakupatsani mwayi oti mupange maubale ndi anthu ena amene inu simukanatha kukumana nawo. Ndi chinthu chofunikira mu kukula kwanu kwa moyo uzimu kuti mumvetsetse za deraa la udindo uwu mogwirizana ndi mau a Mulungu.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*MWAYI*

**Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Kodi maonedwe anga akhale otani pa ntchito komanso kwa ondilemba ntchito?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kukuthandizani inu kuti munthu wolembe ntchito anthu kapena olembedwa amene Mulungu akufuna kuti mukhale ndi cholinga chokwaniritsa utumiki wake ku malo anu wokugwira ntchito.*

**The key point of this lesson:**

*Kuti inu muone ntchito yanu monga malo a utumiki amene Mulungu wakupatsani ku ulemerero ndi utumiki wake.*

**NDIME ZA PAMTIMA:**

*“Ndipo amene aliyense afuna kukhala woyamba mwa inu adzakhala kapolo wa onse. Pakuti ndithu, Mwanawa munthu sanadza kutumikidwa, koma kutumikira, ndi kuepreka moyo wace dipo la kwa anthu ambiri.”*

*– Marko 10:44-45*

# MULUNGU WAKUITANANI KU NTCHITO YAKE

---

Ndi chinthu chofunikira kumvetsa kuti kuitana kwa Mulungu m'moyo mwanu sakuitana inu ku udindo wapaderadera, koma ku ntchito yake. Mulungu wakupatsani inu utumiki wa kuyanjanitsa dziko kwa Khristu, komanso ntchito yanu ndi njira imodzi imene inu mukhonza kuthandizira kukwaniritsira utumiki umenewo.

*“Koma zinthu zonse zicokera kwa Mulungu pamene anatinyanjanitsa kwa Iye yekhal mwa Khristu, natipatsa utumiki wa ciyanjanitso; ndiko kunena kuti Mulungu anali mwa Khristu, ali nkuyanjanitsa dziko lapansi kwa Iye yekha, osawawerengera zolakwa zao, ndipo anaikiza kwa ife mau a ciyanjanitso.” – 2 Akorinto 5:18-19*

## **D. Maitanidwe anu ndi ntchito yanu ndi kutumikira Yesu Khristu ndi moyo wanu wonse.**

*Aefeso 4:1*

## **E. Mulungu akuyembekeza kuti inu mutenge nao mbali mu ntchito yake yofikira anthu otayika a dziko lino ndi uthenga wabwino.**

*Luka 19:10; Luka 10:1-2*

## **F. Mulungu wakuitanani ndi kukulamulirani kuti mukhale m'moyo umene ndiwodzipereka pa kupanga ophunzira a Yesu Khristu.**

*Mateyu 28:18-20*

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi chinthu chimene chimatenga gawo loyambirira m'moyo mwanu lero ndi chiayani, ntchito yanu kapena ntchito ya Mulungu?

Kodi inu mukudzipereka bwanji ku ntchito yotuta m'munda wa Mulungu?

Kodi ntchito yofikira anthu ena ndi uthenga wabwino imakulemetsani?

### **MFUNDO YOFUNIKIRA MU PHUNZIRO IRI!**

Inu muyenera kuona ntchito yanu monga malo a utumiki amene Mulungu wakupatsani ku utumiki ndi ulemerero wake. Pakukhala pamenepo, muyenera kulakhala olumikizika ndi anthu amene akufuna ubale ndi Yesu Khristu. Pamene mutenga ntchito yanu monga malo a utumiki, mwina mukhonza kukhala anthu osakondwera kapena osakhutitsidwa ndi ntchito yanu. Mulungu wakuikani inu pakati pa anthu otaika monga kuunika mu dziko la m'dima kuti mukaimire Yesu Khristu. Cholinga chanu chenicheni chikhale pa anthu amene inu mukuwatumikira kusiyana ndi maudindo a pa ntchito amene inu muli nawo.

# NTCHITO YANU NDI MWAYI WA UTUMIKI

---

**Amene mumagwira nawo ntchito ndi mwayi wanu waukuru umene muli nao wokumana ndi anthu otaika.**

Inu muyenera kumvetsa kuti mwa chikhalidwe anthu otaika samafuna Mulungu.

*Aroma 3:10-11*

**A. Iwo amene mukugwira nawo ntchito ali ndi mwayi oona moyo wanu monga umboni wa tsiku ndi tsiku wa chisomo ndi chikondi cha Mulungu.**

Moyo wanu mwina ukhonza kukhala umboni oona wokhawo wa Yesu Khristu umene ogwira nawo ntchito akhonza kuona.

*Tito 2:12; Afilipi 2:12-16*

## **ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu mumatenga ntchito ngati malo oti mupangire utumiki, kapena ndi njira imodzi yopezera malipiro basi?

Kodi mukufunafuna mwayi kuti mugawane ndi ogwira nawo ntchito anzanu uthenga wabwino?

Kodi wogwira nao ntchito anzanu amadziwa kuti ndi mkhristu?

# NTCHITO YANU IMATHANDIZIRA UTUMIKI WANU

---

**A. Utumiki woyamba ndi banja lanu.**

Ndi udindo wanu kuti mupeze ndalama zokwanira kuti mukhale ndi moyo wabwino popereka zofunikira ku banja lanu.

*1 Timoteo 5:8; 2 Atesalonika 3:10*

**B. Utumiki wachiwiri uli ku banja la mpingo wanu.**

Kupeza ndalama zabwino zimakupangitsani inu kuti mukhale ndi zinthu zoyenerenza kutumikira ku banja lanu la uzimu.

*Agalatiya 6:10*

**C. Utumiki wanu wachitatu ndiko kufikira anthu otaika ndi uthenga wabwino.**

Ndalama zimene mumalandira zimakupangitsa kuti mukhale ndi zinthu zofunikira kuti muikize uthenga wabwino mwa anthu.

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi ntchito yanu imapereka zosowa ku banja lanu?

Kodi ndi njira zina ziti zimene mungagwiritse ntchito zinthu zanu kufikira anthu otaika ndi uthenga wabwino?

## **KODI MUYENERA KUKHALA OLEMBEDWA NTCHITO OTANI?**

**A. Muyenera kutumikira ku malo antchito ngati Yesu Khristu ndi amene wakulembani ntchito.**

Posatengera zotopetsa za kuntchito, muli ndi udindo woti mukhale kuunika kwa Yesu Khristu nthawi zonse.

*“Akapolo inu, mverani m’zonse iwo amene ali ambuye monga mwa thupi, wosati ukapolo wa pamaso, monga okondweretsa anthu, komatu ndi mtima wakulinga kumodzi, akuopa Ambuye. Ciri conse macicita, gwirani ntchito mocokera mumtima, monga kwa Ambuye, osati kwa anthu ai;” – Akolose 3:22-23*

**B. Inu muyenera kuchita mwa kuthekera kwanu ndi kulimbika kuti iye amene anakulembani ntchito apambane.**

Malo amene mumagwira ntchito sanangokhala kuti apere mwayi wantchito kwa inu; nthawi zonse ayenera kuti adzipanga phindu kuti mukhalebe pantchito. Mulungu adzagwira ntchito mwa inu kuti adalitse ndi zinthu amene anakulembani ntchito, ndipo adzagwira ntchito kudzera mwa inu kuti atumikire mwa uzimu kwa iwo ogwira nawo ntchito.

*“Ciri conse dzanja lako licipeza kucicita, usacite ndi mphamvu yako; pakuti mulibe ntchito ngakhale kulingirira ngakhale kudziwa, ngakhale nzeru, kumanda ulikupitako.” – Mlaliki 9:10*

**C. Inu muyenera kukhazikika pa ntchito yanu osati ntchito ya anthu ena.**

Musalore kuti zolakwitsa za wina kapenanso kusagwira ntchito bwino kwake kuti kukukhudzeni kuti potero mukakhale mboni yabwino za Yesu Khristu kudzera mau komanso m’moyo wanu.

*“Ndi kuti muyesetse kukhala cete ndi kucita zainu eni ndi kugwira ntchito ndi manja anu, moga tinakuuzani; kuti mukayende oona mtima pa iwo akunja, ndi kukhala osasowa kanthu.” – 1 Atesalonika 4:11-12*



## D. Inu muyenera kukhala ndi ulemu weniweni pa malo amene mukugwira ntchito ndi atsogoleri ake.

*“Akapolo amvere Ambuye ao a iwo okha, nawakondweretse m’zonse; osakana mau ao; osatopa pa izo, komatu aonetsere cikhulupiriko conse cabwino; kuti akakometsere ciphunzitso ca Mpulumulutsi wathu Mulungu m’zinthu zonse.” – Tito 2:9-10*

- 1. Perekani ulemu ulamuliro wa iwo amene anakulembani ntchito– “osati kuyankha mobwezera”**  
Kusankha kumvera ulamuliro waiwo amene anakulembani ntchito, ngakhale mu nthawi yosagwirizana, zidzakupatsani mwayi woti muchitire umboni za Ambuye Yesu Khristu.
- 2. Perekani ulemu ku katundu wa iwo amene anakulembani ntchito – “osati kuba”**  
Samalirani katundu wa pamalo pamene mukugwirapo ntchito, ndipo musatenge katundu amene siali wanu.
- 3. Perekani ulemu ku nthawi ya iwo amene anakulembani ntchito– “kuonetsa kudalirika konse”**  
Khalani okhulupirika kuchita ntchito ndi kulimbika molingana ndi ndondomeko za nthawi zimene anakupatsani.

### ZOKAMBIRANA:

Kodi inu mumaona kumvera iwo amene anakulembani ntchito ngati Yesu kukhala kovuta?

Kodi inu ndi wogwira ntchito wovuta pa malo amene inu mumagwira?

Kodi umboni wanu wa Yesu wakhudzika bwanji ndi m’mene muliri ngati wogwira ntchito?

## KODI INU MUYENERA KUKHALA OLEMBA NTCHITO OTANI?

### A. Khalani ndi mulingo wabwino ndi ziyembekezo zokomera aliyense ogwira ntchito.

Khalani ndi mulingo wokomera aliyense ogwira ntchito ndipo muonetse kuti muli ofunitsitsa kusunga mulingo umenewo kwa aliyense mofanana.

*“Ndipo ambuye inu, muwacitire zomwezo iwowa, nimuleke kuwaopsa; podziwa kuti Ambuye wao ndi wanu ali m’Mwamba, ndipo palibe tsankhu kwa Iye.” – Aefeso 6:9*

## B. Perekani malipiro abwino komanso mosakondera kwa ogwira ntchito molingana ndi maudindo awo.

Inu musakhale otengeka ndikuchita bwino kwa bizinezi yanu kapena phindu la inu nokha kufikira kuiwala zosowekeza za iwo amene akugwira ntchito. Pamene mutenga zofuna za anthu ogwira ntchito kukhala zofunikira, iwowo adzalemekeza utsogoleri ndi malo omwe akugwira ntchito.

*“Ambuye inu, citirani akapolo anu colungama ndi colingana; podziwa kuti inunso muli naye Mbye m’Mwamba.” – Akolose 4:1*

## C. Nthawi zonse khalani ndi mtima wonga wa mtumiki.

Inu muyenera kutsogolera ogwira ntchito, osati kuwalamulira mwankhanza. Muli ndi udindo woti mutsogolere ogwira ntchito amenewa ku chikhulupiriro mwa Yesu komanso kuti bizinezi ipindule.

*“Ndipo Yesu anawaitana, nanena nao, Mudziwa kuti iwo amene ayasedwa ambuye amitundu ya anthu amacita ufumu pa iwo; ndipo akuru ao amacita ulamuliro pa iwo. Koma mwa inu sikutero ai; koma amene aliyense afuna kukhala wamkuru mwa inu adzakhala mtumiki wanu; Ndipo amene aliyense afuna kukhala woyamba mwa inu adzakhala kapolo wa onse. Pakuti ndithu, Mwanawa munthu sanadza kutumikidwa, koma kutumikira, ndi kuepreka moyo wace dipo la kwa anthu ambiri.” – Marko 10:42-45*

### ZOKAMBIRANA:

Kodi anthu ogwira ntchito amadziwa zimene mumayembekezekezera mwa iwo?

Kodi utsogoleri wanu ukupereka mwayi kwa ogwira ntchito kuti aone Yesu Khristu mwa inu?

## INU MUDZAKUMANA NDI MIKANGANO PA NTCHITO

### YANU

## D. Ntchito yanu ikhonza kulimbana ndi zinthu zina za uzim zoyambirira.

Uwu ndi mkangano umene umafuna inu kuti mufune chitsogozo cha Mulungu kuti mukhonze kudziwa zinthu zimene zingayambirire. Inu simungasiye ntchito yanu, kapena kutenga masiku a tchuthi ku ntchito chifukwa cha mikangano yaying’ono; komabe musagwiritse ntchito monga pothawira ndi kukana kugwira ntchito ya mpingo kapena ya moyo wanu wa uzimu.

*Miyambo 11:1; Yakobo 1:8*

## E. Ntchito yanu ikhonza kulimbana ndi mfundo zina za baibulo.

Pakhonza kukhala nthawi zina zimene okulembani ntchito akhonza kukutumani kuti mugwire ntchito ina yake yosemphana ndi mau a Mulungu. Inu muyenera kupanga ganizo

logwirizana ndi baibulo limene liri lolondola, komanso dzitetezeni nokha ku mayesero amene mukhonza kutengeka ndi zochitika za uchimo komanso maonedwe ena pa zinthu zomwe zakuzungulirani.

***Aefeso 5:3-12***

**F. Mukhonza kukhalanso ndi mikangano ndi anzanu ogwira nawo ntchito.**

Pamene ogwira ntchito ena siali okhulupirira, inu muyenera kusankha mfundo za m'baibulo pothana ndi mikangano komanso ndondomeko ya zinthu zimene malo anu ogwira ntchito amafuna. Inu muyenera kusankha kukhala opanda banga ndi odzichepetsa mu nyengo ina iriyonse kuti mikangano yonse ikonzedwe.

***Mateyu 18:15-17***

**D. Inu mukhonza kukumana ndi mikangano kudzera mu mazunzo.**

Mu nthawi zambiri mazunzo m'malo a ntchito si kanthu kakakuru potengera ndi zotsatira za kusayenda bwino ndi Ambuye kwa okhulupirira. Komabe, pakhonza kukhala nthawi zina zimene mumakumana ndi zotsutsa chifukwa chakuti inu mwakhulupirira Khristu kwambiri. Njira yabwino yoyankhira ku mazunzo ndi kupereka mavuto onse kwa Ambuye komanso kuthana nawo mu njira imene inuyo mukhala opanda banga.

***1 Petro 2:18-23; 3:16-17***

**E. Inu mukhonza kukhala ndi mikangano chifukwa cha mwayi wanu woti mupite patsogolo pa ntchito yanu.**

Mulungu akhonza kugwiritsa ntchito udindo wanu waukuru ndi malipiliro anu ambiri ku ulemelero wake. Komabe, ndalama zambiri kaya udindo wabwino sizinthu zimene nthawi zonse ziri zabwino kwa inu. Udindo wina uliwonse watsopano ukhonza kukhala chotchinga ku nthawi yanu komanso ku utumiki wa Yesu Khristu. Ndi chinthu chabwino kutsimikizika mtima kuti inu mukhonza kukhala okhulupirika ndi udindo waukuru, komanso kuti simudzilora nokha kukhala otanganidwa kwambiri.

***Luka 16:10-12; Yakobo 3:1***

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu muli pa mkangano ndi anzanu ogwira nawo ntchito ku ntchito kwanu?

Kodi munayamba mwakhala ndi nyengo yosankha pakati potumikira Mulungu kapena ntchito yanu?

## **KODI INU MUKUFUNA NTCHITO INA?**

---

**A. Kodi inu mwapemphera ndi kufuna chitsogozo cha Ambuye?**

Mulungu adzakuvumbulutsirani dongosolo lake kwa inu kudzera mu mau a Mulungu komanso pemphero. Zinkhonza kukhala kuti ndi ganizo labwino kulemba zam'mene Mulungu akutsogolerani ndi cholinga choti mukhonza kubwerera ndi kunikiranso.

**B. Kodi munayamba mwapeza uphungu kuchokera kwa mkhristu wokhwima ?**

Kufuna kapena kuyang'ana ntchito yabwino ikhonza kukhala nkhani yovuta. Ndi chnthu chanzeru kuti mufunse uphungu wochokera m'baibulo wochokera kwa mkhristu wokhwima amene inu mumalemekeza.

*Miyambo 11:14*

**C. Kodi mwayi wa ntchito yatsopanoyi ukhonza kukhudza banja lanu motani?**

Nthawi zambiri, ntchito zathu zimakhudza nthawi yathu imene ife timaipereka ku maanja athu. Komabe, ntchito zina zimafuna nthawi yambiri imene ikhonza kulepheretsa kuti inu mukhale ndi ubale wabwino ndi okonedwa anu komanso ana.

*Miyambo 27:23*

**D. Kodi mwayi wa ntchito yatsopanoyi ukhonza kukhudza motani zimene Muungu akuchita m'moyo mwanu?**

Pali ntchito zimene, nthawi zina, zidzatsutsana ndi kuthekera kwanu kopanga ophunzira ndi kutumikira kudzera mu mpingo wanu. Ndi chinthi chofunikira kumvetsetsa kuti Mulungu sangakutsogolereni ku ntchito imene kutsutsana kwake kuli kokhazikika.

*2 Timoteo 2:4*

**E. Kodi pali chinachake chimene mukuthawa chimene mukuyenera kukumana nacho ndi kuyesetsa kukonza?**

Mulungu nthawi zambiri amagwiritsa ntchito nyengo zovuta kuti akuphunzitseni choona chenicheni cha baibulo komanso kulimbikitsa chikhulupiriro chanu mwa Iye. Ngati mukukumana ndi mikangano ku malo anu antchito, ndi chabwino kuti mukonze mavuto amenewo musanayambe kuyang'ana mwayi wa ntchito wina. Mavuto ambiri samatha chifukwa chakuti munthu wasintha malo kapena zochitika.

*Mateyu 5:23-25*

**F. Kodi mwayi wantchito yatsopano umeneyi ukhonza kuthandiza bwanji inu kupeza mpingo watsopano?**

Ngati ntchito yatsopano ikukupangitsani kuti mupite malo ena, ndiye kuti china mwa zinthu zoyambirira ndikupeza mpingo wina woti inu mudzikhonza kutumikirako. Onaninso za phunziro la kupeza mpingo wabwino umene umatha kupanga ophunzira.

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi ntchito imene mukugwira pano ikukhudza motani nthawi yanu pa banja ndi utumiki wanu?

Kodi mufunafuna chitsogozo cha Mulungu ndi uphungu wa Baibulo pa ntchito imene mukugwira pano?

# KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA

49.Kodi ndi ntchito yanji imene Mulungu waitanira okhulupirira onse?

---

---

50.Tchulani mautumuki atatu amene ntchito yanu imathandizira.

d. \_\_\_\_\_

e. \_\_\_\_\_

f. \_\_\_\_\_

51.Fotokozani mwa mau anu kuti kodi inu muyenera kukhala ogwira ntchito wotani?

---

---

---

52.Kodi chikhalidwe chofunikira kwambiri cha anthu olemba kapena kuyang'anira ntchito ndi chotani?

---

---

53.Tchulani mitundu itatu ya mikangano imene mukhonza kukumana nayo pa malo ogwira ntchito.

a. \_\_\_\_\_

b. \_\_\_\_\_

c. \_\_\_\_\_

54.Tchulani zinthu zitatu zimene muyenera kuziganizira pamene mukufufuza ntchito yatsopano.

a. \_\_\_\_\_

b. \_\_\_\_\_

c. \_\_\_\_\_

55.Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?

---

---

---

---

---

## KUPHUNZIRA BAIBULO PAWEKHA

Werengani *Machitidwe 18:1-5* ndi *Machitidwe 20:33-35*. Mtumwi Paulo amakonza mahema kuti apeze zosowa zake, ndipo anagwiritsa ntchito yake monga njira yopangira utumiki. Kodi ndi mfundo ziti zimene inu mwaphunzira kuchokera mu ndime izi zimene mukhonza kuzigwiritsa ntchito pa ntchito yanu?

---

---

---

---

Werengani ndime ziri m'musimu ndipo mulembe chimene baibulo likunena za anthu amene anasankha kukhala a ulesi ndipo analibe mtima wogwira ntchito.

*Miyambo 18:9*

*Miyambo 21:25*

*Miyambo 19:15*

*Miyambo 22:13*

*Miyambo 20:4*

*Miyambo 26:14*

Werengani *Danieli 6*. Mu mutu umenewu, Danieli ndi m'modzi mwa olamulira mu ufumu wa Amedi ndi Aperisi. Kodi mkangano weniweni umene Danieli akukumana nawo ndi otani? Kodi Danieli anachitapo chiyani? Kodi kuyankha kwa Danieli kunakhudza bwanji mfumu ndi ufumu wonse?

---

---

---

---

---

**Werengani Genesesi 39. Yosefe anagulitsidwa ngati kapolo kwa Potifala. Kodi ndime imeneyi ikunena zotani za chikhalidwe cha Yosefe? Kodi Yosefe anachita chiyani pamene anakumana ndi mayesero?**

---

---

---

---

---

---

## 16. DZIKO LOTAIKA

*Baibulo likulamulira anthu a Mulungu kuti adzipatule ku dziko, komanso pa nthawi yomweyo tiyenera kufikira amuna ndi akazi otaika kuti amudziwe Ambuye Yesu Khristu. Pamene mukufuna kupulumutsa otaika, mudzalandira chitsutso kuchokera ku dziko chifukwa limatsutsana ndi cholinga cha muyaya cha Mulungu. Phunziro iri likhala likuyang'ana za kufunikira kwakokhala munthu wochitira umboni wa chisomo cha Yesu Khristu wobweretsa zipatso komanso wolimbana ndi chitsutso china chirichonse cha dziko.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*Utumiki*

**Funso lofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Kodi udindo wanu kwa anthu otaika ndi wotani?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kufikira otaika mosasokoneza mayendedwe anu ndi Ambuye Yesu Khristu.*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Lorani zochita za moyo wanu zionetsere chikondi chanu pa Mulungu.*

**NDIME ZA PA MTIMA:**

*“Pakuti Uthenga Wabwino sundichitsa manyazi manyazi; pakuti ulu mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu aliyense wakukhulupilira, kuyambira Myuda, ndiponse Mhelene.” – Aroma 1:16*

*“Koma ngati wina akonda Mulungu, yemweyi adziwika ndi lye” – 1 Akorinto 8:3*



# **KODI DZIKO LA ANTHU OTAIKA LIMAKUONANI BWANJI?**

## **MFUNDO YOFUNIKIRA PA PHUNZIRO IRI!**

Lorani zochita za moyo wanu zionetsere chikondi chanu pa Mulungu. M'mene inu mumakhalira zigwirizane ndi uthenga wabwino. Utumiki wanu wofikira otaika sungathe kukwaniritsika popanda umboni weniweni woona wa uthenga wabwino, komanso umboni ooneka wa kusinthika kwa miyoyo.

*“Citani zonse kopanda madandaulo ndi makani; kuti mukakhale osalakwa ndi oona; ana a Mulungu opanda cirema pakati pa mbadwo wokhotakhota ndi wopotoka, mwa iwo amene muonekera monga mauniko a m; dziko lapansi.” – Afilipi 2:14-15*

### **A. Dziko likuyang'ana kuti kuti liona ngati mumakhaladi mu chimene mumakhulupirira.**

1. Akuyenera aone chikondi chanu pa Mulungu pa m'mene inu mumakhalira moyo wanu.

**1 Akorinto 8:3**

2. Akuyenera aone kuti mumakhala moyo umene uli wolekana ndi njira za dziko. Inu muyenera kudzilekanitsa ku dziko, osati kudzilekanitsa kuti mukhale osachita chinachirichonse kapena kupanga kanthu mudzikomo.

**1 Akorinto 9:19-22; 2 Akorinto 6:14-18**

3. Akuyenera aone kuti muli omasuka ndi oona mtima mu zinthu zonse.

**2 Akorinto 8:21; Akorinto 12:17**

### **B. Dziko lidzakutsutsani chifukwa inu ndinu oimira Khristu padziko pano.**

1. Satana ndi mphamvu imene iri kuseri kwa chitsutso china chirichonse chimene mumalandira.
  - a. Iye wakhazikitsa zochitika za mdziko muno zimene ziri zotsutsana ndi ntchito ya Ambuye.

**Aefeso 2:1-3**

- b. Iye amafuna kuononga moyo wanu mwa njira imene iye angathe.

**1 Petro 5:8**

2. Inu mudzatsutsidwa chifukwa Yesu anatsutsidwa. Komabe, dziko lidzatsutsa okhulupirira amene akukhala mwa Khristu.

**Yohane 15:18-21; 2 Timoteo 3:12**

3. Inu mudzalandira kutsutsidwa mu magawo atatu akuru akuru....
- a. Anthu adzakutsutsani chifukwa ndi wosemphan ndi mau a Mulungu. Kutsutsa kwambiri kudzabwera kuchokera ku zinthu zofalitsa nkhani, zolembedwa ndi kudzera mu maphunziro.

**1 Yohane 2:15-17; 1 Yohane 3:13**

- b. Anthu otaika adzakutsutsani chifukwa inu simulinsu mbali ya banja lawo.

**Agalatiya 4:29**

- c. Anzanu, banja, ogwira nawo ntchito limodzi, ndi anthu ena amene mumayanjana nawo mu zinthu zina adzakutsutsani. Chitsutso ichi nthawi zina chimakhala chovuta chifukwa cha ubale umene umakhalapo ndi anthu amenewa.

**Marko 6:4; Yohane 1:11**

**Kodi inu mungagonjetse bwanji chitsutso chimene inu mumakumana nacho?**

1. Pewani kukangana m'mene mungathere, ndipo yankhani mofatsa bwino ndi mau ofewa.  
*"Mayankhidwe ofatsa abweza mkwiyo; Koma mau owawitsa aputa msunamo."* -  
**Miyambo 15:1**
2. Mulungu akupatseni inu mtendere ndi adani anu pamene mumukondweretsa ndi moyo wanu.  
*"Njira za munthu zikakonda Yehova, Ayanjanitsana naye ngakhale adani ace."* -  
**Miyambo 16:7**
3. Pemphererani adani anu ndi malingaliro abwino.  
*"Koma Ine ndinena kwa inu, Kondanani nao adani anu, ndi kupempherera iwo akuzunza inu;."* - **Mateyu 5:44**
4. Kondani adani anu ndi kuwathandiza kuti apeze zosowa zawo.  
*"Dalitsani iwo akuzunza inu; dalitsani, musawatemberere. Koma ngati mdani wako akumva njala, umdyetse, ngati akumva ludzu, ummwetse; pakuti pakutero udzaunjika makala a mota pamutu pace. Musagonje kwa coipa, koma ndi cabwino genietsani coipa"* -  
**Aroma 12:14, 20-21**

## **ZOKAMBIRANA:**

Kodi dziko lotaika limaona kuti inu ndi mkhristu?

Kodi inu munalandira chotsutsa china chirichonse kuchokera kwa anthu apabanja panu kapena anzanu chifukwa cha chikhulupiriro chanu mwa Khristu?

Kodi inu mumayankha motani pakakhala chitsutso?

## **KODI INU DZIKO LOTAIKA MUMALIONA BWANJI?**

Anthu, malamulo, ndi zikhalidwe za kumene inu mumakhala zimakhudzana kwambiri ndi m'mene inu mumaonera dziko lotaika. Ndi chinthu chofunikira kumvetsa kuti choonadi cha mau a Mulungu chimayenera kugwira ntchito kwa okhulupirira onse ndi zikhalidwe zonse.

### **OO. Inu muyenera kumvetsetsa za ubale wanu ndi chikhalidwe.**

1. Zikhalidwe zambiri zimakhala zosiyana ndi chiyero komanso zolinga za Mulungu.

*Tito 1:10-14*

2. Inu muyenera kukhala moyo wa umulungu pamene mukutumikira pakati pa zikhalidwe zimene inu mukukhalamo.

*Tito 2:11-14; 1 Petro 2:12*

### **PP. Inu muyenera kumvetsa za ubale wanu ndi boma.**

1. Mverani malamulo a boma lanu monga umboni kwa iwo otaika.

*1Petro 2:13-17; Aroma 13:1-5*

2. Perekani misonkho, perekani ku boma zimene ziyenera bomalo monga mwa lamulo.

*Aroma 13:6-7*

3. Pemphererani boma lanu komanso ufulu oti mukhonze kulalikira uthenga wabwino.

*1 Timoteo 2:1-4*

### **QQ. Inu muyenera kumvetsetsa ubale wanu ndi dziko lotaika.**

1. Kwanu ndi kumwamba, osati dziko lino.

***Aefeso 2:6***

2. Inu ndinu ogonera mudziko lachilendo.

***1 Petro 2:10-12***

3. Dziko lino lilibe chinachirichonse cha mtengo wamuyaya chimene lingathe kukupatsani.

***2 Petro 3:10-13***

4. Inu ndinu kazembe wa Yesu Khristu, ndipo dziko lino ndilo malo a utumiki kuti mukafikire otaika ndi uthenga wa Khristu.

***Mateyu 28:18-20; 2 Akorinto 5:18-20***

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi chikhalidwe chanu ndi boma lanu zikuthandizira bwanji popereka mwayi kuti inu mutumikire Ambuye?

Kodi ubale wanu ndi dziko wasintha bwanji kuyambira pa nthawi imene inu munapulumsidwa?

Mungathe kutchula maina a anthu m'moyo mwanu amene mukudziwa kuti ndi otaika ndipo ayenera kumva uthenga wabwino kuti apulumutsidwe?

## **KODI INU MUMAGAWA BWANJI ZA CHIKHULUPIRIRO CHANU?**

**Yesu anapanga ophunzira pakuwatsogolera kuti akalalikire.**

*“Ndipo Yesu ananena nao, Idzani pambuyo panga, ndipo ndidzakusandutsani inu asodzi a anthu. Ndipo pomwepo anasiya makoka ao, namtsata lye.” – Marko 1:17-18*

**Ngati mutsata Yesu, lye adzakutsogolerani kuti mukafunefune otaika.**

*“Pakuti Mwana wa munthu anadza kufunafuna ndi kupulumutsa, cotayikaco.” – Luka 19:10*

**A. Yambani ndi kumvetsetsa za zimene Mulungu anakuuzani.**

*“Mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse.” – Marko 16:15*

**1. Mulungu anakuuzani kuti MUKANI**

Inu simungagawe chikhulupiriro chanu popanda kupita kumene kuri otaikawo.

**2. Mulungu anakuuzani kuti mupite KUKALAKIRA UTHENGA WABWINO**

Inu simungagawe chikhulupiriro chanu popanda kupita ndi kukalalikirira uthenga wabwino.

**3. Mulungu anakuuzani kuti pitani mukalalikire uthenga wabwino kwa OLENGEDWA ONSE.**

Uthenga wabwino uyenera kupita kwa wina aliyense chifukwa Yesu anafa ndipo anadzukanso chifukwa cha aliyense.

**B. Yang’anitsitsani kwambiri pa kumvera kwanu, osati zotsatira.**

**1. Gawani uthenga wabwino chifukwa munalamulidwa kutero.**

Pamene zochita zanu zikhazikika poyankha funso loti “kodi Mulungu anandiuza kuti nditani?” m’malo mwa “Kodi zimene zitayende ndi chani?” ndiye kuti muyeza za zimene inu mungapindule potengera pa kumvera, osati zotsatira zanu.

*“Pakuti ngati ndilalikira Uthenga Wabwino ndiribe kanthu kakudzitamandira; pakuti condikakamiza ndigwidwa naco; pakuti tsoka ine ngati sindilalikira Uthenga Wabwino!” – 1 Akorinto 9:16*

**2. Musayesedwe kukhala anthu ochonjera pamene mukupereka uthenga wabwino.**

Uthenga wabwino paokha ndi wamphamvu opandanso kuupanga kuti ukome kapena kuti anthu aukhulupirire.

*“Pakuti Uthenga Wabwino sundicititsa manyazi; pakuti uti mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupira; kuyambira Myuda, ndiponso Mhelene.”*

*– Aroma 1:16*

**3. Musayesedwe kupewa kugawa uthenga chifukwa inu mukudzimva kusakonzekera.**

Mulungu wakukonzekeretsani inu kunyamula uthenga waukuru wa imfa ya Yesu Khristu, kuikidwa m’manda komanso kuuka kwake ku dziko.

*“Ndipo kulimbika kotere kwa Mulungu tiri nako mwa Kristu: si kuti tiri okwanira pa ife tokha, kuyesera kanthu monga mocokera mwa ife tokha; kukwanira kwathu kucokera kwa Mulungu” – 2 Akorinto 3:4-6*

**C. Pempherani kuti Mulungu kakutsogolereni inu pamene mukugawa za chikhulupiriro chanu.**

**1. Pempherani kuti Mulungu adzaze mitima yanu ndi kukhumba kwakuti mukhonza kuuza anthu za Yesu Khristu.**

*“Ambuye sazengereza nalolonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa.” – 2 Petro 3:9*

**2. Pempherani kuti Mulungu akupatseni mwayi wokuthandizani inu kugawa uthenga.**

*“Ndi kutipempherera ifenso pomwepo, kuti Mulungu atitsegulire ife pakhomo pa mau, kuti tilankhule cinsinsi ca Kristu; cimenenso ndikhalira m'ndende, kuti ndicionetse ici monga ndiyenera kulankhula.” – Akolose 4:3-4*

**3. Pempherani chifukwa cha kulimbika mtima pogawa uthenga wabwino khomo latseguka.**

*“Mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi yonse mwa Mzimu, ndipo pocezera pamenepo cicezerere ndi kupembedzera oyera mtima onse, ndi ine ndemwe, kuti andipatse mau m'kunditsegulira m'kamwa molimbika, kuti ndizindikiritse anthu cinsinsico ca Uthenga Wabwino, cifukwa ca umene ndiri mtumiki wa m'unyolo, kuti m'menemo ndikalankhule molimbika, monga ndiyenera kulankhula,” – Aefesos 6:18-20*

**MFUNDO YOFUNIKIRA KUDZIWA:**

Njira yokhayo yopezera makomo otseguka ndi kugogoda pa makomo otsekeka. Inu mumapeza makomo otseguka pokhala ndi anthu pa mzokambirana, komanso kuwafunsa ngati akonza kukamba za Yesu. Kodi ndi anthu angati amene akhonza kupulumuka ngati wina atawafunsa kupereka moyo? Kodi ndi anthu angati amene akhonza kupulumuka ngati akanadziwa m'mene zimakhalira?

**D. Khalani ndi ndondomeko ya m'mene mungagawire uthenga.**

Pali njira zambiri zosiyana zogawanirana uthenga wabwino, koma ndi chinthu chabwino kumvetsetsa kuti nthawi zonse uthenga udzakhala ndi imfa, kuikidwa m'manda ndi kuuka kwa Yesu Khristu.

**1 Akorinto 15:1-4**

**Njira yozolowereka yoperekerwa uthenga wabwino ndi njira imene timati “Nseu wa Aroma”.**

1. Inu muyenera kudziwa kuti ndinu otaika musanatthe kuona kufunikira kofuna chipulumutso.

*“Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemmerero wa Mulungu” – Aroma 3:23*

2. Inu muyenera kuona kuti tchimo lanu linachokera kwa Adamu, ndipo inu mwaweruzidwa kufa imfa yolekana ndi Mulungu kwa muyaya.

*“Cifukwa cace, monga ucimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa ucimo; coteri imfa inafikira anthu onse, cifukwa kuti onse anacimwa.” – Aroma 5:12*

3. Inu muyenera kuona kuti tchimo kuti likhonza kubweretsa imfa, koma Mulungu wapereka chipulumutso monga mphatso kudzera mu nsembe ya Yesu Khristu.

*“Pakuti mphototho yace ya ucimo ndi imfa; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu.” – Aroma 6:23*

4. Inu muyenera kudziwa kuti Yesu anafera machimo anu.

*“Koma Mulungu atsimikiza kwa ife cikonai cace ca mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife cikhalire ocimwa, Kristu adatifera ife” – Aroma 5:8*

5. Inu muyenera kuvomereza kuti Yesu ndi Ambuye, ndi kukhulupirira mu mtima mwanu kuti anafa ndipo anaukanso kwa akufa.

*“Kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka: pakuti ndi mtima munthu akhulupira kutengapo cilungamo; ndi m'kamwa abvomereza kutengapo cipulumutso.” – Aroma 10:9-10*

6. Inu muyenera kuitana pa dzina la Yesu kuti mupulumutsidwe nalo.

*“Pakuti, amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka.– Aroma 10:13*

## **MUKHONZANSO KUGAWA UTHENGA WABWINO POGWIRITSA NTCHITO NDIME KAPENA GAWO LA NDIME LIMODZI**

*“Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha.” – Yohane 3:16*

*“Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu; cosacokera kunchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense.” – Aefeso 2:8-9*

*“Ameneyo sanadziwa ucimo anamyesera ucimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale cilungamo ca Mulungu mwa iye.” – 2 Akorinto 5:21*

### **CHITSANZO...**

Yesu akuti njira yokhayo yopitira kwa Mulungu ndi kudzera mwa Iye. Njira yokhayo yoti munthu akhululukidwe ndi kuvomereza mwa chikhulupiriro chimene Yesu anachita kwa ife mu imfa yake, kuikidwa m'manda komanso kuuka.

*“Yesu ananena naye, ine ndinenjira, ndi coonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine.” – Yohane 14:6*

#### **Yesu ndi njira...**

Baibulo likuti anthu onse adzafa ku m'machimo awo ngati sapulumutsidwa ku chilango chimene ayanera kulandira kudzera u kukhetsedwa kwa mwazi wa Yesu Khristu. Yesu anakhala njira ku chipulumutso chanu pakufa m'malo mwanu pamtanda, kuikidwa m'manda masiku atatu ndi usiku utatu, ndi kuukanso ndi kugonjetsa tchimo ndi imfa.

#### **Yesu ndi choonadi ...**

Baibulo likuti anthu onse amakana choonadi cha chimene Mulungu ali posankha kulambira iwo eni komanso chilengedwe. Yesu ndi choonadi chimene iwo akufuna, ndipo anthu onse ayanera kulambira lye monga Mulungu woona.

#### **Yesu ndi moyo...**

Anthu onse amabadwa mu uchimo, ndipo iwo amatsutsidwa polekanitsidwa ndi Mulungu mu imfa ya muyaya mu nyanja ya moto. Iwo akusowa moyo wosatha umene umapezeka mwa Yesu Khristu.

## **E. Khalani okonzeka kugawa umboni wanu**

Chimodzi mwa chinthu chimene chimapangitsa kuti kukambirana kupitilire ndi kugawa nkhani yanu. Umboni wanu uli ndi mphamvu yaikuru kwambiri.



*“Ndipo iwo anamlaka iye cifukwa ca mwazi wa Mwanawankhosa, ndi cifukwa ca mau a umboni wao; ndipo sanakonda moyo wao kungakhale kufikira imfa.” – Chiv 12:11*

Umboni wanu umapereka zoonza za m'mene moyo wasinthira chifukwa cha uthenga wabwino. Umboni wa Paulo ku **Machitidwe 22** ndi chitsanzo chachikuru cha m'mene tikhonza kupangira umboni.

**1. Kodi inu munali wotani kopanda Khristu?**

Paulo analankhura za mtundu wake, kumene amachokera, komanso kupembedza kwake.

***Machitidwe 22:3-5***

**2. Kodi inu munakumana bwanji ndi Khristu?**

Paulo analankhura za m'mene iye anakumanirana ndi Khristu.

a. Paulo analankhura zakulowerera kwa Mulungu. Iye anakumana ndi kuwala kwa Ambuye, osati nzeru kapena kuganiza kwa munthu.

***Machitidwe 22:6***

b. Paulo analankhura za kutsutsidwa kwa tchimo.

***Machitidwe 22:7***

c. Paulo analankhura za kukumana ndi Yesu. Chipulumutso ndi cha munthu osati chipembedzo.

***Machitidwe 22:8-9***

d. Paulo analankhura za kudzipereka kwa umbuye wa Yesu.

***Machitidwe 22:10***

**3. Kodi moyo wanu wasintha bwanji?**

Paulo analankhura za m'mene Mulungu anayambira kugwira ntchito m'moyo mwake.

a. Paulo analankhura za kudzipereka kwake kwa Khristu zimene zinamupangitsa kudzipereka yekha ngati kapolo wa Khristu.

***Machitidwe 22:11-13***

b. Paulo analankhura za kulandira chitsogozo pa moyo wake.

***Machitidwe 22:14-15***

c. Paulo analankhura za kutenga makwerero ofunika pakutsata Ambuye kudzera mu ubatizo.

**Machitidwe 22:16**

d. Paulo analankhura za kukura posatengera kale lake.

**Machitidwe 22:17-20**

**4. Inu ndinu ndani mwa Khristu tsopano?**

Paulo analankhura za utumiki wake woyanjanitsa anthu otaika ndi Khristu.

**Machitidwe 22:21**

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu mukufunadi mwayi oti mutengere uthenga wabwino kwa otaika?

Muli ndi njira yoit muitsate pogawa uthenga wabwinowo?

## KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA

**56. Fotokozani kuti ndi chifukwa chiyani mumakumana ndi zotsutsa zochokera ku dziko.**

---

---

---

**57. Tchulani zinthu zinai zimene zimafotokoza ubale wanu ndi dziko. Lembaninso malemba a m'baibulo.**

k. \_\_\_\_\_

l. \_\_\_\_\_

m. \_\_\_\_\_

n. \_\_\_\_\_

**58. Mwachidule fotokozani za m'mene ndime ziri m'musimu zikhonza kuthandizira kutsutsa za chitsutso cha dziko.**

**Miyambo 15:1**

---

**Miyambo 16:7**

---

**Mateyu 5:44**

---

**Aroma 12:20-21**

---

**59.Kodi malamulo akuruakuru asanu amene tingaphunzire pogawa chikhulupiriro chathu ndi ati?**

- a. \_\_\_\_\_
- b. \_\_\_\_\_
- c. \_\_\_\_\_
- d. \_\_\_\_\_
- e. \_\_\_\_\_

**60.Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?**

---

---

---

---

## **KUPHUNZIRA BAIBULO PAWEKHA**

**Payenera kukhala kukhumba kwina mkati mwanu kuti mugawe za nkhani yaikuru ya Yesu ndi anthu ena. Werengani ndime ziri m'musimu. Ndi ndani akukambidwa mu ndimezo? Kodi wina aliyense akukamba zotani atakumana ndi Yesu?**

*Yohane 1:40-41*

---

---

*Yohane 1:45*

---

---

*Yohane 4:28-29*

---

---

*Machitidwe 9:18-20*

---

---

*Machitidwe 18:25-28*

---

**Kodi umboni wanu wasintha bwanji kuyambira panthawi imene munayamba kupanga ophunzira?**

---

---

---

---

---

**Kodi ndi ndime iti imene mumakonda kugwiritsa ntchito pogawa uthenga wabwino? Nanga ndi chifukwa chiyani?**

---

---

---

---

## 17. MPANDO WAKUWERUZA WA KHRISTU

*Baibulo likukamba momveka bwino kuti ife tonse tidzaima pamaso pa Mulungu ndi kulandira chiweruzo. Kwa mkristu, chiweruzochi chidzakhala pa mpando wakuweruza wa Khristu pamene tidzaweruzidwa molingana ndi ntchito zathu ndi utumiki wathu kwa Ambuye Yesu Khristu. Inu muyenera kyembekezera za tsiku limenero pamene mudzayankhe za m'mene munachitira kwa Yesu Khristu.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*UTUMIKI*

**Mafunso ofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Kodi ndi chain chimene ndidzafunsidwe kuyankha pa mpando wakuweruza wa Khristu?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kumupanga wokhulupirira kuti akhale oyang'anitsitsa pa zinthu zamuyaya pozindikira bwino lomwe za chimene tikhonza kudzayankha kwa Ambuye Yesu Khristu monga mtumiki wake.*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Inu mudzaweruzidwa monga mtumiki wa Yesu Khristu..*

### **NDIME ZA PA MTIMA:**

*"Pakuti ife tonse tiyenera kuonetsedwa ku mpando wa kuweruza wa Khristu, kuti yense alandire zocitika m'thupi, monga momwe anacita, kapena cabwino kapena coipa."*

**– 2 Akorinto 5:10**

# **KODI MPANDO WAKUWERUZA WA KHRISTU NDI CHIYANI?**

**Munthu wina aliyense amene wakhalapo ndi moyo adzaweruzidwa ndi mulungu.**

Otaika adzaweruzidwa, ndipo adzapezedwa olakwa pa mpando woyera waukuru wa chiweruzo, pamene opulumuka adzaweruzidwa pa mpando wakuweruza wa Khristu. .

*“Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa, ciweruzo.”  
– **Ahebri 9:27***

*“Ambiri afunafuna ciyanjano ca mkuru; koma chiweruzo ca munthu cicokera kwa Yehova.” – **Miyamba 29:26***

**RR. Okhulupirira wina aliyense tsiku lina adzaonetsedwa pamaso pa Ambuye Yesu Khristu.**

Mulungu akukhumba inu kuti mukhale opanda chilema pamaso pake pamene inu mudzaonetsedwa kwa lye.

*“Ndipo inu, okhala alendo kale ndi adani m'cifuwa canu m'nchito zoipazo, koma tsopano anakuyanjanitsani m'thupi lace mwa imfayo, kukaimika inu oyera, ndi opanda cirema ndi osatsutsika pamaso pace;” – **Akolose 1:21-22***

*“Ndipo Mulungu wa mtendere yekha ayeretse inu konsekonse; ndipo mzimu wanu ndi moyo wanu ndi thupi lanu zisungidwe zamphumphu, zopanda cirema pa kudza kwace kwa: Ambuye wathu Yesu Kristu.” – **1 Atesalonika 5:23***

**SS. Okhulupirira onse adzayankha za m'mene anachitira pa utumiki wawo wachikhristu Akhristu pa mpando wakuweruza wa Khristu.**

*“Koma iwe uweruziranji mbale wako? Kapena iwenso upeputsiranji mbale wako? Pakuti ife tonse tidzaimirira ku mpando wakuweruza wa Mulungu. Pakuti kwalembedwa, Pali moyo wanga, ari Ambuye, mabondo onse adzagwadira Ine, Ndipo malilime onse adzabvomereza Mulungu, Coteru munthu ali yense wa ife adzadziwerengera mlandu wace kwa Mulungu.” – **Aroma 14:10-12***

### **Chiweruzo cha machimo anu chinachitika pa mtanda wa Kavale.**

Poika chikhulupiro chanu mwa Yesu Khristu monga mpulumutsi, machimo anu analipilidwa, ndipo inu simuyenera kuopa chiweruzo cha machimo anu.

*“Ameneyo sanadziwa ucimo anamyesea ucimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale cilungamo ca Mulungu mwa iye.” – 2 Akorinto 5:21*

*“Amene anasenza macimo athu mwini yekha m'thupi mwace pamtanda, kuti ife, titafa kumacimo, tikakhale ndi moyo kutsata cilungamo; ameneyo mikwingwirima yace munaciritsidwa nayo.” – 1 Petro 2:24*

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu mwakonzeka kuonetsedwa pamaso pa Ambuye Yesu Khristu?

## **KODI MUDZAWERUZIDWA PA CHIYANI PA MPANDO WOWERUZA WA KHRISTU?**

### **MFUNDO YOFUNIKIRA YA PHUNZIRO!**

Yesu Khristu akuyembekezera inu kuti mumulemekeze ndi moyo wanu, choncho inu mudzaweruzidwa chifukwa cha ntchito zimene munachita monga mtumiki wa Ambuye Yesu Khristu pambuto pa kupulumutsidwa.

*“Pakuti ife ndife cipango cace, olengedwa mwa Kristu Yesu, kucita nchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo.” – Aefeso 2:10*

### **F. Inu mudzaweruzidwa pa m'mene munamangira pa maziko a chipulumutso chanu mwa Yesu Khristu.**

Baibulo limagwiritsa ntchito golide, siliva, and miyala ya mtengo wapatali pokamba za ntchito zokhala ndi phindu la muyaya; pamene mitengo, maudzu, ndi dzuputu pokamba za ntchito zosakhala ndi phindu lamuyaya.

**1 Akorinto 3:10**

## G. Inu mudzaweruzidwa molingana ndi kukongola kwa ntchito yanu, osati kuchuruka kwake.

Mulungu sadzaweruzidwa kuchuruka kwa ntchito imene inu mumachita, koma mtundu wa ntchito imene inu mumamutumikira nayo. Iye amakhudzika kwambiri ndi chiyero cha mu mtima mwanu kusiyana ndi kuchuluka ndi ntchito zimene mumamugwirira iye. Chikondi chanu pa Yesu Khristu chidzabweretsa mtundu wa ntchito zabwino.

**1 Akorinto 3:13**

### **MFUNDO YOFUNIKIRA KUDZIWA:**

Nthawi zonse muyenera kuchita chimene chiri cholondora ngakhale mwina simukumva kutero. Musalore kuti zimene mumaona kuti ndi zinthu zolakwikwa monga mtima wanu uonera kukuletsani kuchita ntchito yabwino ya Ambuye. Inu muyenera kutumikira Ambuye ndi mtima odzichepetsa, osalora maimvaimva kukulepheretsani kutumikira.

*“Pereka zocita zako kwa Yehova, Ndipo zolingalira zako zidzakhazikika.” – Miyambo 16:3*

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu mukhonza kufotokoza bwanji kukongola kwa utumiki wanu pa Ambuye?

Kodi Mulungu akulemekezedwa bwanji ndi moyo wanu?

## **KODI INU MUDZAKHUDZIDWA BWANJI PA MPANDO WAKUWERUZA WA KHRISTU?**

Pamene ntchito yanu iyeseledwa ndi moto, ntchito yanu ya muyaya idzakhale koma ntchito yanu yakuthupi idzaonongedwa..

*“Ntchito ya yense idzaonetsedwa; pakuti tsikulo lidzaisonyeza, cifukwa kuti yabvumbuluka m'moto; ndipo mota wokha udzayesera nchito ya yense ikhala yotani. Ngati nchito ya munthu ali yense khala imene anaimangako, adzaandira mphotho. Ngati nchito ya wina itenthedwa, zidzaonongeka zace; koma iye yekha adzapulumutsilwa; koma monga momwe mwa moto.” – 1 Akorinto 3:13-15*

### **A. Pali zotsatira zovuta pa mpando wa chiweruzo.**

1. Akhristu ena adzapezeka kuti ali aperewera chifukwa ntchito zawo zinakhazikika pa zinthu za pansu pano osati za muyaya. Ntchito zawo zinali ndi zinthu zosiyanasiyana (mtengo, udzu ndi ziputu).

**1 Akorinto 3:15**

2. Akhristu ena adzachita manyazi pamaso pa Mulungu chifukwa cholephera kukhala ndi moyo woyenera ndi Ambuye Yesu Khristu pamene adzabweranso.



### **1 Yohane 2:28**

3. Akhristu ena adzaima pamaso pa Ambuye ndi umaliseche wawo chifukwa sanathe kutumukira Ambuye mokhulupirika m'moyo wawo.

### **2 Akorinto 5:2-3; 2 Yohane 8**

#### **MFUNDO YOFUNIKIRA KUDZIWA:**

Inu muyenera kuzindikira kuti maonekedwe ndi zoganzira zikhonza kukhala zinthu zonyenga, ngakhale m'moyo wanu. Inu muli ndi kuthekera koononga moyo wanu ndi zochitika za chipembedzo, komanso mwina osachita kanthu kabwino pa Ambuye. Mulungu amadziwa mitima yathu.

*“Musanyengedwe; Mulungu sanyozeka; pakuti cimene munthu acifesa, cimenenso adzaciduta. Pakuti wakufesera kwa thupi la iye yekha, cocokera m'thupi adzatuta cibvundi; koma wakufesera kwa Mzimu, cocokera mu Mzimu adzatuta moyo wosatha.” – Agalatiya 6:7-8*

1. Tsimikizikani kuti utumiki wanu uli pa Ambuye, osati ku zilakolako za kuthupi.

***Luka 16:15***

2. Tsimikizikani kuti inu mukuikiza pa zinthu zakumwamba osati pa kulandira mphoto zapadziko.

***Mateyu 6:19-20***

#### **B. Pali mphoto zimene zilipo kwa okhulupirira a Chipangano Chatsopano pa mpando wakuweruza wa Khristu.**

Okhulupirira onse adzalandira mphoto ya cholowa cha matupi a ulemelero mukupezeka kwa Mulungu kwa muyaya.

***Akolose 3:23-25; Afilipi 3:20-21***

Mulungu analonjeza kuti onse amene azunzika chifukwa cha iye m'moyo uno adzalamuliranso pamodzi ndi iye.

***Aroma 8:16-19; 2 Timoteo 2:11-12***

#### **1. Korona wa chilungamo**

Korona uyu adzaperekedwa kwa iwo amene anakonda maonekedwe a Yesu Khristu. Zokhumba zanu zenizeni zikhale pa kufuna kukhala ndi Ambuye nthawi zonse.

*“Ndalimbana nako kulimbana kwabwino, ndatsiriza njirayo, ndasunga cikhulupiro: cotsalira wandiikira ine korona wa cilungamo, amene Ambuye, woweruza wolungama, adzandipatsa ine tsiku lijalo: ndipo si kwa ine ndekha, komatunso kwa onse amene anakonda maonekedwe ace.”—2 Timoteo 4:7-8*

## 2. Korona wa Moyo

Korona uyu adzaperekedwa kwa onse amene anakonda Khristu. Chikondi chawo chimawapangitsa kutaya moyo wawo pamene akulimbana ndi mayesero komanso kukumana ndi mazunzo.

*“Usaope zimene uti udzamve kuwawa; taona, mdierekezi adzaponya ena ainu m'nyumba yandende, kuti mukayesedwe; ndipo mudzakhala naco cisautso masiku khumi. Khala wokholupirika kufikira imfa, ndipo ndidzakupatsa iwe korona wa moyo.”— Chivumbulutso 2:10*

*“Wodala munthu wakupirira poyesedwa; pakuti pamene wabvomerezeka, adzalandira korona wa moyo, amene Ambuye adalonjezera iwo akumkonda iye.”— Yakobo 1:12*

## 3. Korona Wosavunda

Korona uyu adzaperekedwa kwa iwo amene sanagwe pa chikhulupiro chao, ndipo iwo akhalabe ndi ali kuchitira umboni wa Yesu Khristu kwa ena pokhala ofatsa ndi odekha mu moyo wawo wa kuthupi, uzimu ndi zoganiza zina.

*“Koma yense wakuyesetsana adzikaniza zonse. Ndipo iwowa atero kuti alandire korona wakubvunda; koma ife wosavvunda. Cifukwa cace ine ndithamanga coteru, si nonga cosinkhasinkha. Ndilimbaaa coteru, si monga ngati kupanda nlengalenga; koma ndipumpuatha thupi langa, ndipo ndiliyesa capolo; kuti, kapena ngakhale rdalalikira kwa ena, ndingakhale votayika ndekha.”— 1 Akorinto 9:25*

## 4. Korona wa Chimwemwe

Korona uyu adzaperekedwa kwa onse amene anatsogolera anthu kwa Yesu Khristu. Kuli chimwemwe kumwamba pamene m'modzi apulumuka.

*“Pakuti ciyembekezo cathu, kapena cimwemwe, kapena korona wakudzitamandira naye nciani? Si ndinu nanga pamaso pa Ambuye wathu Yesu m'kufika kwace?”— 1 Atesalonika 2:19*

## 5. Korona wa Ulemerero

Korona uyu adzaperekedwa kwa onse amene aweta kapena kukhala m'busa wa anthu pa mau a Mulungu. Okhulupirira wina aliyense ayenera kukhala ndi kuchilimika poikiza mau a Mulungu mwa anthu ena.

*“Wetani gulu la Mulungu liri mwa inu, ndi kuliyang'anira, osati mokangamiza, koma mwaufulu, kwa Mulungu; osatsata phindu lonyansa, koma mwacangu; osati monga ocita ufumu pa iwo a udindo wanu, koma okhala zitsanzo za gululo. Ndipo pakuonekera Mbusa wamkulu, mudzalandira korona wa ulemerero, wosafota.”— 1 Peter 5:2-4*

## **MPHOTO INA IRIYONSE IMENE MUNGALANDIRE NDI YAKE YA MULUNGU.**

Ntchito ina iriyonse imene inu mwachita imene iri ndi colowa cha muyaya inakwaniritsidwa ndi Yeus Khristu kudzera mwa inu. Iye yekha ndiye wamkuru ndipo ayenera kulandira ulemelero.

*“Pokhulupira pamenepo, kuti iye amene anayamba mwa inu nchito yabwino, adzaitiriza kufikira tsiku la Yesu Kristu;” – Afilipi 1:6*

*“Potero, okonedwa anga, monga momwe mumvera nthawi zonse, posati pokha pokha pokhala ine ndiripo, komatu makamaka tsopano pokhala ine palibe, gwirani nchito yace ya cipulumutso canu ndi mantha, ndi kunthunthumira; pakuti wakucita mwa inu kufuna ndi kucita komwe, cifukwa ca kukoma mtima kwace, ndiye Mulungu,” – Afilipi 2:13*

Pali chitsanzo chimene chapelekedwa kwa inu mu bukhu la Chibvumbulutso pamene akuru makumi awiri ndi anai amaponya pansu korona wao pa mpando wa Mulungu ndikupereka ulemelero. Inunso bwanji mukhale ndimtima omweo, ndi kupereka ulemelero kwa Ambuye Yesu Khristu pa zimene iye anachita pamoyo wanu.

*“Akulu makumi awiri mphambu anai amagwa pansu pamaso pa iye wakukhala pa mpando wacifumu, namlambira iye amene akhala ndi moyo kufikira nthawi za nthawi, ndipo aponya pansu akorona ao ku mpando wacifumu, ndi kunena, Muyenera inu, Ambuye wathu, ndi Mulungu wathu, kulandira ulemelero ndi ulemu ndi mphamvu; cifukwa mudalenga zonse, ndipo mwa cifuniro canu zinakhala, nizinalengedwa..” – Chivumbulutso 4:10-11*

### **ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu mukhonza kuyembekezera zotani kwa inu pamene mufika pa mpando wakuweruza wa Khristu?

Kodi choonadi chokhudza mpando woweruza wa Khristu chamakhudza bwanji za m'mene inu mumaonera moyo wanu?

## **KODI INU MUNGAKONZEKERE BWANJI ZA MPANDO WAKUWERUZA WAKHRISTU?**

**A. Khazikitsani moyo wanu pa zinthu zimene zikukhudza moyo wamuyaya.**

Kumbukirani, baibulo limagwiritsa ntchito golide, siliva, and ndi miyala ya mtengo wapatali pokamba za ntchito zimene ziri ndi phindu la muyaya; mtengo, maudzu ndi dziputu zimaimira zinthu zimene siziri ndi phindu la muyaya.

*“Koma ngati wina amanga pa mazikowo, golidi, siliva, miyala ya mtengo wace, mtengo, maudzu, dziputu, nchito ya yense idzaonetsedwa ...” – 1 Akorinto 3:12-13*

**1. Golide akuimira cha umulungu.**

Pamene tilambira, kutumikra, ndi kukweza Khristu monga Mulungu, mumasunga golide kumwamba.

***Eksodo 39:30***

**2. Siliva amaimira chiombolo.**

Pamene muudza munthu wina za mtengo umene Yesu analipira chifukwa cha iwo, mumasunga siliva kumwamba.

***Zekariya 11:10-12***

**3. Miyala ya mtengo wapatali imaimira miyoyo ya amuna ndi akazi.**

Pamene mumutsogolera wina kwa Khristu, musunga miyala ya mtengo wapatali kumwamba.

***1 Petro 2:4-5***

**B. Yang'anitsitsani pa kukondweretsa Ambuye ndi moyo wanu tsopano.**

Ngati Mulungu ali osangalala ndi moyo wanu tsopano, iyenso adzasangalala nanu pampando wakuweruza wa Khristu.

*“Koma tilimbika mtima, ndipo tikondwera makamaka kusakhala m'thupi, ndi kukhala kwathu kwa Ambuye. Cifukwa cacenso tifunitsitsa, kapena kwathu kapena kwina, kukhala akumkondweretsa iye.” – 2 Akorinto 5:8-9*

**C. Khazikikani pa kudziwa kuti mudzayankha pa mmene munachitira ndi moyo wanu.**

Khalani moyo wanu mu njira imene imukondweretsa Mulungu, podziwa kuti tsiku lina mudzakhira pa m'mene inu munatumikira lye.

*“Pakuti ife tonse tiyenera kuonetsedwa ku mpando wa kuweruza wa Kristu, kuti yense alandire zocitika m'thupi, monga momwe anacita, kapena cabwino kapena coipa. Podziwa tsono kuopsa kwa Ambuye, tikopa anthu, koma tionetsedwa kwa Mulungu; ndipo ndiyembekezanso kuti tionetsedwa m'zikumbu mtimazanu.” – 2 Akorinto 5:10-11*

**D. Khazikikani pa kubweranso kwa Yesu Khristu.**

Kukhazikika pa kubweranso kwa Ambuye Yesu Khristu ndi chimodzi mwa ziphunzitso za Baibulo zimene zimakhuzza kukhala kwathu kwa tsiku ndi tsiku. Pamene mukhazikika pa kuona Yesu maso ndi maso, mumakura mu chikhalidwe china chake mkati mwanu.

5. Zimabweretsa KULEZA MTIMA mu mtima mwanu.

***Yakobo 5:7-8***

6. Zimabweretsa CHIMWEMWE pakutsogolera anthu ena mu chikhulupiriro mwa Khristu.

***1 Atesalonika 2:19***

7. Zimabweretsa CHIYERO mkati mwanu.

***1 Atesalonika 3:13***

8. Zimabweretsa CHITONTHOZO mkati mwa chisoni.

***1 Atesalonika 4:16-18***

9. Zimabweretsa KUTSIMIKIZIKA MTIMA kuti Mulungu sanathane nanu.

***Afilipi 1:6***

10. Zimabweretsa KULIMBIKA potumikira Ambuye mpaka kumapeto.

***1 Timoteo 4:1-8***

11. Zimabweretsa makhalidwe a CHILUNGAMO mu dziko lino.

***Tito 2:11-14***

12. Zimabweretsa CHIKHULUPIRIRO ngakhale mu nyengo zovuta.

***1 Petro 1:5-7***

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi mukukhala moyo wanu pa zinthu zimene zingapereke phindu la muyaya?

Kodi pali gawo lina m'moyo mwanu limene lasochera ndipo likufunikanso kukonzanso?

Kodi inu muli ndi chikhalidwe china chirichonse chimene chimaonetsa kuti munakhazikika pa kubweranso kwa Yesu Khristu?

## **KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA**

**61. Molingana ndi *1 Akorinto 3:11-15*, kodi ife tidzaweruzidwa pa chiyani pa mpando wa kuweruza wa Khristu?**

---

---

---

**62.Kodi ife sitidzaweruzidwa chifukwa cha machimo athu chifukwa chiyani?**

---

---

---

**63.Kodi ndi makorona asanu ati amene adzaperekedwe? Fotokozani mwachidule ndipo muonetsenso ndime za m'malemba pa mfundo iriyonse.**

- a. 

---

---
- b. 

---

---
- c. 

---

---
- d. 

---

---
- e. 

---

---

**64.Chifukwa chiyani tiyenera kukhazikika pa za mpando wa kuweruza wa Khristu?**

---

---

---

**65.Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo lakuphunzitsani chiyani?**

---

---

---

---

---

---

## **KUPHUNZIRA BAIBULO PAWEKHA**

**Fotokozani mwa mau momwe 2 Akorinto 4:16-18 akugwirizanira ndi mpando wakuweruza wa Khristu.**

---

---

---

---

**Werengani Akolose 1:21-23. Molingana ndi ndime imeneyi, Mulungu akufuna kuti ana ake aonetsedwe opanda chilema. Kodi ndi chenjezo lanji limene likuperekedwa mu ndime imeneyi limene likhonza kumupanga munthu kuti asaonetsedwe wokhala ndi chilema?**

---

---

---

---

**Werengani Akolose 3:1-4. Kodi ndime imeneyi ikukamba chiyani za kumene muyenera kulingalirako? Molingana ndi ndime imeneyi, moyo wanu wabisika mwa Yesu Khristu. Kodi Yesu alikuti pakadali pano? Kodi ndime imeneyi ikulonjeza chiyani za kubweranso kwake?**

---

---

---

---

---

---

**Werengani 2 Timoteo 4:6-7. Mtumwi Paulo anali okonzeka kuonetsedwa pamaso pa Ambuye chifukwa anali otsimikizika kuti watsiriza zonse zimene anayenera kumuchitira Ambuye. Kodi inu muli okonzeka kuonetsedwa pamaso pa Ambuye? Kodi ndi zinthu ziti zimene mungachite kwa Ambuye kuti mutsirize mwa mphamvu pa Iye?**

---

---

---

---

---

---

## **18. NDONDOMEKO ZOTSATIRA**

*Cholinga cha maphunziro opanga ophunzira monga mwa baibulo ndiko kuberekanso ana auzimu a Mulungu. Tsopano, chifukwa mwaphunzira za ziphunzitso zofunika zimene ziri m' mau a Mulungu, ndi nthawi tsopano yoti tikwaniritse za lamulo la Mulungu loti tiberekenso mwa ena chimene chaberekedwa mwa inu.*

**Mau ofunikira mu phunziro iri ndi:**

*KUBEREKANSO*

**Mafunso ofunikira limene liyankhidwe pa phunziro iri ndiri:**

*Kodi ndi udindo wanga kupanga ophunzira?*

**Cholinga chenicheni cha phunziro iri:**

*Kukhazikitsa mwa inu za lamulo la kupanga ophunzira*

**Mfundo yofunikira mu phunziro iri:**

*Inu muli ndi udindo woberekanso za ubale wanu ndi Yesu mwa okhulupirira wina.*

**NDIME ZA PAMTIMA:**

*“Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitisa enanso.” – 2 Timoteo 2:2*

*“Ine ndalemekeza Inu pa dziko lapansi, m'mene ndinatsiriza nchito imene munandipatsa ndicite.” – Yohane 17:4*



# KUMVETSETSA UDINDO WANU

---

## C. Inu mwapatsidwa udindo wotsogolera otaika ku chipulumutso.

Inu mwapatsidwa utumiki wa chiyanjanitso monga akazembe a Mulungu mu dziko lino. Muli ndi udindo wofunafuna anthu otaika kuti akayanjanitsidwe ndi Mulungu kudzera mu uthenga wabwino wa Yesu Khristu.

**2 Akorinto 5:18-20; Luka 19:10**

## D. Inu mwapatsidwa udindo wokwaniritsa Lamulo Lalikuru.

**Mateyu 28:18-20**

1. Kukwaniritsa Lamulo Lalikuru zimafuna munthu afikiridwe ndi uthenga.

**1. Akorinto 9:16**

2. Kukwaniritsa Lamulo Lalikuru zimafuna munthu apange ophunzira.

**1 Akorinto 11:1**

## C. Inu mwapatsidwa udindo kuti muchuruke mu kuchita ntchito ya Ambuye.

**1 Akorinto 15:58**

### MFUNDO YOFUNIKIRA MU PHUNZIRO IRI!

Mulungu analamulira okhulupirira wina aliyense kugawa uthenga kwa anthu otaika komanso kuphunzitsa opulumutsidwa. Inu muli ndi udindo woberekanso ubale wanu ndi Yesu mwa okhulupirira ena. Yesu anatipatsa ife chitsanzo cha m'mene tikhonza kulemekezera Ambuye pomaliza ntchito yopanga ophunzira.

*“Ine ndalemekeza Inu pa dziko lapansi, m'mene ndinatsiriza nchito imene munandipatsa ndicite.”— Yohane 17:4*

1. Yesu ANALALIKIRA popanga dzina la Mulungu ndi chikhalidwe chake kuti zidziwike kwa anthu otaika

**Yohane 17:6**

2. Yesu ANAPANGA OPHUNZIRA makamaka iwo okhulupirira powaphunzitsa kuti adziwe komanso achite mau a Mulungu.

**Yohane 17:8**

3. Yesu ANAZIBEREKANSO Iye yekha pophunzitsa okhulupirira ndi kuwatumiza kunja kuti achite zomwezo ndi anthu ena.

**Yohane 17:18**

# **KUMVETSETSA M'MENE TINGAPANGIRE OPHUNZIRA**

Kupanga ophunzira monga mwa baibulo ndi mwambo umene umatenga nthawi ya moyo wathu wonse wakukhala womvera ndi kuchita mau a Mulungu, ndi cholinga chakuti okhulupirira akhonze kufanana ndi chikhalidwe cha Yesu Khristu.

## **A. Kumvetsetsa zimene mukuphunzitsa.**

### **1. Inu mukuyenera kuphunzitsa wophunzirayo za Yesu.**

Inu mukupanga ophunzira wa Yesu, choncho ndi chinthu chofunikira kuphunzitsa ophunzira wanu kuti asunge zinthu zonse zimene Yesu anaphunzitsa komanso kuti amutsate lye.

*Ahebri s 12:2-3; Mateyu 11:29-30*

### **2. Inu mukuyenera kuphunzitsa wophunzirayo chiphunzitso choona.**

Njira yokhayo imene yophunzitsira chiphunzitso choona ndi kuphunzitsa mau a Mulungu molunjika bwino. Khalani amachawi kuphunzitsa mau a Mulungu osati maganizo ndi zikhalidwe zanu.

*Tito 2:1; 2 Timoteo 1:13; 2 Timoteo 3:16*

## **B. Kumvetsetsa kuti Kupanga ophunzira si pulogalamu, koma ndi maganizidwe a m'mene tingapangire utumiki.**

Ma pulogalamu a mpingo amabwera komanso kupita, pamene utumiki wa baibulo umatulutsa zipatso zimene zimakhalitsa. Kupanga ophunzira si monga maphunziro a baibulo chabe, koma ndi njira ya kuphunzitsa okhulupirira kuti atsate Khristu. Maphunziro amenewa ali ngati chida chothandizira kuti inu muphunzire mau a Mulungu.

*Yohane 15:16*

## **C. Kumvetsetsa kuti Kupanga ophunzira si kungopereka chidziwitso, komanso ndi kupereka zinthu moonetsa kukura kwa moyo wauzimu.**

Chionetsero chakukura muuzimu ndi kuchita choonadi cha baibulo. Okhulupirira amene sanakule amakonda kunyada chifukwa cha zimene amadziwa mu baibulo komabe samadziwa kwenikweni za m'mene akhonza kutsatira Ambuye ndi miyoyo yawo. Kudzera mu zitsanzo zochitika, inu muyenera kugawa mmene choonadi cha baibulo chimene mukuphunzitsa kwa ophunzira anu chikugwirira ntchito moyo wanu.

*1 Akorinto 8:1; 1 Atesalonika 4:1*

## **D. Kumvetsetsa kuti Kupanga Ophunzira kumafunikira kudzipereka kwathunthu kuti mugawane moyo wanu ndi wophunzira wanu.**

Inu mukuyenera kutenga udindo wa kholo limene mwachikondi limepereka china chirichonse chimene chiri chofunikira kuti ophunzira akule. Izi zikutanthauza kuti inu muyenera kukhala omasuka ndi oona mtima pakuyenda kwanu ndi Mulungu kuti mukhonze kuphunzitsa ophunzirayo bwino. Muyenera kupereka moyo wanu. Ophunzira anu

akuyenera kudziwa kuti inu ndinu munthu osamala, ndipo inu mulipo kuti muwathandize kuti akure.

**1 Atesalonika 2:1-10**

**MFUNDO ZA KUZIPEREKA PA KUPANGA OPHUNZIRA**

1. Kupanga ophunzira kumafuna kuti inu mupange chisankho.

*“ngati munthu afuna...” – Luka 9:23*

2. Kupanga ophunzira kumafuna kuchita chimene Yesu anachita.

*“...kudza pambuyo panga...” – Luka 9:23*

3. Kupanga ophunzira kumafuna inu kuti mukhale nsembe yamoyo.

*“...adzikanize yekha...” – Luka 9:23*

4. Kupanga ophunzira kumafuna kudzipereka kwanu ku zinthu zamuyaya.

*“...nanyamule mtanda wake tsiku ndi tsiku...” – Luka 9:23*

5. Kupanga ophunzira kumafuna inu kuti mumutsatire Yesu masiku onse a moyo wanu.

*“...nanditsate ine.” – Luka 9:23*

## **KUMVETSETSA ZA ZOLINGA ZOPANGIRA OPHUNZIRA**

**A. Kukhazikika mu Kulambira:** *Choyang’anira cha moyo wanu*

Pamene mwayamba kumudziwa Yesu monga Mpulumutsi ndi Mbuye, muyenera kuyamba moyo wa chikhulupiriro ndi malingaliro akuona zinthu monga zamuyaya. Mukhonza kuyamba kukhumba kulemekeza ndi kutamanda Mulungu potsata Khristu pa moyo wani ndi kudzipereka konse.

**B. Kukhazikika m’mau a Mulungu:** *Ulamuliro wa moyo wanu*

Kudziwa kwanu kuti Mulungu ndi ndani kuyenera kukutsogolerani kuti muwerenge mau ake. Ndi chinthu chofunikira kuti mudzipereke ndi kukhala mogwirizana ndi choonadi cha baibulo pamene mukuliwerenga, kuzindikira chimene Mulungu akunena kwa inu.

**C. Kukhazikika mu Mpingo Wapamalo:** *Malo amene muyenera kukulira*

Cholinga cha Mulungu pa moyo wanu chimapezeka m’mau a Mulungu, ndipo muyenera kuchikwaniritsa kudzera mu mpingo wanu wapamalo. Inu muli ndi udindo wapaderadera

umene Mulungu anakupatsani mu mpingo mwanu umene mukhonze kuuonetsa kudzera mu nthawi, kuthekera, komanso pa zinthu zimene Mulungu wakupatsani.

**D. Kukhazikika mu Utumiki: *Cholinga cha moyo wanu***

Ndi chinthu chofunikira kukhala m'moyo wofuna kukwaniritsa za chifuniro cha Mulungu. Chifuniro cha Mulungu pa moyo wanu ndiko KUKHALA OPHUNZIRA (khalani woyera, odzala ndi Mzimu Woyera osati tchimo) ndi KUPANGA OPHUNZIRA (kugawana uthenga wabwino, ndi kudzipereka ku zinthu izi kwa anthu okhulupirika).

## **KUMVETSETSA ZA CHIMENE TIYENERA KUYANG'ANA** **POPANGA OPHUNZIRA**

*“Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso.” – 2 Timoteo 2:2*

**A. Khazikikani pa kupanga chiphunzitso kukhala choyambirira.**

Ubale pakati pa ophunzira ndi ophunzitsa umaonetsa ngati kupanga ophunzira kukuchitika kapena ayi; komabe, cholinga chenicheni chopangira ophunzira ndi kukonzekeretsa okhulupirira ndi chiphunzitso choona cha baibulo. Nthawi zonse chiphunzitso cha baibulo chimalunjika pa kutsatira Yesu.

*“Ndipo zimene...” – 2 Timoteo 2:2*

**B. Khazikikani pa kupanga ubale wabwino pakati pa mphumzitsi ndi ophunzira.**

Pakuyenera kukhala ophunzira kuti kupanga ophunzirako kutheke. Izi zimayenera kuchitika kwa m'modzi m'modzi; komabe ndi zinthu zofunikira kukwaniritsa kupanga ophunzira ndi anthu awiri kapena atatu, bola ngati pali mphumzitsi m'modzi, ndipo ena onse ndi ophunzira. Kupanga ophunzira simaphnziro chabe a baibulo, kapena anthu awiri kungokhala ndi nthawi limodzi. Izi zimakhazikika pa waphunzitsa kukhutula moyo wake ndi mau a Mulungu kwa ophunzira.

*“...wazimva kwa ine...” – 2 Timoteo 2:2*

**C. Khazikikani pa kukhala woyankhira kwa ena**

Kupanga ophunzira kumafuna ubale wabwino ndithu pakati pa ophunzira ndi ophunzitsa. Komabe, kupanga ophunzira kumeneku sikuyenera kuchitika pakokha. Pakuyenera kukhala kudziwa kuti tiyenera kukamba za m'mene tachitira ndipo anthu ena akhonza kukhala mboni ya izi komanso kuona za zolinga zimene zakwaniritsidwa.

*“...mwa mboni zambiri...” – 2 Timoteo 2:2*

**D. Khazikikani pa kuphunzitsa mu njira yoti mukhonza kubwereza.**

Perekani choonadi cha baibulo mu njira yosavuta ndi yomveka bwino, ndipo mu njira imeneyo zidzakhala zophweka kwa wophunzira wanu kubwereza ndi kuphunzitsa kwa ophunzira ake.

*“...zomwezi uikize...” – 2Timoteo 2:2*

### **E. Khazikikani pa kuphunzitsa ophunzira okhulupirika**

Kupanga ophunzira kumamangiririka pa ophunzira m’modzi amene akhala pa ubale ndi okhulupirira wina amene iyenso ali okhulupirira. Pakuyenera kukhala nthawi yakuona kukhulupirika kwa munthu, ndipo kupanga ophunzira sikungakhale koyenera kwa okhulupirira watsopano.

*“...mwa anthu okhulupirika...” – 2 Timoteo 2:2*

### **F. Khazikikani popanga ophunzira amene akhonza kupanga ophunzira ena.**

Chifukwa chimene timaperekera “zinthu zimenezi” kwa ophunzira okhulupirira, ndi chakuti iwonso aphunzitse anthu ena. Cholinga chanu chenicheni ndi kupanga ophunzira amene adzapanga ophunzira ambiri.

*“...amene adzadziwa kuphunzitsa enanso.” – 2 Timoteo 2:2*

## **ENA MWA MAFUNSO AMENE MUKHONZA KUFUNSA**

### **A. Kodi Mulungu akhonza kundigwiritsa ine ntchito kupanga ophunzira ngakhale kuti sindine m’busa kapena mtsogoleri mu mpingo?**

Inde. Mulungu wapanga inu monga mtumiki amene akhonza kutumikira chifukwa muli ndi Mzimu Woyera amene akhala mkati mwanu. Mulungu amalemekezedwa kudzera mu zifooko zanu.

*2 Akorinto 3:5-6; 2 Akorinto 12:9-10*

### **B. Kodi ine ndichite chiyani ngati wophunzira wanga wasankha kusiya maphunziro tisanatsirize kuphunzira?**

Ndi chinthu chofunikira kukumbukira kuti pamene mugwira ntchito ya Ambuye, simuchita kwachabe. Nthawi zina, ophunzira amakhonza kusiira panjira. Yesu anali mphunzitsi wabwino ndithu, koma anali ndi ophunzira amene anasiya komanso kumthawa.

*1 Akorinto 15:58; Yohane 6:66; Miyambo 20:6*

### **C. Kodi ine ndingalumikizane bwanji ndi munthu amene ndikhonza kumupanga kukhala wophunzira?**

Pezani ndithu nthawi yoti mudzipereke kuti mukonzekere kupanga ophunzira. Komanso muyenera kukhulupirira utsogoleri wa mpingo wapamalo kuti ukupatsen munthu woti akhale wophunzira.

Yambani ndi kupemphera kwa Mulungu kuti akupatseni wophunzira. Njira yabwino yopezera ndi kumubweretsa munthu kwa Khristu ndi kuyamba kupereka moyo wanu kwa iye.

**MFUNDO YOTSIRIZA YOTI MUDZIWE:**

Kupanga ophunzira ndi ntchito yovuta, koma ndi ntchito imene idzapindula ku umuyaya. Ngati simuli osamala, zinthu za padziko pano zidzakhala mayesero okhazikika amene adzakulepheretsani kuti mupirire popanga ophunzira. Satana nayenso adzayesetsa kukulepheretsani kuti musakwaniritse Lamulo Lalikuru pa moyo wanu.

*2 Timoteo 2:2-4; 1 Petro 5:8*

**ZOKAMBIRANA:**

Kodi inu mukukwanitsa motani Lamulo Lalikuru mu moyo wanu tsopano?

Kodi mwakhala mukuona maphunzira amenewa monga kuphunzira za baibulo, kapena kukonzekeretsedwa kupanga ophunzira kudzera pa moyo wanu?

## KAUNIUNI NDI ZOKAMBIRANA

**66.Kodi ndi zinthu ziwiri ziti zofunika pokwaniritsa Lamulo Lalikuru?**

o. \_\_\_\_\_

p. \_\_\_\_\_

**67.Molingana ndi 2 Timoteo 2:2, kodi ndi zinthu zisanu ndi chimodzi ziti zimene inu muyenera kukhazikika pamene mukumana ndi ophunzira wanu?**

a. \_\_\_\_\_

b. \_\_\_\_\_

c. \_\_\_\_\_

d. \_\_\_\_\_

e. \_\_\_\_\_

f. \_\_\_\_\_

**68.Kodi zolinga zinai zopangira ophunzira ndi ziti? Kodi mukhonza kunena kuti mukuchita chiyani pofuna kwaniritsa pa zolinga izi m'moyo mwanu?**

f. \_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

- g. \_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_
- h. \_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_
- i. \_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_

**69. Kodi cholinga chenicheni cha phunziro iri ndi chiyani, ndipo chakuphunzitsani chiyani?**

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

## **KUPHUNZIRA BAIBULO PAWEKHA**

**Werengani 1 Atesalonika 3:1-3.** Mtumwi Paulo amafuna kuonetsetsa kuti mpingo watsopano wa ku Atesalonika usathe, ndipo anatomiza Timoteyo kumeneko kuti akapange ophunzira. Kodi pali zikhalidwe zotani zapaderadera zimene Paulo akukamba za Timoteyo zimene zikumuyenereza iye kuti apite ndi kukapanga ophunzira ku Atesalonika?

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

**Werengani 1 Atesalonika 4:1.** Kodi Paulo akupempha ndi kudandaulira mpingo waku Atesalonika kuti uchite chiyani pa chiphunzitso chopanga ophunzira chimene anachilandira? Kodi inu mukuganiza kuti ndi udindo wanu kuti muchite chimodzimodzi? Kodi ndi zinthu ziti zimene inu mukumukhulupirira nazo Mulungu kuti akutsogolereni mu zaka zocheza zikubwerazi?

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

